

# *Chikhalidwe Cha Ufumu*

*Wa*

*Mulungu*

## **HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinathandizira anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Otsogolera.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	7
1. Maufumu osaoneka.....	8
2. Mfumu ya Ufumu.....	19
3. Ufumu kalero, lero lino ndi mtsogolo.....	38
4. Zifungulo za Ufumu wa Mulungu.....	57
5. Kuthamangitsidwa mu Ufumu wa Mulungu.....	71
6. Chifaniziro ndi mfundo za Ufumu wa Mulungu.....	84
7. Chikhalidwe cha ufumu wa Mulungu: Gawo loyamba.....	95
8. Chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu: Gawo lachiwiri.....	109
9. Chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu: Gawo lachitatu.....	122
10. Mafanizo a Ufumu.....	130
11. Akazembe a Ufumu wa Mulungu.....	142
Mayankho amafunso odziyesa nokha.....	156

## **KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI**

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Werengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogolera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mawu Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWERENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## **NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU**

### **MKUMANO WOYAMBA**

**Kutsekulira:** Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Ntchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### **MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO**

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphanzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphanzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adziperezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphanzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina ali yense ali ndi buku laphunziroli.

## **PHUNZIRO: UFUMU WA MULUNGU: MAONEKEDWE NDI MFUNDO ZAKE**

### **MAU OTSOGOLERA**

Anthu onse amakhala mu ufumu wa kuthupi wa dziko lapansi. Komanso anthu amakhala mu mizinda ndi m'matauni kapena kumudzi. Madera onsewa ndi gawo limodzi la dziko. Dziko lina lilironse limapanga gawo limodzi la ufumu wa dziko lapansi.

Kuonjezera ufumu wakuthupi wa dziko lapansi, palinso ma ufumu awiri auzimu amene munthu wina aliyense amatha kukhala. Maufumu amenewa ndi ufumu wa Satana ndi Ufumu wa Mulungu.

Koma phunziro ili likamba zokhudza Ufumu wa Mulungu ndipo lifotokozera za ma ufumu awiri auzimu poona amene amalamulira ma ufumu amenewa komanso athu opezeka mu maufumuwa. Chaputala ichi chifotokozeranso za zifunguro zolowera mu Ufumu wa Mulungu ndi kuchenjeza pa zinthu zimene zikhoza kupangitsa munthu kuti aponyendwe kunja kwa Ufumu wa Mulungu. Zinthu zakale, zatsopano komanso zam'tsogolo zokhudza ufumu umenewu zifotokozeledwa. Nao mafanizo okhudza Ufumu, maonekedwe ndi mfundo zokhudza ufumu zatsindikizidwa kwambiri mu chaputala ichi.

Kodi kufunika kophunzira za Ufumu wa Mulungu ndi chiani?

Yesu Khristu anauza ophunzira ake kuti?

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)**

Yesu Khristu asanabwerenso kudzakhazikitsa Ufumu wamuyaya, Uthenga Wabwino uyenera kulalikiidwa dziko lonse lapansi.

Koma kuti tikalalike Uthenga Wabwino wa Ufumu Wamulungu, tiyenera kumvetsa bwino za Ufumu umeneu. Kutu mukhale osunga zifungulo za Ufumu umeneu, muyenera kukumana nao ufumu umeneu.

M'buyomu panali kutsindika kwambiri za moyo ndi utumuki wa mfumu ya Ufumu wa Mulungu, amane ali Yesu Khristu. Sikuti izi ndi zinthu zolakwikwa ayi, koma vuto ndi lakuti palibe kutsindika kwambiri za Uthenga wa ufumuwu. Yesu anauza atsogoleri achipembedzo a nthawi imeneyo kuti:

**Koma tsoka inu, alembi ndi Afarisi, onyenga! cifukwa mutsekera anthu Ufumu wa Kumwamba pamaso pao; pakuti inu nokha simulowamo, Ndipo muwaletsa amene alikulowa, kuti asalowemo. (Mateyu 23:13)**

Cholinga chonse cha moyo wa Khristu Yesu chinakhazikika pa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. Iye anayamba utumiki wake pa dziko lapansi polengeza za kubwera kwa Ufumu wa Mulungu (Mateyu 4:17). Ndipo anamaliza utumiki wake wa dziko lapansi pofotokoza zinthu zokhudza Ufumu wa Mulungu. (Machitidwe 1:3). Pakati pa chiyambi ndimathero autumiki wake wa dziko lapansi, Iye anatsindika kwambiri za Ufumu wa Mulungu.

**Koma anati kwa iwo, Kundienera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi yinanso: cifukwa ndinatamidwa kudzatero. (Luka 4:43)**

Ufumu wa Mulungu chinali chinthu chofunika kwambiri mu utumiki wa Yesu Khristu. Chiphunzitso chake komanso mafanizo ake amatsindika kwambiri za ufumu wa Mulungu. Zozizwa zimene amachita zimangoonetsera mphamvu ya Ufumu wa Mulungu ikugwira ntchito.

Mau akuti “ufumu wa Mulungu” kapena Ufumu wa Kumwamba agwiritsidwa ntchito kokwana makumi asanu mu buku la Mateyu, Marko ndi Yohane. Timauzidwanso kuti tiyambe tathanga Ufumu, kupemphera kuti udze ndikulalikanso za ufumu umeneu. Tikuuzidwanso m'mene tingalowera mu Ufumu umeneu ndipo timaphunzitsidwanso chikhalidwe chatsopano cha Ufumu wa Mulungu.

Kuti tilowe mu Ufumu umeu, kukhazikika ndi kukwanilitsa kulalika za Uthenga Wabwino wa ufumuwu, ndikoyenera kuti timvetse bwino lomwe mfundo zake ndi donsolo la m'mene umayendera. Ichi ndiye cholinga cha phunziro limeneli.

Koma pali cholinga china choposa kumngomvetsetsa mfundo za m'mene Ufumu umayendera. Muyenera kudutsa mlingo ongodziwa za ufumu umeneu ndipo Ufumu uyenera kukhala gawo limodzi lofunika la moyo wanu.

Anthu amafuna kudziwa cholinga cha moyo. Amaunguza cholinga chokhalira moyo angakhale chofera kumene. Inuyo chifukwa chanu chokhalira moyo komanso utumiki wanu chikhale Ufumu wa Mulungu. Uwu ndi Ufumu umene sungagwedezeka ndi mphamvu ina ili yonse ya m'dani kotere kuti Mukhoza kudzipereka moyo wanu onse ku ufumu wa Mulungu.

## **ZOLINGA ZA MAPHUNZIRO AWA**

Pamapeto pamaphunziro awa muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kuzindikira ma Ufumu auzimu osaoneka.
- Kuzindikira olamula ama ufumu osaoneka.
- Kufotokoza malowedwe mu Ufumu wa Mulungu.
- Kufotokoza mwachidule za kale, za lero zamtsogolo zokhudza Ufumu wa Mulungu.
- Kutchula machimo olepheretsa kulowa mu Ufumu wa Mulungu
- Kuzindikira dongosolo ndi mfundo za Ufumu wa Mulungu.
- Kuonetsera kumvetsetsa mfundo zokhudza Ufumu wa Mulungu
- Kuwonetsera kumvetsetsa mafanizo a Ufumu wa Mulungu.
- Kukhala akazembe a Ufumu wa Mulungu pofalitsa Uthenga Wabwino.
- Kupitiriza kuphunzira panokha chiphunzitso ndi utumiki wa Yesu Khristu.

## CHAPUTALA 1

### MA UFUMU OSAONEKA

#### ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yoloweza
- Kuonetsera kumvetsetsa dziko lakuthupi ndi la uzimu.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “Ufumu wa Mulungu”
- Kuzindikira ma ufumu awiri auzimu.
- Kuzindikira olamula a maufumu auzimu.
- Kuzindikira mzika za maufumu auzimu.
- Kufotokozerera tanthauzo la mau oti “Ufumu wa Mulungu.
- Kufotokozerera tanthauzo la mau oti Ufumu wa Satana.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)**

Chaputala ichi chikamba za dziko lakuthupi ndi lauzimu. Dziko lakuthupi limakhudza zinthu zimene Mukhoza kumva, kuona, kugwira kapena kulawa kumene. Ili ndi dziko la zinthu zooneka ndi maso zimene zakuzungulirani.

Komanso pali dziko lina limene lakuzungulirani limene ndi gawo limodzi la moyo wanu. Ili ndi dziko losaoneka limene lili ndi ma Ufumu auzimu awiri. Muchaputala chimenechi muphunzira za maufumu auzimu awiriwa poyang’ana za anthu amene amakhala mu maufumuwa komanso amene amalambulira ma ufumu amenewa. Muphunzira za Ufumu wa Satana komanso Ufumu wa Mulungu.

#### ZAKUTHUPI NDI ZAUZIMU

Munthu amakhala mu magawo awiri amene ali dziko lakuthupi ndi lauzimu. Dziko lakuthupi ndilo limene Mukhoza kumva zinthu, kugwira, kulawa kapena kuti zinthu zake zimaoneka ndi maso. Midzi, dziko kapena m’zinda umene mumakhala ndi gawo limodzi la dziko lakuthupi. Inuyo ndi mzika ya dziko lakuthupi limene limapezeka mu limodzi mwa mayiko adziko lapansi. Mumatha kuwona anthu amene ndi gawo la zonse zopezeka panthaka. Mumatha kulumukizana



nao anthu amenewa. Komanso mumatha kuzindikira zinthu zimene zakuzungulirani monga fungo, phokoso ndi zina zooneka ndi maso.

Koma dziko lina limene mukhala ndilo dziko lauzimu limene Simungathe kuona zinthu ndi maso anu. Koma dziko limeneli ndi dziko lenileni ndithu ngati m'mene likhalira dziko lakuthupi. Paulo akulankhula za kusiyana kwa zinthu zauzimu ndi zakuthupi. Munthu ali ndi gawo lauzimu limene limakhala ndi moyo ndi mzimu wamuyaya. Munthu alinso ndi thupi, moyo ndi mzimu. Mzimu ndi moyo zimapanga gawo lauzimu la munthu pamene thupi la Munthu ndi mbali imodzi ya dziko lakuthupi.

### **MAUFUMU AWIRI AUZIMU**

Pali maufumu a dziko lapansi akuthupi. Ufumu wakuthupi ndi malo kapena anthu amene amalambulidwa ndi mafumu. Baibulo limafotokoza za maufumu adziko lapansi. Pakadali pano, maufumu adziko lapansi ali pansu pa ulamuliro wa Satana.

**Pomwense mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitari, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi, ndi ulemerero wao; nati kwa Iye, Zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansu ndi kundigwadira ine. (Mateyu 4:8-9)**

M'mtsogolo, maufumu onse adziko lapansi adzakhala maufumu a Mulungu. Ndipo Mulungu mwini adzalamulira.

**Ndipo mngelo wacisanu ndi ciwiri anaomba, ndipo panakhala mau akulu m'Mwamba, ndi kunena, Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Kristu wace: ndipo adzacita ufumu kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 11:15)**

Kudziko lakuthupi, mfumu ndi imene imalamulira ufumu. Malo onse ndi anthu okhala mu ufumuwo amakhala ake. Iye amakhala ndi mphamvu ya kuteteza moyo komanso yotha kutenga moyo wa anthu ake mu ufumuwo.

Dziko lauzimu lili ndi ma ufumu awiri auzimu: ufumu wa Satana ndi wa Mulungu. Ufumu wa Satana umapangidwa ndi Satana, dziwanda ndi anthu onse okhala mu uchimo ndikusamvera Mulungu. Pamene Ufumu wa Mulungu umapangidwa ndi Yesu, Mzimu Woyera, zolengedwa zauzimu zotchedwa angelo ndi anthu onse okhala moyo wa ngwiro pomvera Mulungu.

## UFUMU WA MULUNGU

Pali ufumu umodzi wa Mulungu, koma umafotokozeledwa mosiyanasiyana mu Baibulo. Mwachitsanzo mau akuti Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wakumwamba amagwira ntchito mofanana.

Ufumu wa Mulungu ndi chimodzimodzi ndi Ufumu wa Atate(Mateyu26:29), Ufumu wa Yesu (Chibvumbulutso 1:9) (II Timoteyo 4:1), wa Yesu Christu ndi Mulungu (Aefeso 5:5) wa Mbuye wathu ndi Khristu (Chibvumbulutso 11:15 wa Mulugu wathu ndi mphamvu ya Khristu (Chibvumbulutso 12:10), wa Mwana wake okondedwa (Akolose1:13). Mayina onsewa ndi mayina a ufumu wa Mulungu. Koma kuti zinthu zimveke, muphunziro ili tigwiritsa ntchito dzina lakuti “Ufumu wa Mulungu”.

Ufumu wa Mulungu si tchalitchi chifukwa tchalitchi kapena chipembedzo ndi ma bungwe amene amapangidwa ndi anthu. Gulu la mipingo nthawi zambiri limakhazikitsidwa pofuna kuyendetsa zinthu mosavuta. Zitsanzo za magulu a chipembedzo ndi Baptist, Assemblies of God, Methodist ndi matchalitchi ena ambiri.

Baibulo limakamba za mpingo umodzi weniweni owonadi umene si bunge loyambitsidwa ndi anthu. Mpingo weniweni umapangidwa ndi mzika za Ufumu wa Mulungu. Mpingo weniweni ndi thupi la uzimu la anthu okhulupirira limene Mulungu anakhazikitsa komanso amagwiritsa ntchito pofalitsa Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi. Mpingo umewu umapangidwa ndi amayi ndi abambo onse opezeka mu Ufumu wa Mulungu.

Cholinga cha mpingo sikungolalika Uthenga Wabwino okha ayi, koma uyeneranso kuonetsera chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu. Mpingo uyenera kuchita zinthu malingana ndi mfundo za Ufumu ndi ndondomeko za Ufumu wa Mulungu zimene Yesu Khristu anaotsera ngati mfumu ya Ufumu umenewu.

Ufumu wa Mulungu wakhala ulipo kale lonse ndipo ukadalipo mpaka lero lino komanso udzakhala ulipobe mpaka mtsogolo. Pakadali pano ku dziko lakuthupi, Ufumu wa Mulungu uli mwa amayi ndi abambo amane avomeleza Yesu Khristu ngati Mfumu ya moyo wao. Mtsongolomu padzakhala Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso umene udzakhazikitsidwa. Zambiri zokhudza m'mene umakhalira ufumu wa Mulungu kale, lero lino komanso m'mene udzakhaliire mtsogolo zikabwidwa mozama patsogolo pa chaputala ichi.

Chifukwa chakuti Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wauzimu osati wakuthupi, tiyenera kuumvetsa mwauzimu

**Koma munthu wa cibandwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu:  
pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu.  
(1 Akorinto 2:14)**

### **OLAMULA AMAUFUMU**

Ufumu wa Satana umalamulidwa ndi Satana. Muphunzira zambiri mu gowo limene limakhala ndi zoonjezera pophunzira. Pachiyambi Satana anali mngelo Wabwino olengendwa ndi Mulungu ndipo iye anali gawo limodzi la Ufumu wa Mulungu, koma iye anafuna kugalukira ulamuliro wa Mulungu. Mukhoza kuwerenga za kupanduka kwa Satana mu buku la Yesaya 14:12-17 ndi Ezekiyeli 28:12-19. Angelo angapo anatsata Satana poukira Mulungu ndipo naonso anaponyedwa kunja kwa Ufumu wa Mulungu. Satana ndi angelo ake anapanga Ufumu wa Satana.

Ufumu wa Mulungu umalamulidwa ndi Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera ndipo muphunzira zambiri za olamula Ufumu wa Mulungu mu chaputala chachiwiri.

### **MZIKA ZA MAUFUMU**

Kupatula olamulira amaufumu, palinso anthu ena amene ndi mzika za maufumu auzimu amanewa. Mizimu yoipa yotchedwa ziwanda ndi imene imakhala mu Ufumu wa Satana. Mizimu imeneyi imatha kulowa mwa anthu amene ali mu Ufumu wa Satana ndikuwasowetsa mtendere komanso kuwagwiritsa ntchito kuti achite zinthu zoipa.

Chimaliziro cha dziko chisanafike, Satana adzagwiritsa ntchito aneneri onyenga ndi anthu ena otsutsana ndi Yesu Khristu. Iyi ndi dondomeko yomaliza ya Satana yofuna kupusitsa anthu ndikufuna kugwetsa Ufumu wa Mulungu. Ufumu wa Mulungu naonso uli ndi mzika zake. Ena mwa iwo angelo amene ali ndi matupi auzimu ndipo ntchito yawo ndi kutumukira anthu amene ali mu Ufumu umenewu. Ziwanda zimatukumira ntchito za Satana chimodzimodzinso mmene angelo a Mulungu amatumikilira malinga ndi chifuniro cha Mulungu.

Ngakhale kuti angelo ndi ziwanda ndi zinthu zauzimu, koma iwo nthawi zina amadzionetsera ndi maso komanso ndi mawu. Mwachitsanzo, ziwanda zikagwira munthu, munthuyo amatha kulakhula kapena kuchita mwa uchimo. Nthawi zina angelo amathanso kuonekera ku thupi kapena kuoneka ndi maso munjira zosiyasiyana.

Kupatula zinthu zauzimu zimene zatchulidwazi, anthu onse amakhala mu Ufumu wa Mulungu kapena wa Satana.

## **KULOWA MU UFUMU WA MULUNGU.**

Limodzi mwa mafanizo a Yesu Khristu limaonetsa kuti munthu akhoza kukhala miza ya Ufumu wa Mulungu kapena wa Satana. Yesu Khristu anayekeza dziko lapansi ndi munda. Mbeu zabwino m'munda zikuyimira ana a Mulungu amene ali mu Ufumu wake pamene mbeu yoipa imene imamera ngati nansongole kapena tchire m'munda ikuyimira ana a oipayo.

**Ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi nansongole ndiye ana a woipayo; (Mateyu 13:38)**

Munthu amalowa mu Ufumu wa Satana pamene wangobadwa kuthupi. Izi zili chomwechi chifukwa munthu amabadwa ndi mbeu ya uchimo kotero kuti zofuna zakuthupi za munthu zimakhala zoipa.

**Onani, ndinabadwa m'mphulupulu: Ndipo mai wanga anandilandira m'zoipa. (Masalmo 51:5)**

**Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. (Aroma 5:12)**

**pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)**

Chifukwa chakuti timabadwa ndi Chikhalidwe cha uchimo, munthu wina aliyense ilipo nthawi ina imene anakhalapo gawo la Ufumu wa Satana. Cholinga chenicheni cha Baibulo limene ndi mau a Mulungu ndi chofunika kumkopa munthu kuti achoke mu Ufumu oipa ndikulowa ufumu wangwiro wa Mulungu.

Polingalira kuti munthu amabadwira mu Ufumu wa Satana, chifukwa cha chakubadwa ku thupi lochimwa, munthu akuyenera kubadwanso ku uzimu. Tiphunzira zambiri zokhudza izi mu chaputala 4 pamene tione zokhudza zifungulo *zinayi za Ufumu wa Mulungu*.

Iwo amene abadwa mwatsopano amasintha umzika wao kuchokera mu Ufumu wa Satana ndi ndikusamukira mu Ufumu wa Mulungu. Iwo amasintha kudzipereka kwa Satana ndikuyamba kudzipereka kwa Mulungu. Pamene alowa mu Ufumu wa Mulungu, ayenera kuphunzira mfundo kapena ndondomeko zimene zimatsatidwa mu moyo wa Ufumu wa Mulungu. Izi zili ngati kuphunzira kahalidwe chatsopano ku dziko limene inu mwangosamukira kumene. Muphunzira zambiri zokhudza mfundo zofunika zimenezi mu phunziro lina la muphunziro amenewa.

## UBALE PAKATI PA MAUFUMU

Kuchokera nthawi imene Satana anaukira Mulungu, pakhala pali nkondo yaikulu yauzimu pakati pa Ufumu wa Satana ndi Ufumu wa Mulungu. Baibulo linaonetsera za nkondo yapakati pa maufumu awiriwa.

Nkhondo yauzimu ndi yolimbilana maganizo, moyo komanso mzimu wa Munthu. Satana akuyesayesa kuti akamange anthu mu goli la tchimo mu Ufumu wake pakugwiritsa ntchito njira zake zopusitsa anthu. Iye amakomedwetsa amayi ndi abambo kuti akwanilitse zilakolako zoipa zathupi zakanthawi kochepe chabe. Iye amalimbana ndi anthu ake a Mulungu

**Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wochulukana (Yohane 10:10)**

Nkhondoyi ikhala ikupitilabe mudziko lauzimu mpaka chimaliziro cha nthawi. Phunziro lokhudza nkondo yauzimu ndi lozama ndipo chifukwa cha ichi, pali phunziro lapadera limene Harvestime International Institute likupereka limene limene limafukula za *ndondomeko za nkondo yauzimu*. Phunziro limeneli limatsindika za Ufuma wa Satana, njira zimene amagwiritsa ntchito komanso ndondomeko zongonjetsera mphamvu zakumidima.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yoloweza osaonera

---

---

2. Kodi magawikano opezeka pa 1 Akorinto 15: 44-49 akubwera chifukwa chiani?

---

3. Kodi maufumu osaoneka apadziko ndi ati?

---

---

4. Kodi olamula a maufumu osaonekawa ndi ndani?

---

---

5. Kodi Mzika za ufumu wa Satana ndi ndani?

---

6. Kodi mzika za Ufumu wa Mulungu ndi ndani?

---

7. Kodi mau akuti “Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa ku mwamba ndi osiyana bwanji?”

---

---

8. Fotokozerani tanthauzo la mau oti “Ufumu”

---

---

**(Mayanko amafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)**

## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

Phunziro ili likhazikika pa za Ufumu wa Mulungu. Koma ngati m'mene taonera mu chaputula chimenechi, pali Ufumu wina osaoneka ndi maso umene uli Ufumu wauzimu wa Satana. Ndikofunika kwambiri kuti mumvetsetse maufumu auzimu onsewa.

Pali phunziro lina la Harvestime international Institute lotchedwa *Ndondomeko Zauzimu: mlozo wa nkondo Yauzimu*. Phunziro limeli limapereka ndongomeko zolimbana ndi Satana komanso limafotokoza zambiri zokhudza Ufumu wa Satana. Muyenera kukhala ndi Buku limeneli kuti likuthandizireni kumvetsa phunziro la Ufumu wa Mulungu. Koma malingana ndi phunziro ili, m'ndandanda uli munsu ukufotokoza za Satana ndi Ufumu wake.

## UFUMU WA SATANA

### I. Wolamula wa Ufumu wa Satana: Satana

- A. Chiyamabi chake: zonse zolengedwa zinalenagedwa ndi Mulungu. Yohane 1:3, Akolese 1:16-17
- B. Ulemelero wake wakale: Yesaya 14:12-15; Ezekiyeli 28:12-17
- C. Udindo wake wakale: Ezekieli 28:14
- D. Kugwa kwake: Ezekieli.
- E. Mayina ake:

- 1. Mulungu wa dziko lapansi II Akorinto
- 2. Mngelo wa kuunika II Akoirinto 11:14
- 3. Mdierekezi 1 Petulo 5:8; Mateyu 4:1
- 4. Satana Yohane 13:27
- 5. Lusifara Yesaya 14:12
- 6. Chinjoka Chibvumbulutso 12:3
- 7. M'dani 1 Petulo 5:8

#### A. Chikhalidwe chake

- 1. Ali ndi mzeru komanso ndi ochenjera moipa 1 Akolinto 11:3
- 2. Amatha kukwiya kapena kusangalala: Chibvumbulutso 12: 17.
- 3. Ali ndi kuthekera kopanga chiganizo payekha II Timoteyo 2:26.
- 4. Ndi odzikuza: I Timoteyo 3:6
- 5. Ndi wamphamvu: Aefeso 2:2
- 6. Ndi wachinyengo: Aefeso 6:11
- 7. Ndi olusa komanso wankhanza: I Petulo 5:8
- 8. Ndi opusitsa II Akorinto 11:14

#### B. Mau olakhulidwa ndi Satana

- 1. Genesis 3:1,4,5
- 2. Yobu 1:7-12
- 3. Yobu 2:1-6
- 4. Mateyu 4:1-11
- 5. Luka 4:1-13

### II. Mizika za Ufumu Satana: Mizimu ya ziwanda

- A. Satana ndiye olamula wa ziwanda: Mateyu 12:22-28
- B. Chiyambi chao: Chibvumbulutso 12:7-9; Yuda 6
- C. Chikhalidwe chaziwanda

- 1. Mizimuyi imakhala mwa anthu Mateyu 8:16; Luka 10:17,20



2. Zimalakhula Marko 5:9,12; Luka 8:28; Mateyu 8:31
3. Zimakhulupirira: Yakobo 2:19
4. Zimatha kupanga chisankho Luka 8:32; 11:24
5. Zimaonetsera mzeru: Maliko 1:24
6. Zimatha kuonetsa chimwemwe kapena chisangalano Luka 8:28; Yakobo 2:19
7. Zimatha Kuzindikira zinthu Machitidwe 19:15
8. Zili ndi mphamvu zodabwitsa Machitidwe 19:16; Marko 5:2,3
9. Zimapezeka paliponse Danieli 9:21-23; 10:10-14

D. Kagwiridwe kawo kanchito

1. Ndi zogwirizana: Mateyu 12:26,45; Luka 8:30; I Timoteyo 4:1
2. Zimagwira ntchito mumagulu Luka 8:30
3. Kuipa kwao ndi kosiyana-siyana Mateyu 12:43-45
4. Amagwira ntchito mwadongosolo Aefeso 1:21; 3:10; 6:12; Aroma 8:30
5. Pali mitundu yosiyana-siyana ya ziwanda Mateyu 10:1; I Timoteyo 4:1

III. Mzika za Ufumu wa Satana: Anthu onse amene Sali mu Ufumu wa Mulungu: Chibvumbulutso 20:15; 21:8

IV. Malo ogwira ntchito aziwanda ndi Satana:

- A. Zimatha kupezeka pamaso pa Mulungu Yobu 1:6-7
- B. Zimapezeka dziko lonse lapansi: Chibvumbulutso 12:10

V. Ntchito za Satana ndi ziwanda:

Ntchito za Satana ndi ziwanda zafotokozeredwa bwino mu phunziro lina la Harvestime International Institute lotchedwa “*Ndondomeko Zauzimu: Mfundo zothandizira nkhondo Yauzimu*.” kungofotokozerera mwachidule, ntchito zonse za ziwanda ndi Satana zimkhala zolimbana ndi Mulungu makamaka zolinga Zake ndi anthu ake

VI. Okhulupirira ali ndi mphamvu zoposa Satana ndi ziwanda zake:

- A. Mateyu 10:1; Marko 6:7; 9:38; 16:17; Luka 10:17; Acts 5:16; 8:7; 16:16-18; 19:12
- B. Njira zolimbana ndi ziwanda ndi Satana zafotokozeredwa mu buku lotchedwa “*Ndondomeko Zauzimu: Mfundo zothandizira nkhondo Yauzimu*.”

Izi ndi ndondomeko zauzimu zimene zili zothandiza kwambiri kuti mukagwiritse ntchito mphamvu zimene Mulungu anakupatsani polimbana ndi Ufumu wa Satana.

- VII. Mathero a Ufumu wa Satana: Mateyu 8:29; 25:41; II Petulo 2:4; Yuda 6;  
VIII. Chibvumbulutso 12:7-9; 20:10; I Yohane 3:8; Luka 8:28; Mateyu 25:41

## **CHAPUTALA 2**

### **MFUMU YA UFUMU**

#### **ZOLINGA**

Pamapeto pamaphunziro awa muyenera kudziwa zinthu izi:

- Kulemba vesi yoloweza.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti mfumu.
- Kuzindikira Yesu Khristi ngati Mfumu ya mafumu.
- Kupitiliza kuphunzira za moyo ndi utumiki wa Yesu Khristu.

#### **VESI YOTSOGOLERA:**

**Ndipo iye adzacita ufumu pa banja la Yakobo ku nthawi zonse; ndipo ufumu wace sudzatha. (Luka 1:33).**

#### **MAU OYAMBA**

Palibe Ufumu umene umakhala opanda mfumu. Mu chaputala chimenechi, muphunzira za mfumu yopambana mafumu onse, Mfumu ya Mafumu imene ndi Yesu Khristu.

#### **KODI MFUMU NDI NDANI**

Mfumu ndi wolamula wa mphamvu amene amalamula mudzi, mtundu kapena dziko. Ndipo iye salamulidwa ndi wina aliyense.

Mu zaka zambiri zapitazo, panali mafumu ndi maufumu ambiri pa dziko lapansi. Mu maufumu akuthupi a dziko lapansi, malo onse amakhala m' manja mwa amfumu ndipo ulamuliro onse mu ufumuwo umakhala mwa iye.

Malamulo onse amapangindwa ndi a mfumu ndipo onse okhalamo mu ufumuwo amayenera kumvera malamulo onse.

#### **MFUMU YA MAFUMU**

Mfumu yopambana mafumu onse ndiye Yesu Khristu. Paulo akutcha iye kuti ndi Mfumu ya Mafumu:

**Limene adzalionetsa m'nyengo za iye yekha, amene ali Mwini Mphamvu wodala ndi wayekha, ndiye Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye; (1 Timoteo 6:15)**

Bukhu la Chibvumbulutso limamutcha kuti ndi mfumu ya mafumu.

**Cifukwa ali Mbuye wa ambuye, ndi Mfumu ya mafumu; ndipo adzawalakanso iwo akukhala naye, oitanidwa, ndi osankhika ndi okhulupirika. Cibvumbulutso (17:14)**

**Ndipo ali nalo pa cobvala cace ndi pa ntchafu yace dzina lolembedwa, Cibvumbulutso 19:16)**

### **MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE.**

Yesu ndi mfumu ya mafumu chifukwa amalamula ufumu umene ndi wa muyaya komanso wa mphamvu zonse. Ufumu wa Mulungu zudzatha kapena kugwetsedwa chifukwa cha kugalukira kwa anthu. Sipadzapezekanso olamula wina amene adzatenge ulamuliro m'manja mwa mfumu ya mafumu.

### **MFUMU YAKALE LOMWE**

Baibulo limafotokoza za mfumu ya Mafumu. Ndipo gawo limodzi ya nkhani imeneyi ndi utumiki wake wa Yesu Khristu pa dziko lapansi. Koma iye chiyambi chake ndi chakale chifukwa analipo angakhale utumiki wake wapadziko usanayambe. Mukhoza kuwerenga za chiyambi chake chakale lomwe pa Yohane 1:1-18. Mu ndime imeneyi Yesu Khristu akutchedwa “Mawu”

### **MA ULOSI OKHUDZA MFUMU**

Chipangano chakale chili ndi ma ulosi ambiri okhudza Mfumu ya Mafumu. Ulosi ndi mau amene amalukhulidwa ndi Mulungu okhudza tsogolo ndipo munthu sangadziwe izi kugwiritsa ntchito nzeru za umunthu.

Ulosi wa chipangano chakale umavumbulutsa nthawi imene mfumu idzabadwe, m'mene idzabadwire ndi zina zambiri zokhudza mfumuyi monga moyo wake, imfa ndi Chiukitso chake. Chipangano Chatsopano chimaonetsera kukwanilitsidwa kwa ma ulosi amenewa.

(mndandanda wina okhudza ma ulosi amenewa waperekededwa muphunziro la Haverstine International Institute lotchedwa Ndondomeko zosanthulira Baibulo)

## **KUBWADWA KWA YESU KHRISTU**

### **MAKOLO A YESU MONGA MWA THUPI**

Mukhoza kuwerenga zamakolo ake a Yesu monga munthu pa Mateyu 1:1-17 and Luka 3:23-38.

Mbiri ya makolo ake akuthupi imaonetsera bambo ndi mayi apa dziko lapansi. Koma kumbukirani kuti Yesu anali mwana wa Mulungu obadwa kwa namwali; Mariya.

### **KUBADWA KWA MFUMU**

Mukhoza kuwerenga zambiri zakubadwa kwa Yesu kuthupi mu mabuku a Mateyu 1 ndi Luka 1 ndi 2.

### **MAYINA A MFUMU YAMAFUMU**

Yesu Kristu amatchedwa ndi mayina ambiri ena mwa mayina amenewa amaonetsera utumiki wake komanso cholinga chake. Ena mwa mayina a Mfumu ya Mafumu ndi awa:

Adamu wachiwiri:	I Akorinto 15:45-47
Nkhoswe:	I Yohane 2:1
Wamphamvu:	Chibvumbulutso 1:8
Afa ndi Omega:	Chibvumbulutso 21:6
Ameniyo:	Chibvumbulutso 3:14
Nkhalamba yakale lomwe:	Danieli 7:9
Mnthenga wakuimilira pamaso pache	Yesaya 63:9
Odzodzedwa pakati pa abale ake:	Salimo 45:7
Mtumwi wachivemerezo chatu:	Aheberi 3:1
Mkondo wa Yehoha:	Yesayan 51:9-10
woyamba ndi otsiriza wachukhulupiriro chatu:	Aheberi 12:2
wopereka chipulumutso chamuyaya:	Aheberi 5:9
wobadwa wa Mulungu:	I Yohane 5:18
wokondeka:	Aefeso 1:6
woyang'anira moyo wathu:	I Petulo 2:25
Odala ndi wayekha:	I Timoteyo 6:15
Nthanda Zaka:	Zakariya 3:8
Nthambi, chilungamo:	Yeremiya 23:5
Nthambi ya chilungamo:	Yeremiya 33:15
Nthambi ya Muzu wa Jese:	Yesaya 1:1
Mkate wa Moyo:	Yohane 6:35
Nthanda yonyezimira ya mamawa:	Chivumbulutso 22:16

Kazembe wankhondo wa Yehova:  
mwana wa mpala matabwa:  
Mwala wapangodya:  
Womveka mwa zikwi Khumi:  
Khristu:  
Khristu ambuye:  
Khristu Yesu Mbuye wathu:  
Khristu mphamvu ya Mulungu:  
Wauphungu  
Pangano la anthu:  
M'banda kucha wakumwamba  
Nthanda:  
Mpulumutsi:  
Khomo:  
Osankhidwa:  
Emanueli:  
Moyo wosatha:  
Tate wamuyaya:  
Wokhulupirika ndi woona:  
Mboni yokhulupiririka:  
Woyamba kubadwa wa Mulungu:  
Woyamba kubadwa:  
Woyamba kubadwa pakati pa abale aka  
Zipatso zoyamba:  
Oyamba ndi otsiriza:  
Maziko oikidwa ku Zayoni:  
Mbuye waulemelo:  
Mulungu wa Israeli:  
Mulungu ali nafe:  
M'busa Wabwino:  
Mulungu wamkulu:  
Wansembe wamkulu:  
Mutu wathupi:  
Mutu wa Zonse:  
Mwala wapangodya:  
Wolowa mnyumba wa zinthu zonse:  
Odzodzedwa wake:  
Woyera wa Israeli:  
Chiyembekezo cha ulemelo:  
INE NDINE:

Yoswa 5:15  
Mateyu 13:55  
I Petulo 2:6  
Nyimbo 5:10  
Yohane 1:41  
Luka 2:11  
Aroma 8:39  
I Akorinto 1:24  
Yesaya 9:6  
Yesaya 42:6  
Luka 1:78  
II Petulo 1:19  
Aroma 11:26  
Yohane 10:9  
Yesaya 42:1  
Mateyu 1:23  
I Yohane 5:20  
Yesaya 9:6  
Chibvumbulutso 19:11  
Chibvumbulutso 1:5  
Ahebri 1:6  
Salimo 89:27  
Aroma 8:29  
I Akorinto 15:23  
Chibvumbulutso 22:13  
Yesaya 28:16  
Yesaya 33:21  
Yesaya 45:15  
Mateyu 1:23  
Yohane 10:11  
Tito 2:13  
Aheberi 4:14  
Akoloese 1:18  
Aefeso 1:22  
Salimo 118:22  
Aheberi 1:2  
Salimo 2:2  
Yesaya 41:14  
Akolose 1:27  
Yohane 8:58

Chifaniziro cha Mulungu osaoneka:	Akolose1:15
Immanueli:	Yesaya 7:14
Yesu Mbuye wathu:	Aroma 1:3
Oweruza wa Israyeli:	Mika 5:1
Mfumu ya ulemelero:	Salimo 24:7
Mfumu:	Zakariya 9:9
Mfumu yadziko lonse:	Zakariya 14:9
Nkhosa ya Mulungu:	Yohane 1:29
Kuunika kwa dziko lapansi:	Yohane8:12
Duwa lofira:	Nyimbo 2:1
Mkate wa moyo:	Yohane 6:51
Mbuye Mulungu wamphamvu:	Chibvumbulutso 4:8
Mbuye ndi mpulumutsi Yesu	II Petulo 2:20
Mbuye wa onse:	Machitidwe 10:36
Mbuye chilungangamo cathu:	Yeremiya 23:6
Mbuye mombolo:	Yesaya 43:14
Chikondi:	I Yohane 4:8
Munthu wa zisoni:	Yesaya53:3
Mtsogoleri:	Mateyu 23:10
Mesiya:	Danieli 9:25
Mulungu wa mphamvu:	Yesaya9:6
Wamphamvu wa Yakobo:	Yesaya 60:16
mthenga wa Mulungu:	Ekisodo 23:20-23
Woyeretsetsa:	Danieli 9:24
Waphamvu zonse:	Salimo 45:3
Nazarete:	Mateyu 2:23
Mulungu yekhayo wamzeru	I Timoteyo 1:17
Pasaka wathu:	I Akorinto 5:7
Sing'anga:	Luka 4:23
Kalonga wa mtendere:	Yesaya 9:6
Kalonga wa mafumu a dziko lapansi:	Chibvumbulutso 1:5
Mneneri:	Deteronome 18:15-18
Chotetezera:	Aroma 3:25
Mphunzitsi:	Yohane 1:49
Mpulumutsi:	Yesaya 59:20
Chiukitso:	Yohane 11:25
Kapolo olungama:	Yesaya 53:11
Thanthwe:	I Akorinto 10:4
Muzu wa Jese:	Yesaya 11:10
Duwa lofiira la ku Saroni:	Nyimbo 2:1

Mpulumutsi wa dziko lapansi:	I Yohane 4:14
Mbeu ya Davite:	Yohane 7:42
Mbeu ya mkazi	Genesis 3:15
Mwana wa Mulungu:	Aroma 1:4
Mwana wa munthu:	Machitidwe7:56
Mwana wa Mariya:	Maliko 6:3
Mwana wa wamkulu:	Luka 1:32
Nyenyezi m'yakobo:	Numeri 24:17
Mwala	Mateyu 21:42
Dzuwa la chilungamo:	Malaki 4:2
Mwala wa maziko:	Yesaya 28:16
Mphuzitsi	Yohane 3:2
Choonadi	Yohane 14:6
Mphatso yosaneneka:	II Akorinto 9:15
Mphesa:	Yohane 15:1
Njira:	Yohane 14:6
Wodabwitsa:	Yesaya 9:6
Mawu:	Yohane 1:14
Mawu a Mulungu:	Chibvumbulutso 19:13

### **MBIRI YA MOYO WA MFUMU**

Mabuku Mateyu, Luka ndi Maliko amafotokoza mbiri ya mayo wa Mfumu Yesu. Mabuku amanewa analembedwa ndi ophunzira anayi a Yesu Khristu amene anatumukira naye mu utumuki wake.

### **UTUMIKI WA MFUMU**

Utumiki ndi chiphunzitso cha Yesu Khristu chimapezeka mu mabuku a Maliko, Mateyu, Luka ndi Yohane. Mdandanda onse wa zimene Yesu amaphunzitsa zikupezeka mu phunziro la Harvestime International Institute ndipo phunziroli limatchedwa “*Ukadaulo wa kuphunzitsa*”

Ngakhale kuti pali zambiri zimene zalembedwa mu Mauthenga Abwino zokhudza moyo ndi utumiki wa Yesu Khristu, koma Yohane akufotokozanso kuti:

**Koma palinso zina zambiri zimene. Yesu anazicita, zoti zikadalembedwa zonse phe, ndilingalira kuti dziko lapansi silikadakhala nao malo a mabuku amene akadalembedwa. Amen(Yohane21:25)**

### **MFUMU YOKANIDWA**



Malingana ndi makolo ake akuthupi, Yesu Khristu anabadwa ku fuko la chiyuda. Iye anadza ngati Mfumu ya anthu ake omwe a chiyuda koma iwo anamukana. Iye anafunsidwa ngati anali Mfumu yolonjezedwayo. (Mateyu 27:11; Maliko 15:2) Anthu anamuganizira kuti ndi ochokera kwa Satana osati kwa Mulungu. (Mateyu 12:25-28; Luka 11:17-20) Iyi Inali nthawi ina imene anthu anafuna kukakamiza Yesu Khristu kuti amudzodze ngati mfumu yawo. Koma chifukwa chakuti iye samakhazikitsa Ufumu owoneka ndi maso umene iwo amayembekezera, anamuganizira kuti ndi ochokera kwasatana. (Yohane 6:15)

Inalipo nthawi ina imene anthu anamulandira Yesu Khristu ngati Mfumu. Iyi inali nthawi yake yotsiliza kuti afike munzinda wa Yerusalemu. (Mateyu 21 :1-9) koma anthu omwewo amene analemekeza iye ngati mfumu anamuukiranso. Iwo anafuula kuti “Hosana” pamene amalowa mu Yerusalemu. Anthu omwewanso ndi amene anafuula kuti “mpachikeni”. Anthu amenewa anali okhumudwa kuti Yesu sanagwetse kapena kuti kuthetsa ulamuliro wankhanza wa Aroma ndikukhazikitsa ufumu wa mphamvu wa dziko lapansi. Kotero kuti anthu amene anali ndi chiyembekezo choti Iye adzawalanditsa ku alamuliro wa Aroma anali ndi mkwiyo chifukwa sanakwanilitse Ufumu wa padziko lapansi.

Yesu Khristu sanali mfumu imene Ayuda amayembekezera. Iye sanakwanitse kugonjetsa ulamuliro wachiroma. Iye sanakhazikitse Ufumu wa padziko lapansi umene iwo amayembekezera. Ndipo iye sanachite zinthu molingana ndi mmene iwo amayembekezera kuti mfumu iyenera kuchitira. Chimene iwo sanazindikire ndi chakuti Yesu amayenera kaye kulamulira mitima ya anthu asanayambe kulamulira kuthupi.

Chosowa chachikulu cha Ayuda sichinali kukhala ndi ufulu kuchokera kwa Aroma, koma kumasulidwa ku nsinga zauchimo. Chifunguro cha Ufumu wa Yesu Khristu chinali kulapa osati kugalukira ulamuliro wachiroma. (muphunzira zambiri zokhudza izi mu chaputala cha patsolo).

Satana anamuyesa Yesu Khristu kuti akhazikitse Ufumu owoneka ndi maso wapadziko lapansi (Mateyu 4:8; Luka 4:5;) Kufikira chimaliziro cha utumuki wake, ophunzira a Yesu amayembekezera kukhazikitsidwa kwa Ufumu wapadziko lapansi (Machitidwe 1:6) Koma Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso sumayenera kukhazikitsidwa nthawi imeneyo. Yesu anati:

**... Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkondo, kuti ndisaperekedwe kwa Ayuda; koma tsopano ufumu wanga suli wocokera konkuno (Yohane 18:36.)**

Choncho Mfumu inakanidwa ndi anthu ake:

**Anadza kwa zace za iye yekha, ndipo ace a mwini yekha sanamlandira iye. (Yohane 1:11)**

Anali anthu ochepa amene anazindikira kuti Yesu ndi Mfumu. Natanayeli ndi m' modzi mwa ophunzira amene anazindira izi:

**Natanayeli anayankha Iye, Rabi, 14 Inu ndinu Mwana wa Mulungu, 15 ndinu Mfumu ya Israyeli, (Yohane 1:49)**

koma anthu ochepa okhawa amene anazindikira Yesu Khristu ngati Mfumu, vumbulutso lapadera limapelekedwa kwa iwo:

**Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu akukhulupirira dzina lace. (Yohane 1:12)**

Moyo wathu umakhazikika pa maubale. Chinthu chofunukira kwambiri sizimene mumadziwa, koma anthu amene inuyo mumawadziwa. Chimodzimodzi, sizimene timadziwa zokhudza Baibulo zimene zingatipangitse kuti tilowe mu ufumu wa Mulungu koma zimatengera amene tikumudziwa. Ndipo muyenera kudziwa Mfumu ya Mafumu. Mu chaputala chokhudza *zifungulo za Ufumu wa Mulungu*, muphunzira mmene mungalowere mu Ufumu ndi kukhazikika mu Ufumu wa Mulungu.

### **IMFA YA MAFUMU**

Munthu ochimwa sangalowe mu Ufumu wa Mulungu. Ufumu wa Mulungu unali osiyana ndi ma ufumu ena chifukwa unali Ufumu wangwiro. Imfa ya Yesu Khristu inapereka mwayi kuti onse akathe kukhala gawo limodzi la Ufumu wa Mulungu. Panalibe chilichonse chimene Yesu Khristu anachita chomuyeneleza iye kuti afe. Iye sanachimwe koma anafa ndi cholinga choti akafere onse ochimwa. Iye analipira chilango cha imfa kuti apulumutse onse kumachimo awo.

**Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 6:23)**

Mukhoza kuwerenga zokhudza imfa ya Mfumu Yesu mu mabuku a Mateyu 26-27, Maliko 14-15, Luka 22-23 ndi Yohane 18-19.

### **CHIUKITSO CHA MFUMU**

Ataphedwa pa mtanda paja, Mfumu inaikidwa m' manda koma zinakanika kuti akhalebe m' mandamo. Mukhoza kuwerenga nkhani ya Chiukitso cha Yesu Khristu mu mabuku a Mateyu 28, Maliko 16, Luka 24 ndi Yohane 20.

Kudzera mu Chiukitso chake kwa akufa, Yesu Khristu anagonjetsa imfa ya kuthupi. Ngakhale kuti onse amene ali mu Ufumu wa Mulungu amakumana ndi imfa, iwo adzaukitsidw kwa akufa

ngati mmene zinachitikira ndi Yesu. Chifukwa chakuti Mfumu yathu ndi yamuyaya, ifenso ndi gawo limodzi la Ufumu wa muyaya ndipo tidzakhala ndi moyonso wa muyaya.

### **KUONEKERA KWA MFUMU**

Atauka kwa akufa, Yesu Khristu anaonekera kwa anthu osiyanasiyana. Mukhoza kuwerenga zambiri zokhudza kuonekera kwa Yesu mu mabuku awa: Mateyu 28, Maliko 16, Luka 24, Yohane 20 -21 ndi Machitidwe 1.

### **KUKWERA KU MWAMBA KWA MFUMU**

Yesu ataonekera kwa anthu kwa masiku okwana makumi anayi, Iye anabwelera kumwamba. Iye apitilizabe kukhala kumwamba kufukira nthawi yobweranso kudzakhazikitsa Ufumu omaliza itafika. Muphonzira zambiri za kale la Ufumu, mzamtsogolo ndi zinthu zina zochitika lero lino zokhudza Ufumu wa Mulungu. Mukhoza kuwerenga zakubweranso kwa Yesu Khristu mu mabuku awa. Mateyu 28:16-22, Maliko 16:19-20, Luka 24:50-53 ndi Machitidwe 1:1- 11

### **KUTUMA KWAKULU KWA A MFUMU**

Asanakwere kumwamba, Iye anapereka lamulo lalikulu kapena kuti kutuma kwakulu, analamula ophonzira ake onse kuti akhale akazembe a Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi. Muphonzira zambiri zakutumidwa mu machuputala apatsogolo.

### **KUBWERANSO KWA MFUMU**

Baibulo limafotokoza kuti Yesu Khristu adzabweranso ndi ulemelero komanso ndi mphamvu kudzakhazikitsa Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso. Mukhoza kuwerenga zokhudza kubweranso kwake pa 1 Atesalonika 4:13-18. Werengani zakukhazikitsidwa kwa Ufumu ndi zinthu zina zotsatira mu buku la Chibvumbulutso. Baibulo limaonetsera kuti Ufumu wa Mulungu ndi wamuyaya.

**...ndipo Ufumu wake sudzatha. (Luka1:33)**

Ufumu wina uli onse wa padziko lapansi ndi wa Satana udzagonjetsedwa ndi Mfumu ya Mafumu. Pachimaliziro cha zonse kudzalengezedwa kuti:

**Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Kristu wace: ndipo adzacita ufumu kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 11:15)**

## **PITIRIZANIBE MAPHUNZIRO ANU**

Nkhani ya Ufumu wa Mulungu ndi yayikulu kwambiri kotero kuti ndi zovuta kuti itambasulidwe bwino lomwe mu chaputala chimodzi. Chifukwa cha ichi, ndime ya zoonjezera pophunzira ikupatsani mwayi oti muphunzirebe za moyo wa Yesu mwa tsatane-tsatane kudzera mu mabuku a Maliko, Mateyu ndi Yohane.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

---

2. Fotokozerani tanthauzo la mau oti “Mfumu”

---

---

3. Kodi Mfumu ya Ufumu wa Mulungu ndi ndani?

---

4. Ndi mabuku ati a Chipangano Chatsopano amene amafotokoza za moyo, utumiki ndi chiphunzitso cha Yesu Khristu.

---

---

---

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizana kuphunzira za moyo wa Mfumu ndi chiphunzitso cha Ufumu wa Mulungu pogwiritsa ntchito mndanda uli pansiwu. Mndandanda umeneu ukuchokera mu mabuku a chipangano Chatsopano a Maliko, Luka, Mateyu ndi Yohane.

### MFUMU NDI UFUMU WAKE

- I. Chiyamabi chake chakale lomwe. Yohane 1:1-18
- II. Kufotokozera za Mfumu
  - A. Kubwera kwake
    1. Makolo ake ayesu akuthupi Mateyu 1:1-17; Luka 3:23-38
    2. Kubwera kwake:
      - a. Kulengeza zakubadwa kwa Yohane Luka 1:5-25
      - b. Kulengeza zakubadwa kwa Yesu kwa Maria Luka 1:26-38
      - c. Kufika kwa Mariya mu Yudeya Luka 1:39-45
      - d. Matamando a Mariya: Luka 1:46-56
      - e. Kubadwa kwa Yohane Luka 1:57-80
      - f. Kulengezedwa zakubadwa kwa Yesu kwa Yosefe Mateyu 1:18-25
      - g. Kubadwa kwa Mfumu Yesu Luka 2:1-7
      - h. Kulengezedwa zakubadwa kwa Yesu kwa abusa ang'ombe Luka 20:8-20
    3. Umwana mwa Mfumu Yesu
      - a. Kudulidwa kwa Mfumu Yesu: Luka 2: 21
      - b. Kuperekedwa kwa Yesu kukachisi: Luka 2: 22-38
      - c. Umwana wa Yesu
        1. Ku Betelehemu: Mateyu 2:1-12
        2. Ku Iguputo: Mateyu 2:13-18
        3. Ku Nazareti: Mateyu 2:19-23; Luka 2:39
      - d. Umwana wa Mfumu
        1. Kukula kwa mfumu: Luka 2:40
        2. Mfumu ipita ku Yerusalemu: Luka 2: 41-50
        3. Kukula kwa mfumu Luka 2:51-52
    - B. kalambura bwalo: Yohane M'batizi
      1. Uthenga wa Yohane
      2. Uthenga wa Yohane: Mateyu 3:1-6; Marko 1:2-6; Luka 3:3-6
      3. Kufotokozera kwa Yohane: Mateyu 3:7-10; Luka 3:7-14
      4. Kulonjeza kwa Yohane: Mateyu 3:11-12; Maliko :7-8; Luka 3:15-18
  - III. Kuchitilidwa Umboni kwa Mfumu
    - A. Umboni ochitilidwa:
      1. Pa ubatizo wake Mateyu 3:13-17; Maliko 1:9-11; Luka 3:21-23
      2. Kuyesedwa kwake Mateyu 4:1-11; Maliko 1:12-13; Luka 4:1-13

3. Kalambula bwalo wake: Yohane: 3:1-12
  - a. Umboni wa Yohane kwa atsogoleri: Yohane 1:19-28
  - b. Umboni wa Yohane kwa Yesu Khristu: Yohane 1:29-34
- B. Kuchitilidwa umboni kwa Mfumu
  1. Kukhulupirira kwa ophunzira Oyamba: Yohane 1:35-51
  2. Chikhulupiro kudzera mu chozizwa choyamba Yohane 2:1-12
  3. Kuyeretsa kachisi Yohane 2:13-22
  4. Kuvomelezedwa ku Yudeya: Yohane 2: 23-3:21
  5. Umboni wa Yohane: Yohane 3: 22-36
  6. Mu Zebuloni kapena Nefitale: Mateyu 4:12; Maliko 1:14; Luka 3:19-20; 4:14; Yohane 4:1-4
  7. Kuvomelezedwa ku Samariya Yohane 4:5-42
  8. Kuvomelezedwa ku Galilea 4:43-45
- C. Ulamuliro wa Mfumu Yesu
  1. Ulamuliro olalika: Mateyu 4:17; Maliko 1:15; Luka 4:14-15
  2. Ulamuliro pa matenda: Yohane 4:46-54
  3. Kukanidwa kwa ulamuliro wake ku Nazareti: Luka 4:16-30
  4. Kukhala kwake ku kapenamu Mateyu 4:13-16
  5. Ulamuliro wake pa zonse zolengedwa: Mateyu 4:18-22; Marko 1:16-20; Luka 5:1-11
  6. Ulamuliro wake pa ziwanda Maliko 1:21-28; Luka 4:31-37
  7. Ulamuliro pa matenda Mateyu 8:14-17; Marko 1:29-34; Luka 4:38-41
  8. Ulamuliro pa zonse zodetsedwa Mateyu 8:1-4; Maliko 1:40-45; Luka 5:12-16
  9. Ulamuliro okhululukira tchimo Mateyu 9:1-8; Maliko 2:1-12; Luka 5:17-26
  10. Ulamuliro wake pa anthu onse: Mateyu 9:9-13; Marko 2:13-17;
  11. Ulamuliro pazikhalidwe: Mateyu 9:14-17; Maliko 2:18-22; Luka 5:33-39
  12. Ulamuliro wake pa Sabata:
    - a. Kuchiza munthu wopuwala: Yohane 5:1-47
    - b. mtsutso pa ngala za tiligu: Mateyu 12:1-8; Maliko 2:23-28; Luka 6:1-5
    - c. Kudzera kuchiza munthu opuwala dzanja Mateyu 12:9-14; Marko 3:1-6; Luka 6:6-11
  13. Ulamuliro wake ochilitsa: Mateyu 12:15-21; Marko 3:7-12
  14. Ulamuliro wake otuma Marko 3:13-19; Luka 6:12-16
  15. Ulamuliro wake otha kutambasula chilamulo: Mateyu 5:1-7:29; Luka 6:17-42
    - a. Iye ndiye kukwaniritsidwa kwa malembo Mateyu 5:17-20
    - b. Kutsutsana ndi kamvetsetsedwe ka chilamulo mwa chizolowezi:
      1. Kupha: Mateyu 5:21-26

2. Chigololo: Mateyu 5:27-30
  3. Kulekana banja: Mateyu 5:31-32
  4. Kulumbira: Mateyu 5:33-37
  5. Kubwezera: mateyu 5:38-42
  6. chikondi: Mateyu 5:43-48; Luka 6:27-30; 32-36
  - c. kutsutsana ndi zochita za Afarisi:
    - (2) kupereka: Mateyu 6:1-4
    - (2) Pemphero: Mateyu 6:5-15
    - (3) Kusala kudya: Mateyu 6:16-18
    - (4) kaganizidwe pa chuma: Mateyu 6:19-24
    - (5) kupanda chikhulipiriro: Mateyu 6:25-34
  - d. Malangizo kwa iyo adzalowe mu Ufumu:
    - (1) Pemphero: Mateyu 7:7-11
    - (2) Ungwiro: Mateyu 7:12; Luka 6:31, 43-45
    - (3) Njira ya mtanda: Mateyu 7:13-14
    - (4) Chenjezo kwa aphunzitsi onyenga: Mateyu 7:15-23
    - (5) Maziko awiri: Mateyu 7:24-8:1; Luka 6:46-4
17. kuvomelezedwa kwa ulamuliro wa mfumu ku kapenau: Mateyu: 8:5-13, Luka 7:1-10
18. kuvomelezedwa kwa ulamuliro wa Mfumu: Luka 7:11-17
19. kuchitira umboni za Ufumu wa Mulungu kwa ophunzira khumi ndi awiri: Mateyu 9:35-11: Marko 6:6-13

#### IV. Mpungwepungwe okhudza Mfumu

- A. Kukanidwa kwa Yohane: Mateyu 11:2-19; Luka 7:18-35
    - I. Imfa ya Yohane Mateyu 14:1-12; Marko 6:14-29; Luka 9:7-9
  - B. Mizinda yaku Galileya itembeledwa Mateyu 11:20-24
    1. Atembeledwa chifukwa chakusakhulupirira Mateyu 11:20-24.
    2. Kufotokozera kusakhulupirira kwao Mateyu 11:20-24
    3. Kuitanidwa kuti akhulupilire Mateyu: 11:25-27
  - C. Mpungwepungwe pa ochimwa Luka 7:36-50.
  - D. Kuchitira umboni za mfumu Luka 8:1-3
  - E. Kukanidwa kwa Mfumu ndi atsogoleri Mateyu 12:22-37; Marko 3:19-30
  - F. Atsogoleri afuna chizindikiro kuchokera kwa Mfumu: Mateyu 12:38-45
  - G. Kukanidwa ndi fuko lonse Mateyu 12:46-50; Marko 3:31-35; Luka 8:19-21
  - H. Mavumbulutso amfumu
    1. Ufumu lero lino Mateyu 13:1-53; Marko 4:1-34;
    2. Ulamuliro pa chilengedwe Mateyu 8:18, 23-27; Marko 4:35-41; Luka 8:22-25
    3. Ulamuliro pa dziwanda Mateyu 8:28-34; Marko 5:1-20; Luka 8:26-39
    4. Ulamuliro pa kusapenya Mateyu 9:27-34
    5. Mphamvu pa matenda Mateyu 9:18-26; Marko 5:21-43;
- V. Malangizo a Mfumu kwa ophunzira.



- A. Kudyetsa kwa anthu zikwi zisanu Mateyu 14:13-21; Marko 6:30-44; Luka 9:10-17; Yohane 6:1-13
- B. Kukanidwa kwa Ufumu: Mateyu 14:22-23; Marko 6:45-46; Yohane 6:14-15
- C. Aphunzits pogwiritsa chitsanzo ku Genesareti: Mateyu:34-36; Marko 6:53-56
- D. Aphunzitsa za mkate wa moyo: Yohane 6:22-71
- E. Aphunzitsa zakudetsedwa: Mateyu 15:1-20; Marko 7:1-23; Yohane 7:1
- F. Chiphunzitso ku:
  - 1. Taya ndi sido: Mateyu 15:21-28; Marko 7:24-30
  - 2. Dekapoli: Mateyu 15:29-38; Marko 7:31-8:9
  - 3. Magadala: Mateyu 15:39-16:4; Marko 8:10-12
  - 4. Chenjezo la kukanidwa: 6:5-12; Marko 8:13-26
- G. Chivomelezo cha Petro: Mateyu 16:13-20; Marko 8:27-30; Luka 9:18-21
- H. Chiphunzitso chokhudza imfa ya Yesu ya Mfumu: Mateyu 16:21; 17:22-23; Marko 8:31-33; 9:30-32; Luk 9:22; 43-45.
- I. Kupanga ophunzira: Mateyu 16:22-28; Marko 8:34-9:1; Luka 9:23-27
- J. Mavumbulutso a Ufumu wa Mulungu: Mateyu 17:1-8; Marko 9:2-8; Luka 9:28-36
- K. Chiphunzitso chokhudza Eliya: 17:9-13; Marko 9:9-13.
- L. Chiphunzitso cha kudalira: Mateyu 17:14-21; Marko 9:14-29; Luka 9:37-43
- M. hiphunzitso cha umwana: Mateyu 17:24-27
- N. Kudzichepetsa: Mateyu 18:1-5; Marko 9:33-37; Luka 9:46-48
- O. Kunyada: Mateyu 18:6-14; Marko 9:38-50; Luka 9:4
- P. Kukhulukilana: Mateyu 18:15-35
- Q. Kupanga ophunzira: Mateyu 8:19-22; Luka 9:57-62
- R. Cholepheletsa cha abale ake a Yesu: Yohane 7:2-9
- S. Ulendo waku Yerusalemu: Luka 9:51-56; Yohane 7:10

VI. Kulimbana ndi Mfumu:

- A. Mkangano pa chikondwewero cha mahema
  - 1. Afunsa za Ulamuliro wa Yesu: Yohane 7:11-15
  - 2. Mfumu ifotokozera: Yohane 7:16-24
  - 3. Umunthu wa Yesu Yohane 7:16-24
  - 4. Mfumu ifotokozera: Yohane 7:28-30
  - 5. Anthu achitapo kanthu: Yohane 7:31-36
  - 6. Kuitana kwa mfumu: Yohane 7:37-52
- B. Mphungwepungwe pa chilamulo:
- C. Kusamvana pa zakuunika: Yohane 8:12-20
- D. Kuzamvana pa zokhudza kuti Yesu ndi ndani: Yohane 8:21-59
- E. pa kuchilitsidwa munthu kwa munthu wakhungu: Yohane 9:1-41
- F. kusamvana pa za m'busa: Yohane 10:1-21
- G. kuchitira umboni kwa anthu asanu ndi awiri: Luka 10:1-24
- H. kusamvana pa za moyo osatha: Luka 10:25-37
- I. Kusamvana pa mphwando la kuzonzetsanso Yerusalemu Yohane 10:22-39
- J. kusamvana pa machilitso a munthu osalakhula: Luka 11:14-36
- K. kusamvana pa zikhalidwe: Luka 11:37-54

VII. Chiphunzitso cha Yesu kwa ophunzira ake:

- A. Chiphunzitso chachiyanjano Luka 10:38-42
- B. Chiphunzitso cha pemphero: Luka 11:1-13
- C. Mfundo za Ufumu wa Mulungu

- 1. Chinyengo: Luka 12:1-12
- 2. Kusilira: Luka 12:13-34
- 3. Kuyang'anira: Luka 12:35-41
- 4. Kukhulupilira: Luka 12:42-48
- 5. Zotsatira za kubwera kwachiwiri kwa Yesu: Luka 12:49-53
- 6. Zizindiliro za nthawi: Luka 12:54-59
- 7. Kulapa: Luka 13:1-9
- 8. zosowa za Israeli: Luka 13:10-17
- 9. zochitika za Ufumu wa Mulungu: Luka 13:18-21

- D. Kuchoka ku Yudea Yohane 10:40-42
- E. Chiphunzitso chokhudza kulowa Ufumu wa Mulungu Luka 13:22-35
- F. Chiphunzitso munyumba ya Mfarisi: Luka 14:1-24.
- G. Chiphunzitso cha mfundo za Ufumu wa Mulungu za:

- 1. Kupanga ophunzira: Luka 14:25-35
- 2. Mmene Mulungu amaonera ophunzira: Luka 15:1-32
- 3. Chuma: Luka 16:1-31
- 4. Chikhulukiro: Luka 17:1-6
- 5. Kutumikira: Luka 17:7-10

H. Chiukitso:

- 1. Chodabwkwitsa Yohane 11:1-44
- 2. Kulimbana chifukwa cha chozizwa: Yohane 11:45-54

I. Chiphunzitso chokhudza Ufumu wa Mulungu cha:

- 1. Kuthokoza: Luka 17:11-19
- 2. Kubwera kwa Mfumu: Luka 17:20-37
- 3. Pemphero: Luka 18:1-14
- 4. Chilekano: Mateyu 19:1-12; Marko 10:1-12
- 5. Kulowa mu Ufumu wa Mulungu Mateyu 19:13-15; Marko 10:17-31; Luka 18:31-34
- 6. Israeli: Mateyu 20:29-34; Marko 10:46-53; Luka 18:35-43
- 7. Chikhulupiro: Luka 19:1-10
- 8. Kuimitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu: Luka 19:11-28

VIII. Kuonetseredwa kwa Mfumu.

- A. Mfumu ifika ku Betaniya: Yohane 11:55-12:1, 9-11
- B. Kulowa mu Yerusalemu: Mateyu 21:1-11, 14-17; Marko 11:1-11; Luka 19:29-44; Yohane 12:12-19
- C. Ulamuliro wa Mfumu: Mateyu 21:12-13, 18-19; Marko 11:12-18; Luka 19:45-48
- D. Kuitana kwa mfumu: Yohane 12:20-50
- E. Chizindikiro cha Ulamuliro: Mateyu 21:20-22; Marko 11:19-25; Luka 21:37-38
- F. Ulamuliro wa Mfumu ukaikilidwa:

1. Ndi ansembe ndi akulu: Kukanidwa kwa Mfumu: Mateyu 21:23-22:14; Marko 11:27-12:12; Luka 20:1-19
2. Ndi Afarisi ndi Aherodi: Mfundo za Ufumu zokhudza Nsonkho: Mateyu 22:15-22; Marko 12:13-17; Luka 20:20-26
3. Ndi Asaduki: Mfundo za ufumu za chiukitso: Mateyu 22:23-33; Marko 12:18-27; Luka 20:27-40
4. Ndi Afarisi: Lamulo lalikulu mu Ufumu wa Mulungu: Mateyu 22:34-40; Marko 12:28-34

G. Funso la khristu Yesu. Mateyu 22:41-46; Marko 12:35-37;

H. Mfundo Yakuweruza: Mateyu 23:1-39; Marko 12:38-40; Luka 20:45-47

I. I. Mfundo ya Ufumu: Marko 12:41-44; Luka 21:1-4

#### XI. Kukonzekera Imfa ya Mfumu.

##### A. Kulosera kwa Mfumu

1. Funso: Mateyu 24:1-3
2. Mazunzo: Mateyu 24:27-30
3. Kubwera kwa Yesu kwachiwiri: Mateyu 4:27-30
4. Kusonkhanitsidwa Kwa Israeli: Mateyu 24:31
5. Mafanizo a chimaliziro chanthawi:
  - b. Kapolo okhulupilka: Mateyu 24:45-51
  - c. Anamwari khumi: Mateyu 25:1-13
  - d. Ma Talenti: Mateyu 25:14-30

#### 6. Chiweruzo cha anthu amitundu: Mateyu 25:31-46

##### B. Kukonzekera imfa ya Yesu:

1. Kulosera za Imfa ya Mfumu: Mateyu 26:1-2; Marko 14:1; Luka 22:1
2. Chikonzero cha olamulira: Mateyu 26:3-5; Marko 14:1-2; Luka 22:2
3. Adzodzedwa mafuta: Mateyu 26:6-13; Marko 14:3-9; Yohane 12:2-8
4. Ulosi wakuperekedwa kwa Yesu: Mateyu 26:14-16; Marko 14:10-11; Luka 22:3-6
5. Kukonzekera pasaka: Mateyu 26:17-19; Marko 14:12-16; Luka 22:7-13
6. Pasaka: Mateyu 26:20; Marko 14:17; Luka 22:14-16; 24-30
7. Kuperekedwa Kwa Chitsanzo: Yohane 13:1-20
8. Kulosera za Kukanidwa kwa Yesu ndi Petro Yesu ndi Yudasi: Mateyu 26:21-25; Marko 14:18-21; Luka 22:21-23; Yohane 13:21-30
9. Kulosera kukanidwa kwa Yesu: Mateyu 26:31-35; Marko 14:27-31; Luka 22:31-38; Yohane 13:37-38
10. Chikumbukiro: Mateyu 26:26-30; Marko 14:22-26; Luka 22:17-20

##### C. Uthenga omaliza wa Mfumu:

1. Chiyambi: Yohane 13:31-35
2. Zovuta: Yohane 13:36-14:24

3. Malonjezani: Yohane 14:25-31

4. Malangizo okhudza

- a. Kubala chipatso: Yohane 15:1-17
- b. Adani a ophunzira: Yohane :18-16:4
- c. Utumiki wa Mzimu Woyera: Yahane 16:5-15
- d. Zotsatira za Chiukitso: Yohane 16:16-28
- e. Chimaliziro: Yohane 16:29-33

D. Pemphero lomaliza la Mfumu:

1. Pemphero lodzipephelera yekha: Yohane17:1-5
2. Pemphelero lake kwa ophunzira ake: Yohane 17:6-19
3. Pemphero lake kwa okhulupilira onse: Yohane 17:20-26

E. Pemphero mmunda: Mateyu 26:36-46; Marko 14:32-42; Luka 22:39-46; Yohane 18:1

X Imfa ya Mfumu:

A. Kumangidwa: Mateyu 26:47-56; Marko 14:43-52; Luka 22:47-53; Yohane 18:2-12

B. Kuimbidwa mlandu kwa Mfumu ndi akulu achipembedzo:

2. Kuimbidwa mlandu ndi Kayafa: Mateyu 26:57, 59-68; Marko 14:53, 55-56; Luka 22:54, 63-65; Yohane 18:24
3. Kukanodwa ndo Petro: Mateyu 26:58, 69-75; Marko 14:54; 66-72; Luka 22:54-62; Yohane 18:15-18, 25-27
4. Chiganizo cha bwalo lamilandu: Mateyu 27:1; Marko 15:1; Luka 22:66-71.
5. Imfa Ya Yudas: Mateyu 27:3-10

C. Kuimbidwa mlandu kwa mfumu ndi boma

1. Kuimbidwa mlandu ndi Pilato: Mateyu 27:2, 11-14; Marko 15:2-5; Luka 3:1-5; Yohane 18:28-3

2. Kuimbidwa mlandu ndi Herodi: Luka 23:6-12.

3. Kuimbidwa Mlandu ndi Pilato: Mateyu 27:15-26; Marko 15:6-15; Luka 23:13-25; Yohane 18:39-19:1, 4-16

4. Kunyozedwa kwa Mfumu: Mateyu 27:27-30; Marko 15:16-19;

F. Kuikidwa mmanda kwa Mfumu: Mateyu 27:57-60; Marko 15:42-47; Luka 23:50-56; Yohane 19:31-42

G. kutseka manda a Mfumu: Mateyu27:62-66

XI. Chiukitso cha Mfumu

A. Kukonzekera kwa azimayi: Mateyu 28:1; Marko 16:1

B. Kutsekulidwa kwa manda: Mateyu 28:2-4

C. Amayi apita kumanda: Mateyu 28:5-8; Marko 16:2-8; Luka 24:1-8; Yohane 20:1

D. Amayi adziwitsa ophunzira zachiukitso: Luka 24:9-12; Yohane 20:2-10

E. Yesu awonekera kwa Mariya: Marko 16:9-11; Yohane 20:11-18

F. Yesu awonekera kwa azimayi: Mateyu 28:9-10

G. Umboni wa alonda akumanda: Mateyu 28:11-15

H. Awonekera kwa ophunzira ku nseu ku Emau: Marko 16:12-13; Luka 24:13-32

I. Umboni wa ophunzira awiri: Luka24:33-35

- J. Awonekera kwa ophunzira khumu: Marko 16:14; Luka 24:36-43; Yohane 20:19-25
- K. Mfumu iwonekera kwa ophunzira khumi ndi mmodzi: Yohane 20:26-31
- L. Mfumu iwonekera kwa ophunzira asanu ndi awiri: Yohane 21:1-25
- XII. Kutuma kwakulu kwa Mfumu Mateyu 28:16-20; Marko 16:15-18; Luka 24:44-49
- XIII. Mfumu ikwera kumwamba kwa Mfumu: Marko 16:19-20; Luka 24:50-53

## CHAPUTALA 3

### UFUMU KALERO, LERO LINO NDI MTSOGOLO

#### ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kukwanitsa zinthu izi

- Kunena vesi yotsogolera osaonera.
- Kuonetsera Kumvetsetsa m'mene Ufumu wa Mulungu unalili kalero.
- Kuonetsera kumvetsetsa m'mene Ufumu wa Mulungu ulili lero lino.
- Kumvetsetsa m'mene Ufumu wa Mulungu udzakhalire mtsogolo.
- Kufotokozerana mfundo zofunika zokhudza Ufumu wa Mulungu.

#### VESI YOTSOGOLERA

**Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi: (Mateyu 25:34)**

#### MAU OYAMBA

Mu chaputala changopitachi tafotokozerana mfundo zochepa chabe zokhudza Ufumu wa Mulungu komanso olamula wa Ufumu wa Mulungu amene ndi Yesu Khristu. Chaputala ichi chionetsera mongodutsamo za Ufumu wa Mulungu kalero, lelolino komanso m'mene udzakhalire mtsogolo. Ndipo chaputalachi chifotokozeranso mfundo zodziwika bwino lomwe zokhudza Ufumu wa Mulungu.

Pali mutu umodzi umene umamangilira Chipangano Chakale ndi chatsopano. Mutu umewu ndi Ufumu wa Mulungu ndi Mfumuyo ya Ufumu. Mau akuti Ufumu wa Mulungu komanso Ufumu wakumwamba samapeza mu Chipangano Chakale. Mau amenewa amapezeka mu Chipangano Chatsopano. Koma pamene mukhale mukuphunzira zokhudza Ufumu wa Mulungu kalero, mupeza kuti maziko a Ufumu wa Mulungu anakhazikitsidwa mu Chipangano Chakale. Maziko a Ufumu wa Mulungu lero lino komanso mtsogolo anadzalidwa kale mu Chipangano chakale.

#### UFUMU KALERO: CHIPANGANO CHAKALE

Ufumu wa Mulungu ndi wa Muyaya. Izi zikutanthauza kuti wakhala ulipo ndipo udzala ulipobe nthawi zonse.

**Ufumu wanu ndiwo ufumu womka muyaya, Ndi kuweruza kwanu kufikira mibadwo yonse yonse. (Masalmo 145:13)**

Ufumu wa Mulungu Chiyambi chake ndi kumwamba. Chinali cholinga cha Mulungu kuti pamene akumulenga Munthu, Ufumu wa Kumwamba uja ufalikire dziko lapansi limene analenga lija.

### **MUNTHU OSANKHIDWA:**

Pofuna kukwaniritsa zolinga zake, Mulungu analenga chilengedwa cha ngwiro ndi cholinga choti akuze Ufumu Wake. M'munda wa Edeni, Mulungu analenga mamuna ndi mkazi kuti adzadze dziko lapansi. Pochulukana, ndiye kuti anthuwa amakuza Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi.

Kulengedwa kwa dziko lapansi kunali kukonzekeretsa Ufumu wa Mulungu kuti ukakule kudzera mwa munthu.

**Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi: (Mateyu 25:34)**

Munthu oyamba uja amene ndi Adamu ndi Hava, anapatsidwa ulamuliro kuti akakuze Ufumu wa Mulungu.

**Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu: alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa ng'ombe, ndi pa dziko lonse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi. Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace, m'cifanizo ca Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi. Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi. (Genesis 1:26-28)**

Mulungu sanafune kukakamiza munthu kuti atumukire Iye mu Ufumu wa padziko lapansi. Iye amafuna kuti munthu asankhe kukhala gawo la Ufumu wa Mulungu mosakakamizidwa. Chifukwa cha ichi, Mulungu anapanga lamulo mu Ufumu watsopanowu. Lamulo ili limakhazikika pa mfundo ya ufulu osankha. Kupitiriza kukhala mu Ufumu umewu kumatengera chisanko chimene munthu wapanga:

**Ndipo Yehova Mulungu anamuuza munthuyo, nati, Mitengo yonse ya m'munda udyeko; koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu. (Genesis 2:16-17)**

Mukhoza kuwerenga nkhani yokhudza chiganizo cholakwikwa chimene Adamu ndi Hava anapanga. Pamene Adamu ndi Hava anachimwa, iwo anataya cholowa chao mu ufumu wa Mulungu. Iwo anatayanso moyo wamuyaya komanso moyo wabwino wa muufumu wa Mulungu.

Chifukwa cha tchimo, panadza matembelero osiyana-siyana pa munthu, nthaka ndi Satana. Mukhoza kuwerenga zokhudza matembelero amenewa pa Genesis 3. Dziko lapansi sili nalinsu malo abwino, langwiro ngati Ufumu wa Kumwamba. Munthu analibenso ulamuliro pa chilengedwe, ndipo iye anali olekanitsidwa ndi kupezeka kwa Mulungu chifukwa cha tchimo.

Mulungu anapereka mwayi ofuna kukuza Ufumu wake kudzera mwa munthu koma munthu anakana izi. Munthu anataya cholowa chake chokozedwa ndi Mulungu kuchokera pa chiyamambi cha dziko. Chifukwa cha ichi, Satana anatenga ulamuliro wa dziko lapansi. Koma munthawi imene panalibe chiyembekezo, lonjezo la Mulungu lofuna kubwezeretsa Ufumu wa Mulungu kwa munthu linaperekedwa. Mulungu nati kwa Satana:

**Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace.  
(Genesis 3:15)**

Ili linali lonjezo loyamba la Mfumu imene tsiku lina idzabwere ndi kuononga m'daniyo amene ndi Satana. Mfumu yolonjezedwayo idzabadwa kudzera mwa mkazi. Kudzera mu imfa yake, munthu akhoza kuyeletsedwa ku tchimo, kubadwanso mwatsopano mu Ufumu wa Mulungu, kukhala ndi moyo wamuyaya, ndi kutenganso cholowa chake.

## **ANTHU OSANKHIKA**

Munthu atalephera, Mulungu anasankha mtundu umodzi ndi cholinga choti akuze Ufumu wake pa dziko lapansi. Mulungu anasakha Abrahamu ngati poyambira pa mtundu umodzi waukulu. Mulungu anapanga malonjezano ambiri okhudza Israeli komanso ofalitsa Ufumu wake pa dziko lapansi. Mukhoza kuwerenga nkhani yokhudza Abrahamu pa Genesis 12 ndi 25.

Israeli anasankhidwa ndi Mulungu ndi Cholinga, Osati kuti iwo anali opambana. Iwo sanasankhidwe chifukwa chakuti anali opambana kuposa mafuko kapena kuti Mulungu anawakonda kwambiri. Kusankhidwa kwao kunali kupatsidwa udindo wapadera. Ndipo udindo umenewu unali oti akakuze Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi. Mulungu anapereka mfundo kapena kuti malamulo okhudza Ufumu wake kwa ana a Israeli. Ambiri mwa malamulowa akupezeka mu buku la Ekisodo.

Mukudutsa kwa nthawi, mafumu a dziko lapansi amasanakhidwa kuti alamulire Ufumu wa Mulungu. Koma fuko la Israeli linalephera udindo wake okuza ufumu wa Mulungu. Mukhoza kuwerenga zokhudza kulephera kwa Israeli mu buku la Oweruza mu Chipangano Chakale.

Mulungu anafaniza Israeli ndi mphesa umene sumabala zipatso za Ufumu wa Mulungu. Ndipo mapeto ake Mulungu anati:



**Israyeli ndi mpesa wotambalala, wodzibalira wokha zipatso; monga umo zinacurukira zipatso zace, momwemo anacurukitsa maguwa a nsembe ace; monga mwa kukoma kwace kwa dziko lace anapanga zoimiritsa zokoma. Mtima wao wagawikana, tsopano adzapezeka oparamula, adzapasula maguwa ao a nsembe, nadzaononga zoimiritsa zao. Pakuti tsopano adzati, Tiribe mfumu, popeza sitiopa Yehova; ndi mfumu idzaticitira ciani? (Hoseya 10:1-3)**

**Ndipo Ine ndinakuoka mpesa wangwiro, mbeu yoona; kodi bwanji wandisandukira Ine mbeu yopanda pace, ya mpesa wacilendo? (Yeremiya 2:21)**

Chifukwa chakuti anakana Ufumu wa Mulungu komanso udindo wao oti akuze ufumu umenewu, Isreali anakhala fuko logawikana. Anagawikana mu mafuko a Yuda ndi Israeli. Koma mapeto ake, mayiko onsewa anagonjetsedwa ndi anthu amitundu.

Koma posatengera kulephera kwao, Mulungu analonjeza kuti Ufumu wake udzabwezeretsedwa ndipo Israeli adzakhala gawo limodzi la Ufumu uemeu. Mulungu anaperekanso malonjezano okhudza kubwera kwa Ufumu ndi mfumu yake mtsogoro.

Malonjezano anaperekedwa kwa to Davide (II Samueli 7:16; Salimo 22:27-28; 72:7-11; 89:1-4; 96 and 98) kwa Yeremiya (Jeremiya 3:17-18; 23:5-6; 31:31-34). Malonjezano anaperekedwanso kwa mneneri Yesaya (Yesaya 2:2-5; 33:20-22; 35; 62:1-2; 65:17-25). Malonjezano anaperekedwa kwa Ezekieli (Ezekieli 26:25-30; 37:22-28), Yoweri (Yoweri 2:28), Zekariya (Zakariya 8:20-23; 12:10; 14:9-17), Amosi (Amosi 9:15), ndi Mika (Mika 4). Panalinsu malonjezano ena amene anaperekedwa kupatula awa.

Fuko la Israeli linali kudikira kubwera kwa Mesiya amene adzakwanilitse malonjezano amenewa. Iwo anali kudikira kudza kwa ufumu umene udzawalanditse iwo m’manja mwa adani awo ndipo alinso kudikira kubwenzeretsedwa kwa Ufumu wakale.

## **UFUMU WA MULUNGU KALERO**

Pali vesi yofunika kwambiri imene imalumikizitsa Ufumu wa Mulungu mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano.

**Cilamulo ndi aneneci analipo kufikira pa Yohane; kuyambira pamenepo ulalikidwa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu, ndipo munthu ali yense akangamira kulowamo. (Luka 16:16)**

Ma ulosi a chipangano Chakale analosera zakubwera kwa Ufumu wa Mulungu ndipo Chilamulo cha Chipangano Chakale chinadzala mfundo za moyo wa Ufumu wa Mulungu mu Chipangano Chatsopano. Kubwera kwa Yesu sikunafafanize chilamulo koma kukwanilitsa chilamulocho komanso kukuza maziko a mfundo za Ufumu wa Mulungu.

Pamene Yohane M'batizi anali kufuula mu chipululu cha ku Yudeya ndi kulengeza kuti “ufumu wa Mulungu wayandikira”, iye amayankhula zinthu zimene zinali zomvetsetseka ndi ana a Isreali a anthawi imeyo. Iwo anali ndi chiyemebekezo chachikulu chakubwera kwa Ufumu wa Mulungu ndi mfumu ya Ufumu umeneu.

**Ndipo masiku aja anadza Yohane Mbatizi, nalalikira m'cipululu ca Yudeya, nanena, Tembenukani mitima; cifukwa Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Pakuti uyu ndiye ananenayo Yesaya mneneri, kuti, Mau a wopfuula m'cipululu, Konzani khwalala la Ambuye, Lungamitsani njira zace. (Mateyu 3:1-3)**

#### **MUNTHU OSANKHIDWA:**

Mu Chipangano Chakale, Mulungu anasankha Adamu ndi cholinga choti akakuze Ufumu wa Mulungu dziko lonse lapansi. Koma Adamu analephera kukwanitsa udindo wake. koma mu Chipangano Chatsopano, Mulungu asankha munthu m' modzi kuti akakuze Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi. Yesu anakwaniritsa cholinga cha Mulungu chofuna kukuza Ufumu wa Mulungu ndipo ichi chinali cholinga chake chachikulu cha utumiki wake.

Yohane M'batizi atamangidwa ndi kuphedwa, Yesu Khristu anayamba kulalika Uthenga wa Ufumu wa Mulungu.

**Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 4:17)**

Mu utumiki wake wa dziko lapansi, Yesu Khristu anasankha anthu angapo kuti akhale ophunzira ake. Ndipo iye analamula iwo kuti akalalike nati “Ufumu wa Mulungu wayandikira’ (Mateyu 10:7). Kodi mau oti “wayandikira amanthauza chiani? Onani kagwiritsidwe ntchito ka mau omwewa mu nthawi zosiyana:

**Ukani, timuke; taonani, iye wakundipereka wayandikira. (Mateyu 26:46)**

Pamene Yesu Khristu amakamba kuti amene adzandipereke ali nane pafupi, iye amatanthauza Yudasi, amatanthauza kuti nthawi yoti aperekedwe yafika ndipo pamene Yesu amafotokoza kuti ufumu wayandikira. Izi zimatanthauza kuti kuti Ufumu wa Mulungu wafika. Moyo wonse wa Yesu Khristu anakhala akuuza anthu kuti Ufumu wayandikira, kuphunzitsa mfundo za kakhaliidwe ka muufumu wa Mulungu komanso kufotokozerana m'mene anthu angalowere mu Ufumu wa Mulungu.

**Ndipo pamene Afarisi anamfunsa iye, kuti, Ufumu wa Mulungu ukudza liti, anawayarikha, nati, Ufumu wa Mulungu sukudza ndi maonekedwe; ndipo sadzanena, Taonani uwu, kapena uwo! Pakuti, taonani, Ufumu wa Mulungu uli m'kati mwa inu. Luka 17:20-21**

Mafaniza a Ufumu wa Mulungu amene Yesu Khristu anaphunzitsa amafanizira Ufumu ndi mbeu ya mpiru imene inabisika munthaka, komanso ngati chuma chobisika munthaka. Muzitsanzo zonsezi, Ufumu wa Mulungu ukuoneka kuti wafika koma ndi osaoneka ndi maso.

Israeli anali kuyembekezera kuti Ufumu wa Mulugu udzabwera mwa mphamvu ndipo udzakhala owoneka ndi olamulidwa ndi mfumu yowoneka ndi maso.

**Ndipo pakumva izi iwo, iye anaonjeza nanena fanizo, cifukwa anali iye pafupi pa Yerusalemu, ndipo iwo anayesa kuti Ufumu wa Mulungu ukuti uonekere pomwepo. (Luka 19:11)**

Fanizo limene Yesu Khristu amafotokoza ndi la munthu wina wake amene anapita ku dziko lakutali ndipo adzabweranso kudzalandira Ufumu wa Mulungu. Pamene Yesu Khristu anali pafupi kulowa mu mzinda wa Yerusalemu, anali akuwakonzekeretsa anthu za imfa yake. Kudzera mu fanizo limeli, iye anaonetsera kuti Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso wayimitsidwa kaye kufikira kubweranso kachiwiri kwa Yesu Khristu pamene udzakhazikitsidwe.

Ana a Israeli anali kukhulupirira kuti mfumu yakudzayo idzakhazikitsa ufumu wamphamvu owoneka ndi maso ngati m'mene unalili Ufumu wa Davide. Mulungu analonjeza mfumu Davide Kuti:

**Iye adzamangira dzina langa nyumba, ndipo ndidzakhazikitsa cimpando ca ufumu wace ku nthawi zonse. 2 Samueli 7:13**

Pamane Yesu Khristu anali kulowa mu Yerusalemu, anthu amaona ngati kuti iye akudzakhazikitsa Ufumu owoneka ndi maso umene likulu lake lidzakhale Yerusalemu. Izi ndi malingana ndi ulosi wa Chipangano Chakale. Chifukwa cha ichi, anthu anamulemekeza Yesu ngati Mfumu pamene anali kulowa munzinda wa Yerusalemu. Iwo anafuula nati:

**Wolemekezeka Ufumu ulinkudza, wa atate wathu Davide; Hosana m'Kumwambamwamba. (Marko 11:10)**

Koma mu nthawi imeneyi, Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso unali usanakhazikitsidwe. Yesu anali atepereka chitsanzo cha mkate wachotupitsa pofuna kuonetsera kuti Ufumu wa Mulungu ukufalikira pang'onopang'ono chimodzimidzi ndi m'mene chotupitsa chimafalikira mu mkhate (Mateyu 13:33)

Mu nthawi imeneyi Yesu anali atafotokoza kale za fanizo la munthu wina olemekwezeka amene anapita dziko lakutali koma nabwelera kuti adzalandire Ufumu wake. koma Israeli sanamvetse za mafanizo a Ufumu wa Mulungu. Chifukwa chakuti yesu sanakhazikitse ufumu owoneka ndi

maso, anthu omwe aja amene anamulandira ngati mfumu anamutembenukira ndikumukana. Ndipo anapempha kuti aphedwe popachikidwa.

Pamene Yesu Khristu anali padziko lapansi, Ufumu wa Mulungu unali utafika kale. Chifukwa chakuti sunafike malingana ndi m'mene iwo amayembekezera, Ayuda anakana mfumu ndi ufumu wake.

**Anadza kwa zace za iye yekha, ndipo ace a mwini yekha sanamlandira iye. Koma onse amene anamlandira iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace; amene sanabadwa ndi mwazi, kapena ndi cifuniro ca thupi, kapena ndi cifuniro ca munthu, koma ca Mulungu. (Yohane 1:11-13)**

Chifukwa chakuti anamukana iye, Yesu Khristu analengeza kuti Ufumu wa Mulungu udzachotsedwa pakati pa Ayuda ndi ndikuperekedwa kwa anthu amene akhoza kubara chipatso chagwiro.

**Cifukwa cace ndinena kwa inu, 2 Ufumu wa Mulungu udzacosedwa kwa inu, nudzapatsidwa kwa anthu akupatsa zipatso zace. (Mateyu 21:43)**

Chimene amatanthauza Yesu ndi chakuti Ufumu wa Mulungu udzaperekedwa kwa anthu amitundu. Izi zili chomwechi chifukwa iwo anali okonzeka kuulandira.

Yesu anauza Yerusalemu ndi Israeli kuti adzaweruzidwa ndi Mulungu.

**Ndipo adzagwa ndi lupanga lakuthwa, nadzagwidwa ndende kunka ku mitundu yonse ya anthu; ndipo mapazi a anthu akunja adzapondereza kufikira kuti nthawi zao za anthu akunja zakwanira. (Luka 21:24)**

Kamba koti Israeli anakana Ufumu wa Mulungu ndi Mfumu ya Ufumu umenewu, kukhazikitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi kunayimitsidwa kufikira kubweranso kachiwiri kwa Yesu Khristu.

## **ANTHU OSANKHIDWA**

Mu Chipangano Chakale, Mulugu anasankha Israeli ngati gulu la anthu limene lidzagwire ntchito yokuza Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi lonse. Koma Israeli analephera udindo umenewu. Ndipo Mulungu akusakha mpingo ngati gulu la anthu amene analandira Uthenga Wabwino ndikutenga udindo okuza Ufumu Wabwino.

Mtumwi Paulo amene anasankhidwa kuti akalalike Uthenga Wabwino kwa anthu a mitundu analembe:

**Kwa ine wocepa ndi wocepetsa wa onse, oyera mtima anandipatsa cisomo ici, ndilalikire kwa amitundu cuma cosalondoleka ca Kristu; ndi kuwalitsira onse adziwe makonzedwe a cinsinsico, cimene cinabisika ku yambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse; kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu: (Aefeso 3:8-11)**

Mpingo ndi gulu la anthu osaoneka ndi maso limene udindo wake ndi kukuza Ufumu wa Mulungu pa dziko lonse lapansi. Werengani mfundo zalembedwa pachithuzi chili pansichi.

Mpingo wa dziko lapansi lonse -----> Ufumu wa Mulungu  
Mipingo ing'ono ing'ono imene Ufumu wa Mulungu umaoneker kudzera mwa iyo---->  
Mpingo  
Anthu amene amapanga mpingo -----> Okhulupirira

Yesu Khristu anasiyira mpingo udindo:

**Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse (Marko 16:15)**

Iye anaukonzekeretsa mpingo ndi mphamvu kuti ukwaniritse udingo umeu.

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)**

Pamapeto pa zonse, zinthu zonse zidzakhala pansu pa ulamuliro wa mfumu Yesu amene adzabwera kudzakhazikitsa Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso.

## **UFUMU WA MULUNGU LERO LINO**

Yesu Khristu anaphunzitsa kuti Ufumu wa Mulungu uli mwa ife anthu tonse. Izi zikutanthauza kuti pamene pali mfumu ndipo ulamuliro wa mfumuyo umalemekezedwa, pamene ndiye kuti pali Ufumu wa Mulungu. Dziko lapansi ndi malo omwe kugalukira kwa munthu motsutsana ndi Mulungu kumaonekera. Chifukwa cha tchimo, dziko lapansi linatembeleredwa ndipo Satana anatengelapo mwayi ofuna kukhazikitsa Ufumu wake oipa. Zinaonekeratu kuti Satana ndiye olamula wa dziko lapansi pamene iye anamuyesa Khristu Yesu mchipuluru.

**Pomwense mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitari, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi, ndi ulemerero wao; nati kwa Iye, Zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansu ndi kundigwadira ine. Pomwepo Yesu ananena kwa iye, Coka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, Ndipo Iye yekha yekha udzamlambira (Mateyu 4:8-10)**

Sikuti Mulungu anasiya ulamuliro wake ngati Mfumu chifukwa chakugalukira kwa munthu. Koma Mulungu anatsindika ganizo lake lofuna kukhazikitsa Ufumu wa Mulungu.

**Ndipo masiku a mafumu aja Mulungu wa Kumwamba adzaika ufumu woti sudzaonongeka ku nthawi zonse, ndi ulamuliro wace sudzasiyidwira mtundu wina wa anthu, koma udzaphwanya ndi kutha mafumu ao onse nudzakhala cikhalire. (Danieli 2:44)**

Ufumu wa Mulungu ndi wa lero lino komanso ndi wamtsogolo. Sikuti ndi chinthu chimene chidzachitike mtsogolo komanso chimene sitingachidziwe kufikira nthawi imene Ufumu udzakhazikitsidwe, imene ili chimaliziro cha dziko lapansi. Ulamuliro wa Ufumu wa Mulungu pakadali pano uli kuzindikiridwa mkati mwa mitima ya anthu okhao amene amakhulupirira Mulungu. Ulamuliro waufumu ukupezekanso mu mpingo wa Khristu Yesu ndi pena paliponse pamene pali kukonda Mulungu, kubadwa mwatsopano komanso ndiponse pamene anthu akutsogozedwa ndi mfundo za Ufumu wa Mulungu m'moyo wawo.

Baibulo limafotokoza kuti Ufumu wa Mulungu ndi chinsisi chachikulu chifukwa sungamvetsetseke ndi maso athu akuthupi. (marko 4: 11)

**Ndipo pamene Afarisi anamfunsa iye, kuti, Ufumu wa Mulungu ukudza liti, anawayarikha, nati, Ufumu wa Mulungu sukudza ndi maonekedwe; (Luka 17:20).**

Ufumu wa Mulungu ukhoza kuzindikiridwa mwa uzimu pano padziko lapansi. Kapena tikhoza kunena kuti Ufumu unakhazikitsidwa kale kuuzimu koma Ufumu owoneka ndi maso sunakhazikitsidwe. Ufumu owoneka ndi maso pakadali pano uli kumwamba. Koma kumwamba kumene tikukamba si mitambo imene timaona ndi maso athu. Uku ndi kumwamba kumene Yesu Khristu amakhala asanabwere pa dziko lapansi (Yohane 17:5). Uku ndi kumwamba kumene Iye anakwera atauka kwa akufa (Machitidwe 1:9-11)

Kumwamba ndi malo amene Mulungu komanso Yesu amakhalako mowoneka ndi maso. Awa ndi malo amene Yesu Kristu akudikira kuti nthawi yobweranso ikwane kuti adzakhazikitse Ufumu wa Mulungu komaliza. Pamene ali kumwamba, Iye amakhala akupembedzera anthu onse okhulupirira. Pakadali pano ali kudzanja ka manja la Atate. (Aheberi 7:25)

## UFUMU WA MULUNGU MTSOGOLO

Ngakhale kuti Yesu Khristu anauza ophunzira ake kuti Ufumu wa Mulungu wafika ndipo kuti unali pakati pawo, Iye anawonetseranso kuti ufumu wa Mulungu ndi wamtsogolo. Anaphunzitsa ophunzira ake kuti adzipemphera kuti Ufumu wa Mulungu udze (Mateyu 6:10)

Ophunzira a Yesu amkayemebekezera kuti Yesu Khristu akhazikitsa Ufumu wa Mulungu asanaphedwe pamtanda paja. Chifukwa cha ichi, Yesu ataphedwa anakhala anthu opanda chiyembekezo. Koma chiyembekezo chao chinabwerelanso atamva kuti Yesu wauka. Pakati pa nthawi ya Chiukitso chake ndikubweleranso kumwamba, Yesu analankhula zinthu zambiri zokhudza Ufumu wa Mulungu. Izi zinawapangitsa iwo kuti afunse: “kodi mudzabweretsa Ufumu wa Mulungu kwa Israeli pakadali pano. (Machitidwe 1:6) Ndipo Yesu ananayakha nati:

**... Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene Atate anaziika m'ulamuliro wace wa iye yekha (Macitidwe 1:7).**

Kubwera kwa Ufumu wa Mulungu ndi kwachidziwikire, koma nthawi yakukhazikitsa Ufumu wa Mulungu owoneka ndi maso amadziwa ndi Mulungu Tate. Yesu Khristu anafotokoza zinthu zambiri zimene ziyenera kuchitika Ufumu wa Mulungu usanakhazikitsidwe. Zizindikiro zimenezi zinavumbulutsidwa ndi cholinga chofuna kuthandiza okhulupirira kuti azindikire pamene nthawi yatsala pang'ono. Mukhoza kuwerenga zizindikiro izi pa Mateyu 24 and 25, Marko 13 ndi Luka 17:20-37; 21:8-36. Yesu anauza ophunzira ake kuti pamene zinthu izi zichitika adziwe kuti kubwenzeretsedwa kwa Ufumu owoneka ndi maso kwayandikira.

**Inde coteru inunso, pakuona zinthu izi zirikucitika, zindikirani kuti Ufumu wa Mulungu uli pafupi. Luka 21:31**

### **KULALIKIDWA KWA UTHENGA DZIKO LONSE NDI CHIYAMABI CHA CHIMALIZIRO:**

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro Mateyu 24:14**

### **YESU ADZABWERANSO PA DZIKO LAPANSI:**

**... Yesu amene walandiridwa kunka Kumwamba kucokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita Kumwamba. (Macitidwe 1:11)**

### **YESU ADZAGONJETA MA UFUMU ONSE A DZIKO LAPANSI:**

**Pomwepo pali cimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera ciweruzo conse, ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe. Pakuti ayenera kucita ufumu kufikira ataika adani onse pansi pa mapazi ace (1Akorinto 15:24-25)**

**Ndipo mngelo wacisanu ndi ciwiri anaomba, ndipo panakhala mau akulu m'Mwamba, ndi kunena, Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Kristu wace: ndipo adzacita ufumu kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 11:15)**

#### **SATANA NDI MZIKA UFUMU WAKE ADZAGONJETSEDWA:**

**Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi Sulufule, kumeneko kulonso ciromboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi (Cibvumbulutso 20:10).**

#### **MAFUKO ONSE A DZIKO LAPANSI ADZAYANJANITSIDWA MU UFUMU:**

**Ndipo ndinena ndi inu, kuti ambiri a kum'mawa ndi a kumadzulo adzafika, nadzakhala pamodzi ndi Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo, mu Ufumu wa Kumwamba; (Mateyu 8:11)**

#### **ANTHU ONSE ADZABVOMELEZA KUTI YESU NDI MFUMU:**

**Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipi 2:9-11)**

**Ndipo ndinamva ngati mau a khamu lalikuru, ngati mkokomo wa madzi ambiri, ngati mau a mabingu olimba, nizinena, Aleluya; pakuti acita ufumu Ambuye Mulungu wathu, Wamphamvuyonse. (Cibvumbulutso 19:6)**

#### **ANTHU ONSE AMOYO NDI AKUFA ADZAWERUZIDWA NDI MULUNGU:**

**Ndikucitira umboni pamaso pa Mulungu ndi Kristu Yesu, amene adzaweruzidwa amoyo ndi akufa, ndi pa maonekedwe ace ndi ufumu wace; (2 Timoteo 4:1)**

**Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo buku lina lina anatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao. Ndipo nyanja inapereka akufawo anali momwemo, ndipo imfa ndi Hade zinapereka akufawo**



**anali m'menemo; ndipo anaweruzidwa yense monga mwa nchito.  
(Cibvumbulutso 20:12-13)**

**Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa  
m'nyanja yamoto. (Cibvumbulutso 20:15)**

Yesu Khristu anafananizira Ufumu wa Mulungu ngati ukonde waukulu umene umakola nsomba zamitundu yonse. Ndipo pamapeto pake, nsomba zabwino ndi zoipa zimalekanitsidwa (Mateyu 13:47,48)

Iye anaperekanso fanizo la tiligu ndi nansongore zikukulira limodzi. Koma pamapeto pa zonse, tiligu Wabwino analekanitsidwa ndi nansongore. Chitsanzo chimenechi, chikuonetsera kuti Ufumu wa Mulungu unali utafika kale ngakhale kuti anthu oipa anakalipobe. Pakadali pano anthu oipa ndi abwino apitilirabe kukhalira limodzi kufikira nthawi ya Chiweruzo pamene adzalekanitsidwe.

Mafanizo onsewa akukamba za kulekanitsidwa kumene kudzachitike pa nthawi ya Chiweruzo. Iwo amene analowa mu Ufumu wa Mulungu kudzera mukubadwanso mwatsopano adzaloredwa. Ndipo ena onse adzaponyedwa kunja kwa ufumu wa Mulungu.

**Kudzakhala komweko kulira ndi kukukuta mano, pamene mudzaona Abrahamu,  
ndi Isake, ndi Yakobo, ndi aneneri onse, mu. Ufumu wa Mulungu, koma inu nokha  
muturutsidwa kunja. (Luka 13:28).**

**UFUMU OWONEKA NDI MASO UDZAKHAZIKITSIDWA:**

**Ndipo anampatsa ulamuliro, ndi ulemerero, ndi ufumu, kuti anthu onse, ndi  
mitundu yonse ya anthu, ndi a manenedwe onse, amtumikire; ulamuliro wace ndi  
ulamuliro wosatha ndi ufumu wace sudzaonongeka. (Danieli 7:14)**

**OKHULUPIRIRA ENIENI ADZALAMULIRA NDI YESU KHRISTU:**

**Iye wakulakika, ndidzampatsa akhale pansu ndi Ine pa mpando wacifumu wanga,  
monga Inenso ndinalakika, ndipo ndinakhala pansu ndi Atate wanga pa mpando  
wacifumu wace (Cibvumbulutso 3:21).**

**KUDZAKHALA KUMWAMBA NDI DZIKO LAPANSI LATSOPANO:**

Mukhoza kuwerenga maonekedwa a kumwamba ndi dziko lapansi pa Chibvumbulutso 21 ndi 22. Yerusalemu adzakhala mpando wachifumu wa Mulungu ndipo mafuko onse a dziko lapansi adzasokhanitsidwa.

**Pa nthawi yomweyo adzacha Yerusalemu mpando wa Yehova; ndipo mitundu yonse idzasonkhanidwa kumeneko, ku dzina la Yehova, ku Yerusalemu; ndipo sadzayendanso konse m'kuumirira kwa mtima wao woipa (Yeremiya 3:17).**

### **KUFOTOKOZERA MWA CHIDULE**

Tingofotokozerapo mwachidule zokhudza Ufumu wa Mulungu kalero, lelo lino komanso m'mene udzakhalire mtsogolomo.

<----- Ufumu wa Mulungu kumwamba----->



Ufumu wa Mulungu  
pa dziko la lapansi



kubweranso kwa mfumu  
pachimaliziri cha nthawi



kukhazikitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu owoneka ndi  
maso womaliza

kukuzidwa ndi ----->Munthu----->Israeli----->Mpingo ----->

Onani madontho amene ali pamwamba pa chithuzicho akuonetsa kuti Ufumu wa Mulungu unalipo ngakhale dziko lapansi lisanalengedwe ndipo udzakhalapo nthawi zonse.

Milozo imene ili panso pachithunzi ikuonetsa kuti Mulungu analenga dziko lapansi ngati njira imodzi yofuna kukuza Ufumu wakumwamba pa dziko lapansi. Iye anasankha munthu ngati chida chofalitsira Ufumu wa Mulungu koma munthu uja analephera udindo wake.

Kenako Mulungu anasankha mtundu wa anthu pofunu kufalitsa Ufumu wake padziko lapansi. Koma Israeli analepheranso udindo wake. Iwo anayamba kupembedza milungu yachilendo ndikuyamba kukhala molingana ndi mfundo zachikunja osati za Ufumu wa Mulungu.

Chifukwa cha kulephera kwa Israeli, Mulungu anatumiza mwana wake Yesu Khristu. Pamene Adamu analephera, Yesu Khristu ngati Adamu wachiwiri anakwaniritsa ndipo anabweletsa Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi. Yesu anapereka njira kudzera mukubadwanso mwatsopano kuti munthu akhoza kulowanso mu Ufumu wa Mulungu. Ufumu umeneu uli mwa Munthu ngakhale kuti munthuyo ali pa dziko lapansi. Chifukwa chakuti Mfumu ndi ufumu wake zinakanidwa, kukhazikitsidwa kwa Ufumu owoneka ndi maso kunayimitsidwa kufikira kubweranso kachiwiri kwa Yesu Khristu.

Pofuna kufalitsa Uthenga Wabwino waufumu, Mulungu anasankha mpingo ngati chida chofalitsira Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi. Ndipo pamene Israeli analephera, mpingo wa Mulungu sudzalephera. Pamene Uthenga Wabwino udzalalikiidwa dziko lonse lapansi, pamenepo ndi pamene Yesu Khristu adzabwerenso kachiwiri. Pamene Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa, maufumu onse adziko lapansi adzagonjetsedwa.

#### **MFUNDO ZOKHUDZA UFUMU WA MULUNGU.**

Zina mwa mfundo zokhudza ufumu wa Mulungu ndi izi.

#### **ULAMULIRA WAKE NDI MULUNGU NDIPO MPANDO WAKE ALI KUMWAMBA:**

**Yehova anakhazika mpando wacifumu wace Kumwamba; Ndi ufumu wace ucita mphamvu ponsepo. (Masalmo 103:19)**

#### **OLAMULIRA WAKE NDI MFUMU IMENE SIMASINTHA:**

**Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse. (Ahebri 13:8)**

#### **UFUMU WAKE NDI WAMUYAYA**

**Ufumu wanu ndiwo ufumu womka muyaya, Ndi kuweruza kwanu kufikira mibadwo yonse yonse. (Masalmo 145:13)**

**Komatu ndiyenera ndipite ulendo wanga lero ndi mawa ndi mkuca, cifukwa sikuloleka kuti mneneri aonongeke kunjja kwace kwa Yerusalemu. (Luka 13:33)**

**(Koma ponena za Mwana, ati, Mpando wacifumu wanu, Mulungu, ufikira nthawi za nthawi; Ndipo ndodo yacifumu yoongoka ndiyo ndodo ya ufumu wanu. (Ahebri 1:8)**

**Ha! zizindikilo zace nzazikuru, ndi zozizwa zace nza mphamvu, ufumu wace ndiwo ufumu wosatha, ndi kulamulira kwace ku mibadwo mibadwo. (Danieli 4:3)**

#### **UFUMU WA MULUNGU SUNGASITHIKE, KUGWEDEZEKA KAPENA KUONONGEDWA:**

**Mwa ici polandira ufumu wosagwedezeke, tikhale naco cisomo, cimene tikatumikire naco Mulungu momkondweretsa, ndi kumcitira ulemu ndi mantha. (Aheberi 12:28)**

#### **UFUMU WA MULUNGU UNAKONZEKERETSEDWA KUCHOKERA PA CHIYAMBI POMWE:**

**Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi: (Mateyu 25:34)**

**MULUNGU AKUFUNA KUTI CHOLOWA CHATHU CHIKHALE UFUMU WAKE:**

**Musaopa, kagulu ka nkhosa inu; cifukwa Atate wanu akonda kukupatsani Ufumu. (Luka 12:32)**

**ndipo Ine ndikuikirani ufumu, monganso Atate wanga anandiikira Ine, kuti mukadye ndi kumwa kugome kwanga mu Ufumu wanga (Luka 22:29)**

**UFUMU NDI WA MBUYE WATHU:**

**Pakuti ufumuwo ngwa Yehova; Iye acita ufumu mwa amitundu. (Masalmo 22:28)**

**Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo. (Mateyu 6:13)**

**Ndipo Yehova adzakhala mfumu ya dziko lonse; tsiku lomwelo Yehova adzakhala Iye yekha, ndi dzina lace ilo lokha. (Zakariya 14:9)**

**UFUMU WA MULUNGU NDI WAMPHAMVU KUPOSA MAUFUMU ENA ONSE:**

**Yehova anakhazika mpando wacifumu wace Kumwamba; Ndi ufumu wace ucita mphamvu ponsepo, (Masalmo 103:19)**

**UFUMU WA MULUNGU NDI WA ANTHU AMAFUKO ONSE:**

**Ndipo anthu adzacokera kum'mawa, ndi kumadzulo, ndi kumpoto, ndi kumwela, nadzakhalapansi mu Ufumu wa Mulungu. (Luka 13:29)**

**UFUMU WA MULUGU SI UFUMU WA DZIKO LAPANSI:**

**Yesu anayankha, Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkondo, kuti ndisaperekedwe kwa Ayuda; koma tsopano ufumu wanga suli wocokera konkuno. (Yohane 18:36)**

**UFUMU WA MULUNGU WAKHAZIKIKA PA MFUNDO ZAUZIMU:**

**Pakuti ufumu wa Mulungu sukhalakudya ndi cakumwa, koma cilungamo, ndi mtendere, ndi cimwemwe mwa Mzimu Woyera. (Aroma 14:17)**

**Pakuti ufumu wa Mulungu suli m'mau, koma mumphamvu, Mufuna ciani?  
(1 Akorinto 4:20)**

**MWAZI NDI THUPI ZILIBE GAWO MU UFUMU WA MULUNGU:**

**Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3)**

**Yesu anayankha, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:5)**

**PALI ZIFUNGURO ZINGAPO ZA UFUMU WA MULUNGU:**

**Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. (Mateyu 16:19)**

Ndipo zifunguro zimenezi zifotokozeredwa mu chaputala chikubwerachi.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

---

2. Papepala lapadera, lembani mwachidule mbiri yakale ya Ufumu wa Mulungu.
3. Papepala lapadera, fotokozani mwachidule za Ufumu wa Mulungu lero lino.
4. Unikilirani mwachidule mfundo zimene mwaphunzira mu muphunziro ili ndipo lembani mfundo zimene Mukhoza kukumbukira.

---

---

---

---

## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

Mu mphunziro limeneli, taphunzira kuti pali ma ufumu awiri auzimu ndipo wina aliynense ndi mzika ya umodzi mwa maufumu awiriwa. Mukhoza kukhala mu Ufumu wa Satana kapena wa Mulugu. Ndipo inu ngati muli pa dziko lapansi ndiye kuti mulinso mu ufumu wa dziko lapansi. Izi zikutanthauza kuti mumakhala m'dziko limene limayendetsedwa ndi anthu (boma)

Ma boma anakhazikitsidwa ndi Mulungu ndi cholinga chofuna kuonetsetsa kuti pali dongosolo la kachitidwe kazinthu komanso kuti malamulo akutsatidwa pano pa dziko. Mulungu ndiye amene amayenera kukhala olamula ma boma onse ndipo iwo amayenera kuyendetsedwa molingana ndi Mau a Mulungu, zolinga zake komanso dongosolo lake la Mulungu. Ndi zachidziwikire lero lino kuti maboma sakutsata ndondomeko zimene Mulungu anakhazikitsa. Ambiri mwa iwo ndi opondoleza komanso oipa. Maboma ambiri samagwiritsa ntchito mfundo za Mulungu. Kuonjezera apa, maboma ambiri ndi olamula awo amakana kuti kunjika kuno kuli Mulungu. Chifukwa cha ichi, maboma oterewa akhoza kutchidwa ma ufumu oyendetsedwa ndi Satana

Chifukwa chakuti inu mumakhala m'dziko limene limayendetsedwa ndi anthu, ndizofunika kuti muzidziwe zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza phunziro limeneli.

### **MA UFUMU A DZIKOLAPANSI**

- I. Mulungu ndiye chiyambi cha boma
  - A. Ma boma amakhazikitsidwa ndi Mulungu: Aroma 13:1
  - B. Olamulira ndi atumiki a Mulungu: Aroma 13:4,6
  - C. Mulungu amatha kukhazikitsa komanso kuchotsa ma Boma malinga ndi chifuniro chake: Danieli 4:32; 5:21; Salimo 75:7
  
- II. Cholinga cha Mulungu pokhazikitsa Boma
  - A. Cholinga choyamba cha Mulungu chinali:
    1. Kukhazikitsa dongosolo pakati pa anthu: Aroma 13:3,4
    2. Kulimbikitsa ugwiro komanso kuweruza zinthu zosayenera 13: -3-4
  - B. Ma boma anatsutsana ndi dongosolo lake
    1. Anayamba kugwiritsa ntchito ulamuro wa Mulungu pofuna kukwaniritsa zofuna za mtima zoipa I Mafumu 21:7-14
    2. Chifukwa cha ichi, Mulungu anabweretsa Chiweruzo pa onse olamula 1 Mafumu 21:19
  
- III. Udindo wa boma pa anthu ake

- A. Silieyenera kuwatsogolera anthu ku tchimo
- B. Kulimbikitsa umoyo Wabwino wa anthu: Aroma 13:1-5
- C. Kuweruza kapena kudana ndi choipa: Aroma 13:3-4
- D. Kulimbikitsa mtendere m'dziko: I Samueli 30:21-24
- E. Kuteteza ma Ufulu a mzika zake: Machitidwe 22:25-30

IV. Mfundo zothandiza olamulira:

- A. Ayenera kukhala wa nzeru: Genesis 41:33, Deteronome 1:13
- B. Ayenera kuteteza anthu osauka ndi kukuthandiza onse ovutika ndi osowa: Aroma 12:4; Salimo 82:3-4
- C. Olamula ayenera kuzindikira Mulungu ngati Mulungu Salimo 2:10-11.
- D. Olamura amene sazindikira adzachotsedwa:
  - 1. Nebukatineza: Danieali 4
  - 2. Belshazzar: Danieli 5
  - 3. Herodi: Machitidwe 12:21-23

V. Ubale wa anthu ndi boma

- A. Anthu sayenera kutsutsana ndi malamulo komanso olamula: Aroma 13:2
  - 1. Kudzipereka chifukwa cha dzina la Mulungu I Petro 2:13-14
  - 2. Kunoza kapena kuchepetsa boma ndi tchimo pamaso pa Mulungu Petro 2:10
  - 3. Anthu ayenera kumvera malamulo (Marko 12:17)
- B. Koma pali malamulo ena amene sitienera kumvera: malamuro adziko sayenera kumveledwa ngati atsutsana ndi Malamulo a Mulungu komanso Zolinga za Mulungu
  - 1. Ekisodo 1:17
  - 2. Danieli 3:18
  - 3. Machitidwe 5:29
- C. Anthu ayenera kupereka misonkho kuboma Aroma 13:6-7; Mateyu 17:25-27
- D. Mulungu nthawi zina amapereka ufumu kuti anthu asankhe boma limene akulifuna: I Samueli 8:4-9
- E. Anthu ayenera kupemphelera boma lawo 1 Timothy 2:1-

VI. Ma boma onse ndi akanthawi kochepa chabe ndipo nthawi ilipo imene sadzakhalapo: I Akorinto 15:24



## CHAPUTALA 4

### ZIFUNGULO ZA UFUMU WA MULUNGU

#### ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili, muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kupeza zifungulo za Ufumu wa Mulungu.
- Kuzindikira amene anapatsidwa zifungulo.
- Kuzindikira kuti kulapa kumatipangitsa kuti tilowe mu Ufumu wa Mulungu.
- Kuzindikira kuti kupitilira kukula m'moyo wauzimu ndikofunika kuti tilowe mu Ufumu wa Mulungu.

#### VESI YOTSOGOLERA

**Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. (Mateyu 16:19)**

#### MAU OYAMBA

Mwaphunzira kale phunziro lokhudza Ufumu wamuyaya wa Mulungu ndi mfumu yake amene ndi Yesu Khristu. Mu chaputala ichi, muphunzira m'mene mungalowere mu ufumu wa Mulungu pamene mukhale mukuphunzira “zifunguro za Ufumu”

#### UFUMU OKHAZIKITSIDWA

Yesu asanabwelere kumwamba, anauza ophunzira ake:

**Ndipo Ine ndikuikirani ufumu, monganso Atate wanga anandiikira Ine, kuti mukadye ndi kumwa kugome kwanga mu Ufumu wanga; (Luka 22:29)**

Yesu anayankhula za mpingo wake umene udzakuze Ufumu Wa Mulungu.

**Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazikitsa Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo. Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. (Mateyu 16:18-19)**

mu ndime imeyi, Yesu akuonetsera kuti Simoni Petro adzakhala m' modzi mwa maziko a mpingo oyamba. Izi zikutanthauza kuti adzatenga mbali yofunika kwambiri pakukuza Ufumu wa Mulungu. Dzina loti Petro limatanthauza kuti thanthwe.

Yesu anayankhula kuti “pa thanthwe ili ndi dzamangapo mpingo wanga” izi zikuonetsa kuti maziko a mpingo ali mwa Khristu Yesu. Ndipo padzakhala miyala ina imene idzakhale yofunika kwambiri monga Simoni Petro. Koma Yesu Khristu ndiye mwala wapangodya weniweni umene mpingo onse wakhazikikapo.

Yesu analankhula zinthu ziwiri zokhudza mpingo wake:

**Choyamba:** Ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo “izizi zikutanthauza kuti mpingo udzakhala ndi adani olimbana nawo koma sadzauogonjetsa”

**Chachiwiri:** Yesu analonjeza kupereka zifunguro za Ufumu wa Mulungu ku mpingo wake.

Kudziko lakuthupi, ngati munthu ali ndi zifungulo za nyumba ndiye kuti munthu ameneyo ali ndi ulamuliro wa nyumbayo.

Ulamuliro umene Yesu amakamba apa ndi wauzimu. Iye anapereka zifunguro zauzimu zotsekulira zitseko za Ufumu wake. Yesu ananena kuti “ndidzawapatsa iwo.” Izi zikutanthauza kuti mphamvu ndi ulamuliro wa mpingo ukuchokera mwa Khristu Yesu. Mau akuti ndidzawapatsa akutanthauza kuti zifungulozo zinali zisanaperekedwe mu nthawi imene Yesu amayankhula. Mphamvu imeneyi inaperekedwa pa Machitidwe 2 pemene Mzimu Woyera anaperekedwa kwa okhulupirira.

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)**

Zifunguro za Ufumu wa Mulungu ndi mphamvu yomanga komanso kumasula. Kumanga kuli ngati kutseka chitseko cha chipinda ndipo kumasura ndikupereka ufulu kwa chinthu kapena zili ngati kutsekula khomo lachipinda.

Chimene amatanthauza Yesu ndi chakuti mpingo udzakhala chida chotsekulira makomo a Ufumu wa Mulungu ku mayiko adziko lonse lapansi. Petulo adzakhala munthu oyamba kugwiritsa ntchito zifungulo za Ufumu wa Mulungu. Iye adzatsekula makomo a utumiki kwa anthu amitundu.

Mpingo udzakhala ndi ulamuliro omasula mphamvu zauzimu zoyenera ndi kumanga mphamvu zonse zoipa. Nyengo ina ili yonse imene okhulupirira amakumana nayo, kumanga ndi kumasula ndiye chinsisi cha chigonjetso.

## MUNGALOWE BWANJI UFUMU WA MULUNGU

Zifunguro zolowera mu Ufumu wa Mulungu zinaperekedwa ku mpingo ndi Yesu Khristu. Koma funso mkumati, kodi ndiye tingalowe bwanji mu Ufumu wa Mulungu?

Pa Yohane 3:1-21 pali nkhani ya Nikodemo amene anali wamkulu wachipembedzo. Iye anadza kwa Yesu ndi cholinga choti adziwe m'mene angalowera Ufumu wa Mulungu.

**Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3)**

Koma Nikodemo sanamvetsetse. Iye anafunsa:

**Nikodemo anati kwa iye, Munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amace ndi kubadwa? (Yohane 3:4)**

Yesu anauza Nikodemo kuti kubadwa mwatsopano kumene amakamba sikubadwanso kuthupi. Anthu amakhala mzika za dziko chifukwa chakubadwanso kuthupi.

Munthu akamabadwa kuthupi, amabadwa ndi Chikhalidwe chauchimo.

**Onani, ndinabadwa m'mphulupulu: Ndipo mai wanga anandilandira m'zoipa. (Masalmo 51:5)**

Chifukwa chakuti Ufumu wa Mulungu ndi wauzimu, muyeneranso kubadwa mu ufumu umenewu mwauzimu. Muyenera kusintha umzikawanu kuchoka mu Ufumu wa Satana ndikulowa mu Ufumu wa Mulungu.

Yesu anati:

**Cobadwa m'thupi cikhala thupi, ndipo cobadwa mwa Mzimu, cikhala mzimu. Usadabwe cifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwatsopano. (Yohane 3:6-7)**

Paulo anafotokoza kuti sitingathe kulowa mu Ufumu wa Mulungu ndi thupi ndi mwazi:

**Koma ndinena ici, abale, kuti 16 thupi ndi mwazi sizingathe kulowa Ufumu wa Mulungu; kapena cibvundi sicilowa cisabvundi. (1Akorinto 15:50)**

Njira yokhayo imene munthu angalowe mu Ufumu wa Mulungu ndikubadwanso mwatsopano pakuvomeleza kuti Yesu anatifera ndikupereka dipo la machimo athu. Muyenera kuvomeleza

machimo anu ndikupempha chikhululukiro komanso kuika chikhulupiriro chanu mwa Khristu Yesu:

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye. (Yohane 3:16-17)**

Yesu anabwera padziko lapansi ndi cholinga chofuna kukuza Ufumu wa Mulungu. Anthu ena amene anamuzindikira ngati mfumu amkaona ngati kuti Ufumu wa Mulungu ubwera kudzera mu kuukira. Iwo amkaona ngati kuti Ufumu wa Mulungu ubwera pogalukira ulamuliro wa nthawi imeneyo. Koma Yesu anaphunzitsa kuti chinsisi cha Ufumu wake ndi kulapa osati kugalukira.

**Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenekani mtima, khulupirirani uthenga wabwino. (Marko 1:14-15)**

Yesu Khristu anapachikidwa ndi abambo awiri ndipo m'modzi mwa iwo analapa napempha iye kuti:

**Ndipo ananena, Yesu, ndikumbukileni m'mene mulowa Ufumuwanu. Ndipo Iye ananena naye, Indetu, ndinena ndi iwe, Lero lino udzakhala ndine m'Paradiso. (Luka 23:42-43)**

Kulapa ndiye njira yokhayo yolowera mu Ufumu wa Mulungu.

Yesu Khristu anachenjeza kuti kudzabwera ziphunzitso zambiri zabodza komanso ananeri onyenga. Ndipo iwo adzanamiza anthu kuti iwo ndiwo njira yolowera mu Ufumu wa Mulungu.

**Lowani pa cipata copapatiza; cifukwa cipata ciri cacikuru, ndi njira yakumuka nayo kukuonongeka iri yotakata; ndipo ali ambiri amene alowa pa ico. Pakuti cipata ciri copapatiza, ndi icepetsa njirayo yakumuka nayo kumoyo, ndimo akucipeza cimeneco ali owerengeka. (Mateyu 7:13-14)**

Njira yokhayo Yolowera mu Ufumu wa Mulungu ndiye Yesu Khristu. Yesu anachenjeza kuti tiyenera kulowera pa chipata chopatiza cha Ufumu wa Mulungu Chifukwa tsiku lina chipata chidzatsekedwa:

**Yesetsani kulowa pa khomo lopapatiza; cifukwa anthu ambiri, ndikuuzani, adzafunafuna kulowamo, koma sadzakhoza. Pamene atauka mwini nyumba natseka pakhomo, ndipo inu mudzayamba kuima pabwalo, ndi kugogoda pacitseko, ndi**

**kunena, Ambuye titsegulireni ife; ndipo iye adzayankha nadzati ndi inu, Sindidziwa inu kumene mucokerako; (Luka 13:24-25)**

Pakadali pano chipata cha Ufumu wa Mulungu ndi Chotsekula. Munthu akhoza kulowa pakulapa machimo. Ikadzafika nthawi yachiweruzo, nthawi idzakhala itatha ndipo khomo lidzakhala litatsekedwa.

### **MAFANIZO ATATU AKULOWA MU UFUMU**

Yesu anafotokoza mafanizo osiyanasiyana pa Luka 15:1-32. Zambiri zokhudza mafanizo amenewa Zikambidwa mtsogolo. Mafanizo anali zitsanzo zakuthupi zimene zimaonetsera choonadi chazimu. Werengani fanizo pa Luka 15 limene limakamba za nkhoa ndi ndalama zotaika. Mafanizo onsewa akukamba zakulowa mu Ufumu wa Mulungu.

- Fanizo la m'busa akufunafuna nkhoa yotaika limaonetsera m'mene Mulungu amafunira anthu otaika kuti abwelere mu Ufumu wa Mulungu.
- Fanizo la mzimayi akufufuza ndalama yotaikayo limaonetsa kudzipereka kumene tiyenera kukhala nako pofunafuna onse otaika kuti abwerenso mu Ufumu wa Mulungu.
- Fanizo la mwana olowelera limaonetsera mfundo yakulapa ngati njira yolowera Ufumu wa Mulungu.

### **CHIKHULUPIRIRO NDIYE NJIRA**

Ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu chimene chimatitengera mu Ufumu wa Mulungu.

**Mverani, abale anga okonedwa; kodi Mulungu sanasankha osauka a dziko lapansi akhale olemera ndi cikhulupiriro, ndi olova nyumba a ufumu umene adaulonieza kwa iwo akumkonda iye? (Yakobo 2:5)**

Mtumwi Paulo akukamba za makhalidwe auzimumu amene tiyenera kufunitsitsa kukhala nawo pamene tabadwanso mwatsopano.

**Ndipo mwa ici comwe, pakutengeraponso cangu conse, muonjezerapo ukoma pa cikhulupiriro canu, ndi paukoma cizindikiritso; ndi pacizindikiritso codziletsa; ndi pacodziletsa cipiriro; ndi pacipiriro zipembedzo; ndi pacipembedzo cikondi ca pa abale; ndi pacikondi ca pa abale cikondi. Pakuti izi zikakhala ndi inu, ndipo zikacuruka, zidzacita kuti musakhale aulesi kapena opanda zipatso pa cizindikiritso ca Ambuye wathu Yesu Kristu. Pakuti iye wakusowa izi ali wakhungu, wa cimbuuzi, woiwala matsukidwe ace potaya zoipa zace zakale, Momwemo abale, onjezani kucita cangu kukhazikitsa maitanidwe ndi masankhulidwe anu; pakuti mukacita izi, simudzakhumudwa nthawi zonse; pakuti kotero kudzaonjezedwa kwa**

**inu kolemerera khomo lakulowa ufumu wosatha wa Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Kristu (2 Petro 1:5-11).**

pamene munthu walowa mu Ufumu wa Mulungu, mukuyenera kukuza Chikhalidwe chogwirizana ndi mfundo za Ufumu wa Mulungu. Ndipo ngati simuchita izi, mapeto ake mumayamba kuyiwala zimene Mulungu anakuchitirani pokutsukani kumachimo. Kenako mumabwelera ku moyo wanu wakale.

Mtumwi Petro akufotokoza kuti ngati munthu apitilira kukulabe moyo wauzimu, amakhala nacho chitsimikizo cholowa Ufumu wa Mulungu. Patsogolo pa phunziro ili, muphunzira mfundo za Chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu zimene zingathe kukuthandizani kuti mukakule moyo wanu wauzimu.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

---

2. Kodi zifunguro za ufumu wa Mulungu zinaperekedwa kwa ndani?

---

3. Kodi zifunguro za Ufumu wa Mulungu ndi chiani?

---

4. Kodi munthu achite chiani kuti achoke mu Ufumu wa Satana ndikulowa mu ufumu wa Mulungu.

---

---

5. Kodi Yesu anauza Nikodemo kuti apange chiani kuti akalowe ufumu wa Mulungu?

---

6. Kodi ndime ya II Petro 1:5-11 imaphunzitsa chiani (gwiritsani ntchito Baibulo kuti muone ndime imeneyi)

---

7. Kodi kumanga chinthu kumatanthauza chiani?

---

8. Kodi tanthauzo lakumasula ndi chiani?

---

**(Mayanko amafunso ali kumapeto kwa Buku ili)**

## **ZOONJERA POPHUNZIRA**

Mu chaputala changopitachi, tinaona mfundo zokhudza moyo wa Yesu Khristu ndi chiphunzitso chake molingana ndi Ufumu wa Mulungu. Komanso taona mfundo zingapo zokhudza Ufumu wa Mulungu.

Pakadali pano muphunzira mwatsatanetsatane Buku limodzi la Uthenga Wabwino. Buku la Mateyu linalembwedwa kupita kwa Ayuda, koma bukuli ndi la onse okhulupirira Mulungu. Mateyu akutsindika za Yesu Khristu ngati Mesiya olonjezedwa komanso ngati mfumu ya Ayuda. Mateyu anatsindikanso za Uthenga wa Ufumu Wa Mulungu umene Yesu Khristu anaphunzitsa. Ndipo chifukwa chakutsindika kumeneku, Mateyu ndi buku limodzi limene limaona zinthu molingana ndi Ufumu wa Mulungu. Mau akuti Ufumu wa Mulungu akupezeka kokwana makumi asanu ndipo iye akugwiritsanso ntchito mau oti “Ufumu wakumwamba” pofuna kukamba za Ufumu wa Mulungu.

### **Gwiritsani ntchito m’ndanda uli munsimu**

#### **Gawo Loyamba: Makolo a Yesu akuthupi**

##### **1:1-17**

- I. Chiyambi: 1:1
- II. Anthu opezeka mu makolo ake a Yesu akuthupi 1:2-16
- III. Dongosolo la makolo ake a Yesu akuthupi: 1:17

#### **Gawo Lachiwiri: Kubadwa kwa Mfumu 1:18-2:23**

- I. Kuyima kwa Mariya: 1:18-23
- II. Kubadawa: 1:24-25
- III. Zinthu zochitika zokhudza kubadwa kwake: 2:1-23
  - A. Anzeru akum’ mawa ndi chiwembu cha Herodi: 2:1-12
  - B. Kuthawira ku Ayigupto 2:13-15
  - C. Chiwembu cha Herodi 2:16-18
  - D. Kubwelera ku Nazareti 2:19-23

#### **Gawo Lachitatu: Kukonzekeretsedwa 3:1-4:11**

- I. Kukonzekera kubwera kwa Mfumu: 3:1-17
  - A. Utimuki wa Yohane M’batizi 3:1-12
  - B. Kubatizidwa kwa Mfumu: 3:13-17



II. Kukonzekera kwa mfumu: 4:1-11

- A. Satana Alimbana ndi umunthu wa Yesu Khristu: 4:1-4
- B. Satana alimbana ndi umulungu wa Yesu: 4:5-7
- C. Satana alimbani ndi Ulamuliro wa Yesu Khristu

**Gawo Lachinayi: Utumiki wa Mfumu ku Galiyeya 4:12-13:58**

- I. Kuyitana anthu Kukulapa: 4:12-17
- II. Asodzi anayi ayitanidwa kukhala ophunzira a Yesu: 4:18-22
- III. Kuchita bwino koyambilira ndi kudziwika: 4:23-25
- IV. Mfundo za chikkhalidwe cha mzika za Mu Ufumu wa Mulungu: 5:1-7:28
  - A. Maonedwe a zinthu a mzika za Ufumu wa Mulungu: 5:1-12.
  - B. Mboni za Ufumu wa Mulungu: Mchere ndi kuunika: 5:13-16
  - C. Mfundo za ufumu wa Mulungu zokhudza chilamulo ndi aneneri: 5:17-48
    - 1. Malamulo a Mulungu: 15:17-20
    - 2. Chilamulo chatsopano 15:21-48
      - a. Kupha 15:21-26
      - b. Chingololo: 15:27-30
      - c. Chilekano: 15:31-32
      - d. Malumbiro: 15:33-37
      - e. Kukhala ndi anthu ena: 15:38-48
  - D. Mapembedzedwe oyera mu Ufumu wa Mulungu: 6:1-18
    - 1. kupereka: Outward look: 6:1-4
    - 2. Kupemphera: Upward look: 6:5-15
    - 3. Kusala: kochokera mkati: 6:16-18
  - E. Zinthu zofunika kwambiri mu Ufumu wa Mulungu: 6:19-33.
    - 1. Zinthu zimene timalemekeza: 6:19-21
    - 2. Zimene mumatumikira: 6:22-24
    - 3. Zofuna zakuthupi: 6:25-34
    - 4. Zoyenera kufunafuna mu Ufumu wa Mulungu: 6:33
  - F. Kachitidwe koyenera mu Ufumu wa Mulungu: 7:1-29
    - 1. Kuweruza: 7:1-5
    - 2. Kusamalitsa zinthu zopatulika: 7:6
    - 3. Pemphero

- a. Mitundu inayi yapemphero, kupempha, kugogoda, kufunafuna.
    - b. Kusiyantsa kwa bambo wa kuthupi ndi Atate wathu wakumwamba: 7:9-11
  - G. Chenjezo lapadera kwa mzika za Ufumu wa Mulungu: 7:13-29
    - 1. Zipata ziwiri: 7:13-14
    - 2. Aneneri onyenga: 7:15-20
    - 3. Chizindikiro cha munthu wa Mulungu: kuchita chifuniro cha Mulungu: 7:21-23
    - 4. Kusiyana pakati pa munthu opusa ndi ochenjera: 7:24-27
  - H. Kuzizwa ndi chiphunzitso cha Yesu: 7:28-29
- V. Ulamuliro wa Mfumu Yesu: 8:1-9:38
  - A. Ulamuliro pamatenda: 8:1-17
    - 1. Kuchilitsa wakhate: 8:1-4
    - 2. Kuchilitsidwa kwa Kenturiyo: 8:5-13
    - 3. Kuchilitsidwa kwa mpongozi wa Petro: 8:14-15
    - 4. Kuchilitsidwa kwa matenda osiyana-siyana: 8:16-17
  - B. Ulamuliro pa ophunzira ake: 8:18-22
  - C. Ulamuliro pa chilengedwe: 8:23-27
  - D. Ulamuliro pa ziwanda: 8:28-34
  - E. Ulamuliro pa tchimo: 9:1-8
  - F. Ulamuliro pa anthu onse: 9:9-17
    - 1. Kuyitandidwa kwa Mateyu: 9:9
    - 2. Kudya limodzi ndi ochimwa: 9:10-13
    - 3. Kuyankha mafunso a anthu onse: 9:14-17
  - G. Ulamuliro pa imfa: mwana wa mkazi wa Yairo: 9:18-19, 23-26
  - H. Ulamuliro pa matenda ena onse: 9:20-38
    - 1. Mzimayi wa nthenda ya chikhalire: 9:20-22
    - 2. Khungu: 9:27-31
    - 3. Wosalankhula ndi waziwanda: 9:32-34
    - 4. Chifundo cha Khristu Yesu Khristu 9:35-38
- VI. Kutumidwa ndi mfumu: 10:1-42
  - A. Atumwi khumi ndi ulamuliro wao: 10:1-4
  - B. Malangizo apaulendo 10:5-42
    - 1. Koti apite: 10:5-6
    - 2. Utumiki: 10:7-8
    - 3. Zoyenera kuphunzitsa: 10:9-15
    - 4. Malangizo auzimu: 10:16-42

- VII. Maonedwe azinthu mu Ufumu wa Mulungu: 11:1-30
  - A. Kusamvetsetsa Ufumu wa Mulungu: 11:1-11
  - B. Chisokonekero mu Ufumu wa Mulungu: 11:12-19
  - C. Ufumu ukanidwa: 11:20-24
  - D. Ufumu ulandiridwa: 11:25-30
  
- VIII. Mpungwepungwe ndi Afalisi: 12:1-14
  - A. Kukolora pa tsiku lasabata: 12:1-8
  - B. Kuchilitsa pa tsiku lasabata: 12:9-13
  - C. Zotsatira zake: 12:14-21
- IX. Tchimo losakhululukidwa: 12:22-37
- X. Yesu awayankha Afarisi: 12:38-45
- XI. Kutsogoza zinthu zauzimu osati ma ubale akuthupi mu Ufumu wa Mulungu: 12:46-50
- XII. Mafanizo a Ufumu wa Mulungu: 13:1-53
  - A. Fanizo la Ofesa mbeu: 13:1-9
  - B. Chifukwa chimene Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo: 13:10-17
  - C. Kumasulira fanizo la ofesa mbeu: 13:18-23
  - D. Fanizo la tirigu ndi nansongore: 13:24-30
  - E. Fanizo la mbeu yampiru: 13:31-32
  - F. Fanizo la mkate wachotupitsa: 13:33
  - G. Kufotokozera mafanizo mwachidule: 13:34-35
  - H. Kumasulira tanthauzo la fanizo la tiligu ndi nansongore: 13:36-43
  - I. Fanizo la chuma chobisika m'munda: 13:44
  - J. Fanizo la ngale: 13:45-46
  - K. Fanizo la khoka loponyedwa munyanja: 13:47-50
  - L. Mau omaliza amafanizo: 13:51-52
- XIII. Kulandiridwa kwa Mfumu m'mudzi wakwawo: 13:53-58

**Gawo lachinayi: Utumiki wa Yesu ku madera aku Galileya 14:1-18:35**

- I. Imfa ya Yohane M'batizi 14:1-12
- II. Yesu awachokera anthu kupita malo achipululu: 14:13-15:20
  - A. Kudyetsa anthu zikwi zisanu: 14:13-21
  - B. Anthu otsata Yesu chifukwa cha chakudya: 14:22-23
  - C. Yesu ayenda panyanja: 14:24-33
  - D. Utumiki ku Genesarete: 14:34-36
  - E. Mphungwepungwe ndi Afalisi ndi Alembi: 15:1-20
  
- III. Yesu apatukira kumbali ya Turo ndi Sido: 15:21-28

- A. Azimayi aku Turo ndi Sido: 15:21-28
- IV. Yesu kufupi ndi Nyanja ya Galileya: 15:29-38
  - A. Machiritso pafupi ndi Nyanja ya Galileya: 15:29-31
  - B. Adyetsa anthu 4,000: 15:32-38
- V. Utumuki ku Magadana: 15:39-16:4
- VI. Awachenjeza ophunzira kuti asamale ndi Afarisi ndi Asaduki: 16:5-12
  - A. Afuna chizindikilo: 16:1-4
  - B. Awachenjeza kuti asamale ndi chiphunzitso chao: 16:5-12
- VII. Apita ku Kaisareya wa Filipi: 16:13-17:21
  - A. Awayensa ophunzira ake: 16:13-20
  - B. Ayakhula za imfa Yake, Chiukitso ndikubweranso kachiwiri: 16:21-28
  - C. Mawalitsidwe a Yesu: 17:1-13
  - D. Achiritsa wakhunyu: 17:14-20
- VIII. Apita ku Galileya: 17:22-18:35
  - A. Awakumbutsa za imfa yake ndi Chiukitso
  - B. Kupereka msonkho: 17:24-27
  - C. Wamkulu ndi ndani mu Ufumu: 18:1-6
  - D. Chenjezo la wamangawa: 18:7-9
  - E. Fanizo la nkhosa yotaika: 18:10-14
  - F. Kuweruza milandu pakati pa mzika za Ufumu wa Mulungu: 18:15-35
    - 1. Kaweruzidwe ka milandu: 18:15-17
    - 2. Udindo ndi cholowa cha mzika za Ufumu wa Mulungu: 18:18-20
    - 3. Kukhulukirana wina ndi mzake: 18:21-22
    - 4. Mfumu ndi angongore ake: 18:23-35

**Gawo 6: Utumiki wa Mfumu ku Pereya 19:1-20:34**

- I. Chikhamu chichiritsidwa: 19:1-2
- II. Funso lokhudza chilekano: 19:3-12
- III. Yesu Khristu adalitsa ana: 19:13-15
- IV. Yesu acheza ndi mwini chuma: 19:16-22
- V. Kuipa kokhala ndi chuma: 19:23-30
- VI. Fanizo la anthu olembedwa ntchito: 20:1-16
- VII. Kuyandikira kwa imfa ndi Chiukitso cha Yesu Khristu: 20:17-19

- VIII. Pempho lodzikonda la mayi a Zebedayo: 20:20-28
- IX. Akhungu awiri achiritsidwa pafupi ndi Yeriko: 20:29-34

**Gawo 7: Sabata yomaliza la Mfumu Yesu 21:1-27:3.**

- I. Kulandilidwa ngati Mfumu ku Yerusalemu: 21:1-11
  - II. Yesu ayeretsa kachisi: 21:12-17
  - III. Mkuyu utembeledwa: 21:18-22
  - IV. Ulamuliro wa Yesu Ufunsidwa: 21:23-32
  - V. Fanizo la olima munda wamphesa: 21:33-46
  - VI. Fanizo la ukwati: 22:1-14
  - VII. Afuna kumunyoza Yesu: 22:15-45
- A. Fuso lokhudza kupereka msonkho kwa Kayisala: 22:15-22
  - B. Funso lokhudza chiwukitso: 22:23-33
  - C. Funso lokhudza lamulo lalikulu: 22:34-40
  - D. Mafunso amene Yesu anafunsa: 22:41-46

**VIII. Zokambitsana zokhudza alembi ndi Afarisi: 23:1-39**

- A. Amakhala ngati ali ndi ulamuliro pachipembedzo: 23:1-3
- B. Amaika goli pa anthu ena: 23:4
- C. Iwo amakonda kuyamikilidwa koma samaonetsera: 23:5-7
- D. Uphungu kwa ophunzira ake: 23:8-12
- E. Tsoka kwa Alembi ndi Afarisi: 23:13-36
- F. Yesu alilira Yerusalemu: 23:37-39

**IX. Tsogolo la Ufumu wa Mulungu: 24:1-25:46**

- A. Kuwonongedwa kwa kachisi: 24:1-2
- B. Zindikiro za chimaliziro: 24:3-14
- C. Mazuzo anthawi imeneyo: 24:15-22
- D. Zizindikiro zakubweranso kwa Yesu khristu: 24:23-31
- E. Fanizo la mtengo wa mkuyu: 24:32-35
- F. Tsiku la Ambuye: 24:36-41
- G. Awalamula kuti ayang'anire: 24:42-51
- H. Fanizo lokhudza chimaliziro chanthawi: 25:1-46

- 1. Anamwali khumi: 25:1-13
- 2. Fanizo la matalente: 25:14-30
- 3. Mbuzi ndi nkhosa: 25:31-46

**X. Zinthu zochitika Yesu asanapachikidwe: 26:1-27:31**

- A. Akulu Ayuda apangana kuti angwire Yesu: 26:1-2
- B. Upo loti amuphe Yesu Khristu: 26:3-5
- C. Adzodzwedwa mafuta Yesu: 26:6-13
- D. Yudasi alola kumpereka Yesu: 26:14-16
- E. Mgonero omaliza wa Ambuye: 26:17-29
  - 1. Kukonzekera pasaka: 26:17-19
  - 2. M'gonero omaliza 26:20-29
  - 3. Chenjezo kwa Petro: 26:30-35
- F. Gestemane: 26:36-46
- G. Yesu aperekedwa: 26:47-56
- H. Yesu atengeredwa kubwaro la Ayuda: 26:57-27:26

**Gawo 8: Imfa ya mfumu ndi chigonjetso 27:27-28:20**

- I. Kupachikidwa kwa Yesu Khristu 27:27-66
  - A. Yesu anyozedwa ndi asirikali 27:27-31
  - B. Yesu atengedwa kukapachikidwa: 27:32-54
  - C. Azimayi okhulupirira apita kumanda: 27:55-66
- II. Chiukotso cha Yesu Khristu: 28:1-15
- III. Kutuma kwakulu: 28:16-20

## CHAPUTALA 5

### KUTHAMANGITSIDWA MU UFUMU

#### ZOLINGA

Pamapeto pachutala ichi muyenera kukwanilitsa izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kupeza ma vesi okamba zinthu zolepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu.
- Kufotokoza tanthauzo la machimo olepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu.
- Kupeza ma vesi ofotokoza njira zothana ndi machimo olepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu.

#### VESI YOTSOGOLERA

**Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. (Mateyu 7:21)**

#### MAU OYAMBA

Mu chaputala chathachi, tinaona zifunguro zolowera Ufumu wa Mulungu. Koma mu chaputala ichi, tiona zinthu zimene zimalepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu komanso mfundo yoopsa yoti anthu ena adzathamangitsidwa mu Ufumu wa Mulungu.

#### KUTHAMINGITSIDWA MU UFUMU

Pali anthu ambiri amene amanena kuti iwo ali mu ufumu wa Mulungu koma chonsecho iwo si mzika za Ufumu wa Mulungu. Baibulo limafotokoza kuti ufumu wa Mulungu udzatsala ndi mbeu yabwino yokha ndipo nansongore yense adzaponyedwa kunja.

**Ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo; ndipo m'dani amene anamfesa uwu ndiye mdierekezi: ndi kututa ndico cimariziro ca nthawi ya pansi pano; ndi otutawo ndiwo angelo. Ndipo monga namsongole asonkhanitsidwa pamodzi, natenthedwa pamoto, matero mudzakhala m'cimariziro ca nthawi ya pansi pano. Mwana wa munthu adzatumanga angelo ace, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi, ndi kucotsa mu Ufumu wace zokhumudwitsa zonse, ndi anthu akucita kusayeruzika, ndipo adzawataya iwo m'ng'anjo yamoto; kumeneko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano. Pomwepo olungamawo adzawalitsa monga dzuwa, mu Ufumu wa Atate wao. Amene ali ndi makutu amve. (Mateyu 13:38-43)**

Pakadali pano pali anthu ena amene amati ndi mzika za Ufumu wa Mulungu komabe ndi kumakhala mu uchimo. Koma nthawi ikudza imene Mulungu adzalekanitsa mzika zenizeni za Ufumu wa Mulungu ndipo ena adzathamangitsidwa mu Ufumu wa Mulungu.

Baibulo limafanizira Ufumu wa Mulungu ngati ukonde waukulu umene umakola nsomba zosiyanasiyana:

**Ndiponso, Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi khoka loponyedwa m'nyanja, ndi 1 kusunghanitsa pamodzi za mitundu yonse; limene podzala, analibvuulira pamtunda; ndipo m'mene anakhala pansa, anazisonkhanitsa zabwino m'zotengera, koma zoipa anazitaya kuthengo. Padzatero pa cimariziro ca nthawi ya pansa pano: angelo adzaturuka, 2 nadzawasankhula oipa pakati pa abwino, nadzawataya m'ng'anjo yamoto; komweko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano. (Mateyu 13:47-50)**

Baibulo limafotokoza zimene zidzachitike tsiku lina:

**... ambiri a kum'mawa ndi a kumadzulo adzafika, nadzakhala pamodzi ndi Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo, mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 8:11)**

Ndipo Yesu akunjezeranso kuti:

**Kudzakhala komweko kulira ndi kukukuta mano, pamene mudzaona Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo, ndi aneneri onse, mu. Ufumu wa Mulungu, koma inu nokha muturutsidwa kunja. (Luka 13:28)**

Ufumu wa Mulungu usanakhazikitsidwe, Mulungu adzaweruza anthu onse, amoyo ndi akufa:

**Ndikucitira umboni pamaso pa Mulungu ndi Kristu Yesu, amene adzaweruza amoyo ndi akufa, ndi pa maonekedwe ace ndi ufumu wace; (2 Timoteo 4:1)**

Panthawi ya Chiweruzo chomaliza padzakhala kulekanitsidwa kwa anthu onse. Ena adzalowa mu Ufumu koma ena adzatulutsidwa mu Ufumu wa Mulungu:

**Koma pamene Mwana wa munthu adzadza mu ulemerero wace, ndi angelo onse pamodzi naye, pomwepo Iye adzakhala pa cimando ca kuwala kwace: ndipo adzasonkhanidwa pamaso pace anthu a mitundu yonse; ndipo Iye adzalekanitsa iwo wina ndi mnzace, monga mbusa alekanitsa nkhosa ndi mbuzi; nadzakhallitsa nkhosa ku dzanja lace lamanja, koma mbuzi kulamanzere. Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani**



**mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi.  
(Mateyu 25:31-34)**

### **KUPEZA UNZIKA WAMUYAYA**

Chifukwa chakuti Baibulo limafotokoza kuti anthu ena adzatulutsidwa mu Ufumu wa Mulungu, ndi zofunika kudziwa m'mene tingapezere umzika wamuyaya mu Ufumu wa Mulungu. Yesu anati:

**Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba.  
(Mateyu 7:21)**

Kuvomeleza Yesu Khristu ngati mbuye sizokwana kuti munthu akhale mzika ya ufumu wa Mulungu. Yesu Khristu anayakhula kuti kungovomeleza pakamwa sizokwana ayi. Choyenera kuchita ndi kuchita chifuniro cha Mulungu komanso kulapa machimo anu pakulandira Yesu Khristu ngati Mbuye ndi mpulumutsi.

**Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa.  
(2 Petro 3:9)**

Pamene mwavomeleza Yesu Khristu ngati mbuye ndi mpulumutsi, muyenera kupitilira kuchitabe chifuniro chake. Muyenera kukhala molingana ndi mfundo za Ufumu wa Mulungu umene mwalowau. Mfundo zimenezi zifotokozeredwa patsogolo pa chaputala ichi.

Kukhala mzika ya Ufumu wa Mulungu sikungovomereza kokha ndi pakamwa. Zimafuna kusintha kwa maganizidwe ndi Machitidwe a zinthu. Muyenera kuyamba kuchita zinthu mwatsopano komanso malingana ndi Ufumu wa Mulungu.

Yesu Khristu akutsindika Kufunika kochita chifuniro cha Mulungu mu nkhani imene ikupezeka pa Mateyu 21:28-32. Werengani nkhani imeneyi mu Baibulo ndipo mupeza kuti nkhanayi ikuonetsera kuti kungovomeleza kokha Uthenga Wabwino sikokwanira ayi. Tikuyenera kuchitapo kanthu.

### **MACHIMO OLEPHERETSA KULOWA UFUMU WA MULUNGU.**

Tchimo ndi kumphwanya chilamulo cha Mulungu ndipo limalepheretsa munthu kulowa Ufumu wa Mulungu

**Yense wakucita cimo acitanso kusayeruzika; ndipo cimo ndilo kusayeruzika.  
(1 Yohane 3:4)**

Pali machimo ambiri amene amatchulidwa mu Chipangano Chatsopano. Phunziro lotchedwa *Maziko Achikhulupiriro* limapereka m'dandanda wa machimo amenewa.

Pali ndime ziwiri zodziwikiratu zimene zimatchula machimo olepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu:

**Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu?  
Musasoceretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa Ufumu wa Mulungu.  
(1 Akorinto 6:9-10)**

**Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (Agalatiya 5:19-21)**

Machimo ena atchulidwa mu ndime zonsezi koma pali machimo ena amene sakupezeka mu ndime zimenezi.

**Machimo atchulidwa munsimu akupezeka mu mabuku a Akorinto ndi Agalatiya:**

## **KUSALUNGAMA**

Chinthu chimene chikutchulidwa pa ndime yaku Akorinto ndi chakuti anthu osalungama sadzalandira Ufumu wa Mulungu. Ndipo ku Agalatiya akubwerenzaso kuti osalungama sadzalowa Ufumu wa Mulungu chifukwa ichi ndi chidetso.

Mayiko ambiri ali ndi malumuro oti ngati munthu amwalira, anthu otsala amatha kutenga katundu wa munthu omwalirayo. Munthu otenga katundu wa Malemuyo amatchedwa opeza cholowa kapena chopindura. Inu ngati muli opeza cholowa, ndiye kuti mukupatsidwa kathu ndi munthu wina wake. Koma kuti mulandire katundu kapena chuma cha munthu omwalirayu, muyenera kukwaniritsa zinthu zingapo malingana ndi malamuro a dziko.

Inuyo ndi opeza cholowa cha Ufumu wa Mulungu ndipo izi zinatheka kudzera mu imfa ya Yesu Khristu. Kudzera mu imfa Yafera machimo athu, tinapeza mwayi olowa mu Ufumu wa Mulungu. koma kuti tikhale opeza cholowa oyenera, tiyenera kupeza chikhululukiro chamachimo. Muyenera kukhulupirira Yesu Khristu kuti asithe makhaliidwe anu, maganizidwe, machitidwe a zinthu zanu ndi kuyamba kukhala moyo wa ngwiro.

Mau akuti kulungama amatanthauza kukhala Woyera komanso okhazikika pa choonadi. Zimatanthauza kuchita molingana ndi mau a Mulungu pa chili chonse chimene timachita.

Sitingakwalitse kukhala olungama chifukwa chakumvera chilamulo. Munthu amalungamitsidwa kudzera mu chikhulupiriro mwa Khristu Yesu. Munthu amene wakhulupirira Yesu Khristu amakhala olungama wake wa Mulungu ndipo iye amakhala chimene Mulungu amafuna kuti munthu akhale.

**Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa iye. (2 Akorinto 5:21)**

Alembi, Afarisi ndi atsogoleri ana achipembedzo anthawi ya Yesu Khristu amayesa kukhala olungama pakutsata malamulo. Koma Yesu anawachenjeza:

**... ngati cilungamo canu sicicuruka coposa ca alembi ndi Afarisi, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:20)**

Munthu wina aliyense amene atsata malamulo ndi zikhalidwe zachipembedzo ndi cholinga chofuna kukhala olungama ali ngati Afarisi ndi Alembi. Zinthu izi zimapereka kulungama kwabodza. Kumeneku ndikungokhala nao maonekedwe achipembedzo osati kusinthika kwa mtima. Ndipo ngati wina aphunzitsa zinthu izi ngati njira yolowera Ufumu wa Mulungu, ndiye kuti munthu ameneyu ndi cholepheretsa kulowa Ufumu Mulungu.

Mau akuti kusalungama ndi chidetso amayendera limodzi. Ngakhale kuti Agalitiya ndi Akorinto sakutchula machimo onse, koma mau awiri amenewa amafotokozera ntchimo lina lilironse. Munthu wina aliyense amene amakhala moyo osalungama chifukwa cha tchimo sakalowa Ufumu Wa Mulungu. Ndime yaku Akorinto ikugwiritsa ntchito mau oti “musanyengeke.” Kukhulupirira kuti Mukhoza kukhala m'mene mungafunire ndikukulowa Ufumu wa Mulungu ndikudzinyenga chabe.

## **ADAMA**

Dama ndi kugonana pakati pa anthu awiri amene sanakwatirane. Chigololo ndi mbali imodzi ya dama. Chigololo ndi kugonana ndi munthu amene simkazi kapena mamuna wako. Pamene dama limakudzanso kugonana pakati pa amayi okhaokha kapena azibambo.

## **MAFANO:**

Mafano ndikupembedza milungu ina. Izi sizingotanthauza kupembedza zinthu zosemedwa zokha ayi. Koma mafano ndi chinthu china chilichonse chimene chimatengegwa chofunika kuposa Mulungu.

Anthu amafano ndi amene amapembedza zinthu zina osati Mulungu weniweni. Kusazindindikira malo ake a Mulungu pa moyo wathu kukhoza kukhala mafano.

**OLEDZERA:**

kudzera ndi pamene thupi lathu kapena maganizidwe anthu amasokonekera chifukwa chakumwa mowa .

Machimo ali munsimu ndi amene atchuludwa ndime yaku Agalatiya:

**AKUDZIIPSYA NDI AMUNA:**

Izi ndi kuchita zinthu zonyasa zachiwerewere, kapena kuti machimo akugonana akuthupi pakati pa amuna okhaokha.

**OLANDA**

Awa ndi anthu amene amatengelapo mwayi anthu ena. Mwachitsanzo anthu amenewa amatha kugona ndi anthu ena. Pamene achita izi, amakhala kuti akuchimwira thupi lao lomwe.

**AKUBA:**

Awa ndi anthu amene amaba. Ametenga zinthu zimene sizawo popanda chilolezo. Ndipo anthu oterewa amtchedwa ambanda.

**OSILIRA:**

Kusilira ndikukhumbitsitsa chinthu chimene ndi cha munthu wina chitakhala chako osati amene ali nachoyo. Munthu akhoza kusilira katundu, chuma kapena udindo wa ena.

**OLANDA:**

Kulanda ndi kutenga katundu amene si wako pogwiritsa ntchito mphamvu. Kapena kukakamiza munthu kuti akupatse kanthu.

**OLALATIRA:**

Awa ndi anthu amene amayankhula zinthu zonyasa kapena kuyankhulira anthu ena zoipa.

Machimo ali munsimu akupezeka ku ndime yaku Agalatiya:

**KUKHUMBA ZONYASA:**

Ili ndi tchimo lokhumba kuchita zinthu zoipa komanso zochititsa manyazi.

### **NYANGA**

Nyanga ndi mtchitidwe wa ufiti kapena kuti wamatsenga. Ufiti ukhoza kukhalanso zinthu monga kupepetula, kupembedza satana kapena kugwiritsa ntchito zinthumwa.

### **MADANO:**

Mau akuti madano ndi otsutsana mumanthauzo ndi mau oti chikondi. Madano ndi kudana ndi munthu kapena kuti kusakonda anthu.

### **MPATUKO:**

Mipatuko ndi kusagwirizana pakati pa anthu kapena kuti kulimbana pakati pa anthu.

### **NJIRU:**

Njiru ndi chimodzimodzi ndi nsanje kapena ndi mtchitidwe ofuna kufanana ndi anthu ena.

### **ZOPSA MTIMA:**

Kupsa mtima ndi kukhala ndi mkwiyo.

### **NDEU:**

Ndeu ndikumenyana kapena kukanga kapena kusagwirizana.

### **ZIPHUNZITSO ZONYENGA:**

Chiphunzitso chonyenga ndi chikhulupiriro chili chonse chosemphana ndi mau a Mulungu. Nthawi zambiri awa amakhala maganizo a munthu.

## **KUKANIZIDWA KULOWA**

Kupatula machimo atchulidwawa, pali zinthu zina zimene Baibulo limafotokoza kuti ndizolepheletsa kulowa Ufumu wa Mulungu.

### **MWAZI NDI THUPI:**

Paulo anchenjeza kuti:

**Koma ndinena ici, abale, kuti 16 thupi ndi mwazi sizingathe kulowa Ufumu wa Mulungu; kapena cibvundi sicilowa cisabvundi. 1 Akorinto 15:50**

Izi zikugwirizana ndi zifungulo za Ufumu wa Mulungu zimene takamba kale. Ufumu wa Mulungu ndi wauzimu, kotere kuti munthu sangalowe ndi mwazi ndi thupi. Chifukwa cha ichi, munthu ayenera kubadwanso mwatsopano kuti alowe Ufumu wa Mulungu.

**Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu.**

**Yesu anayankha, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3-5)**

**Pakuti kotero kudzaonjeredwa kwa inu kolemerera khomo lakulowa ufumu wosatha wa Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Kristu. (2 Petro 1:11)**

**OPANDA CHIKHULUPIRO NGATI CHA MWANA:**

Yesu anati:

**Indetu ndinena kwa inu, Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 18:3)**

**Ndithu ndinena ndi inu, Munthu ali yense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana, sadzalowamo konse. (Marko 10:15)**

Mkofunika kukhala ngati ka mwana kuti tikalowe Ufumu wa Mulungu. koma izi sizikutanthauza kuti muyenera kusanduka kamwana mmaganizidwe anu kapena thupi lanu. Izi zimatanthauza kuti Inuyo muyenera kukhala ndi chikhulupiro ngati chamwana kutu mukalowe Ufumu wa Mulungu.

**CHUMA:**

Mu utumiki wa Yesu, Iye anakumana ndi wachuma wina amene anafuna kutsata iye. Munthu ameneyu anali olungama koma Yesu ananena kwa Iye nati:

**Undicha Ine wabwino bwanji? palibe wabwino, koma mmodzi, ndiye Mulungu. Udziwa malamulo. Usacite cigololo, Usaphe, Usabe, Usacite umboni wonama,**

**Lemekeza atate wako ndi amako. Koma anati, Izi zonse ndazisunga kuyambira ubwana wanga. Koma m'mene Yesu anamva, anati kwa iye, Usowa cinthu cimodzi: gulitsa ziri zonse uli nazo, nugawire osauka; ndipo udzakhala naco cuma ceni ceni m'Mwamba; ndipo ukadze kuno, unditsate Ine. Koma pakumva izi anagwidwa naco cisoni cambiri; pakuti anali mwini cuma cambiri. (Luka 18:18-23)**

Munthu wachumayu anakanika kutsata Yesu chifukwa chuma chake chinali chofunika kuposa Yesu Khristu.

**Ndipo Yesu pomuona iye anati, Ha! mkovuta nanga kwa anthu eni cuma kulowa Ufumu wa Mulungu! (Luka 18:24)**

**Ndipo Yesu anaunguzaunguza, nanena ndi ophunzira ace, Okhala naco cuma adzalowa mu Ufumu wa Mulungu ndi kubvutika nanga! Ndipo ophunzirawo anazizwa ndithu ndi mau ace. Koma Yesu anayankhanso nanena nao, Ananu, nkobvuta ndithu kwa iwo akutama cuma kulowa mu Ufumu wa Mulungu! Nkwa pafupi kuti ngamila ipyole diso la singano koposa kuti mwini cuma alowe mu Ufumu wa Mulungu. (Maliko 10:23-25)**

kodi Yesu amatanthauza kuti chuma chimalepheretsa anthu kulowa Ufumu wa Mulungu? Ndi chikondi pa chuma chimene chimalepheretsa anthu kulowa Ufumu wa Mulungu osati chuma.

**Pakuti muzu wa zoipa zonse ndiwo cikondi ca pa ndalama; cimene ena pocikhumba, anasocera, nataya cikhulupiriro, nadzipyoza ndi zowawa zambiri. (1 Timoteo 6:10)**

Pamene chuma chikhala chofunika kuposa kutsata Yesu, izi zimalapheleretsa munthu kulowa Ufumu wa Mulungu.

### **KUTHANA NDI VUTO LIMENERI**

Ngati inu muli ndi vuto limeneri, yankho lake ndi kulapa mwa Yesu Khristu: Paulo anati:

**Ndipo ena ainu munali otere; koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa, koma munayesedwa olungama, m'dzina la Ambuye Yesu Kristu, ndi mwa Mzimu wa Mulungu wathu. (1 Akorinto 6:11)**

Posatengera zimene mwakhala mukuchita mbuyomo kapena zimene mukuchita pakadali pano, Inuyo Mukhoza kukhulukidwa.

**Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti**

**atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse.  
(Yohane 1:8-9)**

Pamene mwayeletsedwa, mumakhululukidwa machimo ena ali onse amene amalepheretsa anthu kulowa Ufumu wa Mulungu.

### **KUNGOCHIDULA**

Yesu anaphunzitsa kuti ngati phazi kapena mwendo wako ukupangitsa kuti uchimwe ndi bwino kungozidula kapena ngati maso akukuchimwitsa, ndibwino kungowachotsa.

**Ndipo ngati diso lako likulakwitsa ulikolowole; kulowa iwe m'Ufumu wa Mulungu ndi diso limodzi kuli kwabwino koposa ndi kukhala ndi maso awiri ndi kuonyedwa m'gehena; (Maliko 9:47)**

Chimene Yesu amanthauza ndi chakuti chirichonse chimene chikupangitsa kuti munthu achimwe chiyenera kuchotsedwa mmoyo wanu. Posatengera kuti chinthucho ndi chofunika, koma chiyenera kuchotsedwa ndithu. Iye anagwiritsa ntchito chitsanzo cha diso, mkono ndi dzanja zimene ziri zinthu zofunika kuthupi. Koma Yesu akuti ngati zinthu zimenezi zikuchimwitsa, ndibwino kungozidula koposa kuti zikulepheretse kulowa Ufumu wa Mulungu.

Palibe chinthu china chilichonse kaya ndi chuma kapena zokondweretsa thupi zimene ziyenera kutilepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu.



## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsolera

---

---

2. Lembani ma vesi awiri amene amatchula machimo olepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu.

\_\_\_\_\_ ndi \_\_\_\_\_

3. Werengani chiganizo chili munsimu ndipo ngati chiganizochi chili cholondora lembani T pampata umene waperekedwa. Ndipo ngati chili chosalondora lembani F pampata uli kutsogoro kwa chiganizocho.

- \_\_\_\_\_ ngati muli ndi chuma simungathe kulowa Ufumu wa Mulungu.
- \_\_\_\_\_ Mwazi ndi thupi sizingathe kulowa Ufumu wa Mulungu
- \_\_\_\_\_ Yesu anaonetsa kuti tiyenera kuchotsa chirichonse cholepheretsa kulowa mu Ufumu wa Mulungu.
- \_\_\_\_\_ Yesu anena kuti tiyenera kukhala ngati kamwana kuti tilowe Ufumu wa Mulungu.
- \_\_\_\_\_ Muyenera kulandira Yesu ngati Mbuye ndi mpulumutsi kuti mulowe mu Ufumu wa Mulungu.
- \_\_\_\_\_ Chofunika ndi kungonena kuti Yesu ndi Ambuye kuti mukalowe Ufumu wa Mulungu.

4. Perekani ma vesi amene amafotokozero m'mene mungachotsere machimo olepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu.

---

---

5. Werengani m'ndanda wamachimo olepheretsa kulowa Ufumu wa Mulungu mu gawo loyamba kenako Werengani tanthauzo lake mu gawo lachiwiri. Ndipo lembani namabala kutsogolo kwa tchimo limene latchulidwa mu gawo 1 ndipo nambalayi ikhale yogwirizana ndi tanthauzo latchimo limene laperekedwa mu gawo lachiwiri.

## Gawo loyamba

- \_2\_a. Osalungama
- \_\_\_b. Dama
- \_\_\_c. Mafano
- \_\_\_d. Chigololo
- \_\_\_e. Oledzera
- \_\_\_f. Zonyasa
- \_\_\_g. Chodetsa chokhumba chonyasa
- \_\_\_h. Akuba
- \_\_\_i. Kusilira
- \_\_\_j. Olanda
- \_\_\_k. Zotetana
- \_\_\_l. Chikhumbitso chonyasa
- \_\_\_m. Nyanga
- \_\_\_n. madano
- \_\_\_o. magawano/mipatuko
- \_\_\_p. Kutsanzira
- \_\_\_q. Mkwiyoy
- \_\_\_r. Ndeu
- \_\_\_s. Magawano/mpungwepungwe
- \_\_\_t. Chiphunzitso chonyenga
- \_\_\_u. kaduka/nsanje
- \_\_\_v. akupha
- \_\_\_w. Chisawawa

## Gawo lachiwiri

1. kukhala mwachikunja, khalidwe lachipolowe.
2. Tchimo lina lilironse.
3. nsanje ndi kuchita bwino kwa anthu ena.
4. Kuchotsa moyo wa munthu wina.
5. Kugonana pakati pa anthu osakwatira
6. Osokonekera ndi chakumwa chaukali.
7. Anthu akuba.
8. kulankhula monyoza anthu ena mosayenera.
9. Kupembedza mafano.
10. mzimbo ochita mchitidwe onyasa ogonana.
11. Kugonana ndi munthu amene simkazi wako.
12. Chodetsa Chokhumbitsa chonyasa.
13. kusilira chinthu chamwini.
14. kulanda zinthu mokakamiza.
15. Maimvaimva auchimo, kuchita zonyasa.
16. Mkwiyoy.
17. Zikhulupiliro zosemphana ndi mau a Mulungu.
18. madano.
19. Kusagwirizana kapena kusamvetsetsana
20. Kufunitisa zonyasa.
21. makangano, ndeuy.
22. kubweretsa mpungwepungwe.
23. Mtchitidwe wa ufiti.

## ZOONJERA POPHNZIRA

Werengani ma vesi okamba za Ufumu wa Mulungu mu Buku la maliko ndipo fokotokozani mwachidule mfundo zimene zikuphunzitsa m'mavesi amenewa

Maliko:

1:14-15

---

3:24

---

4:11,26,30

---

9:1,47

---

10:14-15, 23-25

---

11:9-10

---

13:8

---

14:25

---

15:43

## CHAPUTALA 6

### CHIFANIZIRO NDI MFUNDO ZA UFUMU WA MULUNGU

#### ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la maut oti “Chifaniziro”
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “mfundo”
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “chifaniziro cha Baibulo”
- Fotokozerani tanthauzo la mau oti Mfundo za Baibulo”
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “Chifaniziro ndi mfundo za Ufumu”

#### VESI YOTSOGOLERA

**Conseci, anati Davide, anandidziwitsa ndi kucilemba kucokera kwa dzanja la Yehova; ndizo nchito zonse za cifaniziro ici. (1 Mbiri 28:19)**

#### MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi, mwaphunzira zokhudza zifunguro zolowera Ufumu wa Mulungu. Pamene mwapeza umzika mu Ufumu wa Mulungu, Muyenera kudziwa dongosolo la kachitidwe kazinthu komanso mfundo za kakhalidwe mu Ufumu wa Mulungu. Izi ndi chimodzimodzi kuphunzira Chikhalidwe katsopano mu dziko lachilendo limene mwangosamukira kumene.

Baibulo ndi zolembedwa zimene zimafotokoza chifaniziro ndi mfundo zimene zimatsatidwa mu Ufumu wa Mulungu. Tisanaphunzire mfundo zimenezi, tiyenera kudziwa kufunika kwa mfundo zimenezi.

#### MFUNDO NDI CHIFANIZIRO

Chifaniziro ndi chitsanzo chimene chimaperekedwa ndi cholinga choti chitsatiridwe. Mwachitsanzo. Kumayiko anzathu aku ulaya, pamene afuna kupanga chovala, amayamba kaye adula chifaniziro chimene chimawonetsera mmene akufunira kaya ndi buluku kapena dilesi kuti idzaonekere. Kuchokera pa chifaniziro chimenechi, madilesi kapena zovala zina zimatha kudulidwa kuchokera chifaniziro choyamba chija. Ndipo zovala zonse zimene zadulidwa kuchokera ku chifaniziro choyamba zimafanana.

Tanthauzo la mfundo likhoza kufotokozedwa ngati choonadi, njira, kapena lamulo limene limathandizira mmene anthu angakhalire. Tikhoza kunenenanso kuti ichi ndi choonadi chimodzi chachikulu chimene chimakhala ndi mfundo zina zing'onozing'ono zimene zimafotokozera choonadi chachikulu. Mwachitsanzo, Malamulo akulu a dziko la America amapereka danga loti munthu akhoza kulankhula zinthu zakukhosi. Mfundo yaying'ono yofotokozera choonadi chachikulu ndi chakuti munthu akhoza Kulemba, kuyankhula mwaufulu komanso kuchita mkumano ovomelezedwa ngati mbali imodzi ya Ufulu olakhula zakukhozi.

### **MFUNDO NDI CHIFANIZIRO CHA BAIBULO**

Chifaniziro cha Baibulo ndi chitsanzo chauzimu chimene Baibulo limapereka kuti ife tikatsanze. Mwachitsanzo, moyo wa Yesu Khristu ndi chitsanzo chabwino choti anthu okhulupirira akatsate.

Mfundo za Baibulo ndi choonadi chimene Baibulo limaphunzitsa ndipo mfundo zimezi zimakhala ndi mfundo zina zing'onozing'ono zimene zimwagwira ntchito m'madera osiyanasiyana. Mwachitsanzo, Yesu Khristu anaphunzitsa mfundo yakuti: "Perekani ndipo kudzapatsidwa kwa inu." Iyi ndi mfundo yaikulu imene mfundo zake zing'onzing'ono zikhoza kukhala kupereka katundu, ndalama ngakhale ubale umene. Koma mukupereka zonsezi, madalitso auzimu amalandilidwa ngati zotsatira.

### **KUFUNUNIKA KWA MFUNDO NDI CHIFANIZIRO.**

Werengani Ezekieli 43:7-12. Ndime imeneyi ikutsindika kufunika kwa mfundo ndi kachitidwe kazinthu. Mulungu anakhazikitsa mfundo komanso kachitidwe kazinthu kapaderdera kamene Isreali amayenera kutsata mu nkhani za uzimu komanso mmene iwo amayenera kupembedzera.

Koma Israeli anakhazikitsa kachitidwe kazinthu kosemphana ndi Mulungu. chifukwa chakuti Israeli anakhazikitsa Chifaniziro chosemphana ndi Mulungu, iwo anakhala ngati adzimangira chikupa kapena khoma limene limalepheretsa kuti m'dalitso wa mphamvu ya Mulungu uwafikire. Izi zimallepheretsanso kuti mapembedzedwe awo akhale oyenera pamaso pa Mulungu.

Mneneri Ezekieli anauza anthu kuti awone mlingo wa Mulungu kapena chifaniziro cha Mulungu ndi kusinkhasinkhanso moyo wao moyenera:

**Wabadwa ndi munthu iwe, onetsa nyumba ya Israyeli kacisiyu, kuti acite manyazi ndi mphulupulu zao; ndipo ayese muyeso wace. (Ezekieli 43:10)**

Pamene anthu akhazikitsa kachitidwe kazinthu molingana ndi mmene akuionera zinthu zinthu iwo eni, amakhala kuti akhazikitsa mlingo wabodza. Iwo amayamba kuphunzitsa zinthu zimene ndi maganizo awo osati chiphunzitsa chimene Baibulo limaphunzitsa.

Yesu anafotokoza za anthu amenewa:

**Koma andilambira Ine kwacabe, Ndi kuphunzitsa maphunzitso, malangizo a anthu. (Mateyu 15:9)**

Ndikofunika kuti mudziwe mfundo ndi Chifaniziro cha Baibulo chifukwa ngati simutero, kupembedza kwanu kukhoza Kukhala kwa chabe.

Pali kachitidwe kazinthu kosiyanasiyana malingana ndi dziko lapansi kamene anthu amagwiritsa ntchito pochita zinthu zawo. Nthawi zina anthu amatenga anthu ena ngati chifaniziro chao cha kachitidwe kazinthu osati mau a Mulungu. Mtumwi Paulo analemba:

**Dziwani tsono, kuti sikadzagwa pansi kanthu ka mau a Yehova, amene Yehova ananena za nyumba ya Ahabu; pakuti Yehova wacita cimene adanena mwa mtumiki wace Eliya. (2 Mafumu 10:10)**

Pamene Mose anapatsidwa chifaniziro chakamangidwe kachihema, Iye anasamalitsa kuti achite molingana ndi ndondomeko zimene zinaperekedwa ndi Mulungu:

**Monga mwa zonse Ine ndirikuonetsa iwe, cifaniziro ca kacisi, ndi cifaniziro ca zipangizo zace zonse, momwemo ucimange. (Eksodo 25:9)**

**Ndipo uyang'anire uzipanga monga mwacifaniziro cao, cimene anakuonetsa m'phirimo. (Eksodo 25:40)**

**amene atumikira cifaniziro ndi mthunzi wa zakumwambazo monga Mose acenjezedwa m'mene anafuna kupanga cihema: pakuti, Cenjera, ati, ucite zonse monga mwa citsanzoco caonetsedwa kwa iwe m'phiri. (Ahebri 8:5)**

Mfumu Davide inasamalitsa potsata chifaniziro chakachitidwe kazinthu malinga ndi Mulungu pamene anali kukonzekera kumanga kachisi:

**Conseci, anati Davide, anandidziwitsa ndi kucilemba kucokera kwa dzanja la Yehova; ndizo nchito zonse za cifaniziro ici. (1 Mbiri 28:19)**

Anthu amanewa anasamalitsa Chifaniziro chakuthupi. Ngati izi zili chonchi ndiye kuti ife tiyenera kusamalitsanso kwambiri potsata mfundo ndi ndondomeko zauzimu zopezeka mu Baibulo.

## **ZITSANZO ZA KACHITIDWE KAZINTHU MU BAIBULO (NDONDOMEKO ZA KACHITIDWE KAZINTHU MU BAIBULO.**

Yesu Khristu ndi chitsanzo chabwino chimene okhulupirira ayenera kutsata:

**Pakuti ndakupatsani inu citsanzo, kuti, monga Ine ndakucitirani inu, inunso mucite. (Yohane 13:15)**

Mbiri ya amayi ndi abambo amene anatsata Mulungu imapezeka mu Baibulo ngati chitsanzo choti ife titsatire:

**Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife. (1Akorinto 10:11)**

Pali zitsanzo za mmene mafuko ena anakhalira ngati chitsanzo choti mafuko ena atsate. Komanso pali makhalidwe ena oipa amene Baibulo limapereka ngati chitsanzio choti tichipewe.

**ndipo pakuisandutsa makala midzi ya Sodoma ndi Gomora anaitsutsa poigwetsa, ataiika citsanzo ca kwa iwo akakhala osapembedza; (2 Petro 2:6)**

Atsogoleri achikhristu ayenera kukhala chitsanzo kwa anthu owatsatira:

**Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; osati monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. (1 Petro 5:2-3)**

Mtumwi Paulo analemba:

**Abale khalani pamodzi akutsanza anga, ndipo yang'anirani iwo akuyenda kotero monga muli ndi ife citsanzo canu. (2 Afilipi 3:17)**

**si cifukwa tiribe ulamuliro, komatu kuti tidzipereke tokha tikhale kwa inu citsanzo canu, kuti mukatitsanze ife. (2 Atesalonika 3:9)**

Naonso okhulupirira ayenera kukhala chitsanzo chabwino kwa anthu ena:

**Munthu asapeputse ubwana wako; komatu khala citsanzo kwa iwo okhulupira, m'mau, m'mayendedwe, m'cikondi, m'cikhulupiriro, m'kuyera mtima. (1 Timoteo 4:12)**

**kotero kuti munayamba kukhala inu citsanzo kwa onse akukhulupira m'Makedoniya ndi m'Akaya. (1 Atesalonika 1:7)**

**m'zonse udzionetsere wekha citsanzo ca nchito zabwino; m'ciphunzitse cako uonetsere cosabvunda, ulemekezeko, (Tito 2:7)**

Kuti mukakhale chitsanzo chabwino kwa anthu ena, muyenera kumvetsetsa komanso kutenga mfundo za Baibulo ngati gawo la moyo wanu.

### **ZITSANZO ZA MFUNDO ZA BAIBULO**

Pa Ahebri 5:12 Paulo akutchula za “mfundo yoyamba ya mau Mulungu. Ndipo pa Ahebri 6:1-3, Paulo akutchula mfundo zimenezi. Chifkwa cha kufunika kwa mfundo zimenezi, Harvestime International Institute ili ndi phunziro lapaderadera lotchedwa *“Maziko a Chikhulupiriro”*

Tikupemphani kuti mupeze buku la phunziro limeneri kuti likuthandizireni kumvetsa phunziroli.

### **CHIFANIZIRO NDI MFUNDO ZA BAIBULO**

Mu chaputala chikubwerachi muphunzira za Chifaniziro ndi mfundo za Baibulo zimene zimatsatidwa mu Ufumu wa Mulungu. Mfundo ndi chifaniziro ichi, zimasiyana ndi mfundo za maufumu a dziko lapansi.

### **MAYESO ODZIYESA NOKHA**

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

---

2. Kodi mau oti “chifaniziro” amanthauza chiani?

---

---

3. Fotokozani tanthauzo la mau oti “Mfundo” malingana ndi phunziro ili.

---

---

4. Kodi mau oti “Chifaniziro cha Baibulo” amanthauza chiani?



- 
- 
5. Kodi mau oti chifanizirondi mfundo za makhalidwe a Ufumu wa Mulungu”  
amatanthauza chiani?
- 
- 

**(Mayanko amafunso amenewa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)**

## ZOPHUZIRO ZOONJEZERA

Mu machuputala akubwerawa mukhala mukuphunzira mfundo za kakhaliidwe kwa mu Ufumu wa Mulungu. Ndipo mfundo zimezi zakhazikika pa malamulo amane Yesu Khristu anapereka. Gwiritsani ntchito m'ndandanda waperekedwau kuti mukaphunzire malamulo amenewa.

### MALAMULO OPEREKEDWA ND MFUMU

#### KULAPA:

- Lapani: Mateyu 4:17; Chibvumbulutso 2:5
- Idzani kwa ine: Mateyu 11:28
- Koma muthange Ufumu wace ndi cilungamo cace: Mateyu 6:33
- Khululukirani ngati wina wakulakwiran kathu: Marko 11:25
- Mudzikanize nokha: Mateyu 16:24
- Pemphani ...funani...gogodani: Mateyu 7:7
- Yesetsani kulowa pa khomo lopapatiza: Luka 13:24
- **ZOKHULUPIRIRA:**
- Khulupirirani Uthenga Wabwino: Maliko 1:15
- Khulupirirani ine khulupirirani Mulungu: Yohane 14:1
- Khulupirirani Mulungu otuma ine: Yohane 6:28-29
- Khulupirirani Ine, kuti Ine ndiri mwa Atate ndi Atate ali mwa Ine: Yohane 14:11
- Khulupirirani ntchito zimene ndichita: Yohane 10:37-38
- Pokhala muli nako kuunika, khulupirirani kuunikako: Yohane 12:36
- Khulupirirani kuti mwalandira: Marko 11:24

#### Kubadwa mwatsopano:

- Muyeneranso kubadwa mwatsopano: Yohane 3:7
- Yamba watsuka mkati kaye: Mateyu 23:26
- Ukakoma mtengo chipatso chake chikomanso: Mateyu 12:33
- Khalani mwa ine ndipo ndidzakhala mwa inu: Yohane 15:4
- Khalani nao mchere mwainu nokha: Maliko 9:50
- Gwirani ntchito chifukwa chakudya chimene chitsalira osati chotayika: Yohane 6:27
- Kondwerani kuti mayina anu alembedwa kumwamba: Luka 10:20
- **KULANDIRA MZIMU OYERA:**
- Landirani Mzimu Woyera: Yohane 20:22
- Ayambe akhuta ana kaye: Marko 7:27
- Ngati Munthu amva ludzu adze kwa ine, amwe: Yohane: 7:37-39
- Sungani malamulo anga: Yohane 14:15-17

- Pemphani...mokokamira: Yohane 16:24; Luka 11:5-13
- Khalani kufikira mamvekedwe amphamvu yakumwamba: Luka 24:49
- Komanso Nkhoswe adzachitira umboni, inunso muchitira umboni: Yohane 15:26-27

## KUTSATA YESU

- Mutsate ine: Yohane 12:26
- Batizidwa: Mateyu 3:13-15; 28:19
- Muzichita izi kuti mundikumbukire ine: Luka 22:17-19
- Inunso musambitsane mapazi wina ndi mzake Yohane 13:14-15
- Ngati wina afuna kutsata ine ...azenze mtanda wake: Luka 9:23
- Phunzirani kwa ine: Mateyu 11:29
- Khalani mchikondi change: Yohane 15:9
- **PEMPHERO:**
- Pempheranai nthwawi zonse: Luka 21:36
- Pemperani mungalowe kuyesedwa: Luka 22:40-46
- Pempherani kuti mwini zinthu akankhe anchito kututa: Luka 10:2
- Pempelerani akuchita inu chipongwe: Luka 6:28
- Pemphero mu dzina la Atate: Mateyu 16:24-26; Yohane 16:24-26
- Chifukwa chake pempherani inu chomwechi: Mateyu 6:9-13
- Pamene mupemphera musabwerezebwereze Mateyu 6:7-8
- **CHIKHULUPIRIRO**
- Khulupirirani Mulungu: Maliko 11:22
- Usakhale osakhulupilira: Yohane 20:27
- Musakhale okaika: Luka 12:29
- musadele nkhwana ndi moyo wanu: Mateyu 6:25-34
- mtima wanu usavutike: Yohane 14:1-27
- Limbani mtima: Mateyu 14:27
- Musaope: Maliko 5:36; Luka 12:4-7
- **KUKHULUPIRIKA KUFIKIRA IMFA:**
- Khalani okhulupirika kufikira imfa: Chivumbulutso 2:10
- Gwiritsitsani chimene muli nacho: Chibvumbulutso 3:11
- kondwerani pamene muzunzidwa: Mateyu 5:11-12; Luka 6:23
- Pamene akuzunzani munzinda wina, pitani mzinda wina: Mateyu 10:23
- Musadere nkhwana kuti mudzayakhula bwanji: Mateyu 10:19
- Musang'ung'udze wina ndi mzake: Yohane 6:41-43
- weramukani, tukulani mitu yanu: Luka 21:28
- **KULALIKA UTHENGA:**
- Kulalika uthenga kwa onse: Mateyu 10:7; Marko 16:15

- Kulalikira kulapa mudzina la Khristu Yesu: Luka 24:46-4
- Batizani mu dzina la Tate, Mwana ndi la Mzimu Woyera: Mateyu 28:19
- Mukawaphunzitse zinthu zonse zimene ndikulumulani: Mateyu 28:20
- chimene ndikuuzani muchiyakhule: Mateyu 10:27; Marko 4:22
- Dyetsa nkhosa zanga: Yohane 21:15-17
- Chiritsani odwala: Mateyu 10:8
- **KUSILIRA:**
- Mudziyang'anire kupewa nsiliro uli onse: Luka 12:15
- Musadzikundikire chuma pa dziko lapansi: Mateyu 6:19-20
- Mupereke zakhumi zanu koma osachita zina zosayenera: Mateyu 23:23
- Mudzipereka kwa iwo akukupemphani: Mateyu 5:42
- koma patsani mpatso zachifundo: Luka 11:41
- pamene mukonza mphwando muitane asauka: Luka 14:12-13
- **CHINYENGO:**
- Chenjerani ndi chotupitsa cha Afarisi: Luka 12:1
- chenjerani ndi Alembi: Luka 20:46-47
- Musaope ntchito zao: Mateyu 23:2-3
- Mwasandutsa nyumba ya Atate wanga yochitira malonda: Yohane 2:16
- Musachite ntchito zachifundo pamaso pa anthu: Mateyu 6:1-4
- Lowa m'chipinda chako nupemphere: Mateyu 6:5-6
- pamene musala chakudya musadzionetsera kwa anthu: Mateyu 6:16-18
- **KUFATSA:**
- Senzani goli langa: Mateyu 11:29
- Musamagwiritsa ntchito mphamvu ngati achikunja: Mateyu 20:25-26
- Koma amene afuna kukhala wankhulu akhale mtumiki: Marko 10:43-44
- Musatchedwe mphunzitsi: Mateyu 23:8
- Khala panso kunthungo: Luka 14:8-11
- Kondwerani osati kuti mizimu ingonjera inu: Luka 10:20
- Nenani "ife ndi akapolo opanda pake": Luka 17:10
- **CHIKONDI CHAPA ABALE:**
- Kondanani wina ndi mzake ngati mmene ndakukonderani ine: Yahane 15:12
- Musanyoze mmodzi mwa wang'ono awa: Mateyu 18:10-14
- Patsanani mtendere wina ndi mzake ...uyanjane ndi m'mbale wako: Mateyu 5:23-24; Marko 9:50
- Uyanjanitsidwe ndi m'mbale wako zolakawa zanu: Mateyu 18:15-17
- Khulukira m'mbale wako kasanu ndi kwawiri patsiku: Mateyu 18:21-22; Luka 17:3-4
- Musaweruze molingana ndi moaonekedwe: Mateyu 7:1-5; Yohane 7:24
- Musawatsutse: Luka 6:37
- **CHIKONDI CHENICHENI:**

- Khalani wagwiro: Mateyu 5:48
- Gulitsa zonse uli nazo ndikupereka zachifundo: Mateyu 19:21; Luka 12:32-33
- Kondani adani anu: Mateyu 5:44; 26:52
- Chitirani zabwino adanani anu: Luka 6:27-28
- Muzibwereketsa osayembekezera kathu: Luka 6:35
- Mkaneni oipayo: Mateyu 5:39-41
- -Mkudekha kwanu, sungani miyoyo yanu: Luka 21:19
- **CHIKONDI PA MULUNGU:**
- Ukonde Mulungu wako ndi mzeru zako zonse, mphamvu zako zonse ndi mtima wako onse: Marko 12:30
- Muzitumikira Mulungu yekha: Mateyu 4:10
- Kupembedza Mulungu Tate mu Mzimu ndi choonadi: Yohane 4:23-24
- Musatchure munthu wina aliyense tate pa dziko lapansi: Mateyu 23:9
- Usamuyese Mbuye Mulungu wako: Mateyu 4:7
- Anthu onse alemekeze Mulungu: Luka 12:5 Yohane 5:22-23
- **Udindo wanu pa Mulungu ndi anthu:**
- Zakaisala zipite kwa kaisara: Marko 12:17
- Musamalumbire: Mateyu 5:34-37; Marko 4:22
- Chimene Mulungu wachimanga Munthu asachileknitise: Mateyu 19:5-6
- Fulumira kuyanjana ndi mzako wa mlandu: Mateyu 5:25
- Musaretse ena kuchotsa ziwanda: Marko 9:38-40
- Idyani zimene mwapatsidwa: Luka 10:38
- Sonkhanitsani zotsara kuti zisatayike: Yohane 6:12
- **UDINDO PA NANSI WAKO:**
- Konda mzako monga udzikondera iwe mwini: Mateyu 19:17-19
- Usaphe: Mateyu 19:18
- Usachite chigoloro: Mateyu 19:18
- Usabe: Mateyu 19:18
- Usachitire Umboni wabodza: Mateyu 19:18
- Lemekeza atate ako ndi amayi ako: Mateyu 19:19
- Mudzichitira ena zimene mufuna akuchitireni: Luka 6:31
- **MZERU:**
- Khalani ochenjera ngati njoka ndi oona mtima ngati nkhunda: Mateyu 10:16
- Chenjerani ndi anthu: Mateyu 10:17
- wakhungu atsogolere wakhungu: Mateyu 15:12-14
- Musamapatsa chotupitsa kwa agalu: Mateyu 7:6
- amene ali ndi thumba la ndalama alitenge: Luka 22:35-36

- Sasani fumbi kumapazi anu ngati sakulandirani: 11 Luka 9:5; 10:10-
- **KUSANTHULA MALEMBA:**
- Musanthula malemba: Yohane 5:39
- Kumbukirani mau amene ndinanena kwa inu: Yohane 15:20
- Lolani mau awa akhazikike m' makutu mwanu: Luka 9:44
- kotero yanganirani ndi mamvedwe: Luka 8:18
- Yang'anirani mamvedwe anu: Marko 4:24
- Chenjerani ndi chotupitsa cha Afalisi Mateyu 16:6-12
- Chenjerani ndi aneneri onyenga: Mateyu 7:15-17
- **LOLANI KUUNIKA KWANU KUWALE:**
- Kuwala kwanu kuonekere: Mateyu 5:16
- Yanganira kuunika kuli mwa iwe kungakhale mdima: Luka 11:35
- Pita nubale chipatso: Yohane 15:16
- Kotere Khalani achifundo: Luka 6:36
- Chitirani umboni zazikulu zimene Mulungu wakuchitirani: Marko 5:19
- Kwezani maso anu ndikuyamg'ana m'minda: Yohane 4:35
- Yendani pokhala nako kuunika: Yohane 12:35
- **KUBWERA KWACHIWIRI KWA YUSU:**
- Chimene mulinacho gwirani: Chibvumbulutso  
2:25; 3:2-3
- khalani okonzeka mwana wa munthu akubwera Luka 12:40
- khalani odzimangilira mchiuno ndipo nyali zanu zikhale zoyaka: Luka 12:35-36
- mudziyang'anire nokho mitima yanu ingalemetsedwe: Luka 21:34
- Kumbukirani mkazi wa loti: Luka 17:31-32
- yang'anirani poti wina angosocheretse inu: Marko 13:5-6; Luka  
21:8
- -Yang'anirani: Marko 13:34-3

## CHAPUTALA 7

### CHIKHALIDWE CHA UFUMU

#### MFUNDO ZA UFUMU WA – GAWO LOYAMBA

#### ZOLINGA

##### **Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:**

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokozerera kufunika kodziwa mfundo za Ufumu wa Mulungu.
- Kuzindikira mfundo zikuluzikulu zoyendetsera Ufumu wa Mulungu.
- Kupeza maziko amene mfundo za ufumu zakhazikika.
- Kutchula malumulo awiri amene mfundo zonse zimakhazikikapo.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Ndipo Ine ndikuikirani ufumu, monganso Atate wanga anandiikira Ine, kuti mukadye ndi kumwa kugome kwanga mu Ufumu wanga; (Luka 22:29)**

#### MAU OYAMBA

Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi kuitanira kwa anthu onse kuti abwerere ku moyo umene Mulungu anakhazikitsa pachiyambi. Koma sikuti pali mlingo wakhalidwe la munthu umene Mulungu anakhazikitsa kuti ngati munthu afikira, pamene ndiye kuti alowa Ufumu wa Mulungu. Kulapa ndiye chinthu chokhacho chimene chimamuyeneleza munthu kuti alowe Ufumu wa Mulungu. Kudzera mukulapa ndikuvomeleza Yesu ngati mpulumutsi, munthu amabadwanso mu Ufumu ndikukhala mzika ya Ufumu wa Mulungu.

Umzika mu Ufumu wa Mulungu umafuna Chikhalidwe chatsopano cholingana ndi malamulo a Ufumuwo. Moyo mu ufumu wauzimu umagwirizana ndi moyo wathu ku dziko lakuthupi ngakhale kuti chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu ndi chosiyana kwambiri ndi Chikhalidwe cha maufumu a dziko lapansi, chifukwa cha ichi, mfundo za maufumu amenewa ndi zosiyana kambiri. Pamene munthu walowa mu Ufumu wa Mulungu zili ngati kusamukira dziko lachilendo ndipo chifukwa cha ichi, munthu ayenera kuphunziranso Chikhalidwe chatsopano.

Ku dziko lakuthupi, Chikhalidwe chikhoza kufotokozeredwa ngati ndondomeko za kachitidwe ka zinthu kamene kamathandiza kuyendetsa zinthu pamene pali anthu. Mu chaputala chimenechi, muphunzira za Chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu. Ndipo chaputala

chamtsogolo, tidzaona choonadi china chokhudza Ufumu wa Mulungu chimene chikuvumbulutsidwa mu mafanizo:

## **KUFUNIKA KWA MFUNDO ZA UFUMU**

Ndikofunikira kuti mudziwe mfundo zoyendetsera moyo mu Ufumu wa Mulungu pa zifukwa izi:

Muyenera kukhala molingana ndi mfundo za Ufumu kuti mukhalebe Mzika ya Ufumu wa Mulungu:

Ngakhale kuti kulapa ndi chinthu chokhacho chomutengera Munthu mu Ufumu wa Mulungu, koma pali chinthu china chokhazikika chomuyeneleza munthu kuti akapitilire kukhalabe mzika ya Ufumu wa Mulungu, Yesu ananena:

**Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. (Mateyu 7:21)**

Chifuniro cha atate chimene chinaonetseredwa ndi Yesu Khristu ndi chimene chimayendetsa moyo wa okhulupirira mu ufumu wa Mulungu.

## **YESU ANAYANKHULA KUTI MFUNDO ZA UFUMU WA MULUNGU NDI ZOFUNIKA:**

Pa Luka 12:22-31 Yesu anaphunzitsa kuti Ufumu wa Mulungu chiyenera kukhala chinthu choyamba cha moyo. Iye anatsiriza ndi mau awa:

**Komatu tafuna-funani Ufumu wace, ndipo izi adzakuonjezerani. (Luka 12:31)**

Pamene muyamba mwafunafuna ufumu wa Mulungu, makamaka mfundo zake, Chikhalidwe chake ndi Uthenga wake, zinthu zonse zamoyo zidzakutsana.

## **ZIPATSO ZA UFUMU WA MULUNGU: UMBONI WA UMZIKA**

Yesu anauza Ayuda umboni wa umzika wa Ufumu wa Mulungu kuti ndi kubala zipatso (Mateyu 21:43) Chipatso cha Ufumu wa Mulungu ndi chimene chimaonekera kunja kuchokera mkati. Izi ndi chimodzimidzi chipatso chamtengo wakuthupi umene zipatso zake zimaonetsera moyo



umene uli mkati mwa mtengowo. Inuyo ngati mzika ya Ufumu wa Mulungu, zipatso zimaonekera m'mene mumakhalira moyo wanu wakuthupi\*.

Kuti mudzalamulire nao mu Ufumu wa mulugu muyenera kudziwa mfundo zake:

Timoteyo wachiwiri amaonetsa kuti okhulupirira adzalamulira ndi Yesu Khristu mu Ufumu wa Mulungu ukudzao. Kulamulira kumatathauza kukhala ndi mphamvu ndi ulamuliro. Kuti mulamulire muyenera kudziwa malamulo amene amayendetsa Ufumu wa Mulungu.

### **MAZIKO A MFUNDO ZA UFUMU WA MULUNGU.**

Maziko ndi msanamira imene pamangingidwapo kathu. Pamene anthu akumanga nyumba, ayenera kuiyika maziko oyenera. Maziko amenewa ndi amene amathandizira kuti nyumba ikhazikike.

Kulungama ndiye maziko a Ufumu wa Mulungu komanso mfundo yoyendetsera Ufumu wa Mulungu:

**Koma ponena za Mwana, ati, Mpando wacifumu wanu, Mulungu, ufikira nthawi za nthawi; Ndipo ndodo yacifumu yoongoka ndiyo ndodo ya ufumu wanu. (Ahebri 1:8)**

Ndodo imene amfumu amanyamula m'manja ndi chizikindikiro cha ulamuliro. Ulamuliro kapena mphamvu ya Ufumu wa Mulungu ndi kulungama. Koma kulungama kumaneku sikumabwera chifukwa chakuyesayesa kwathu kapena chifukwa cha chipembedzo. Yesu anati:

**Pakuti ndinena ndi inu, ngati cilungamo canu sicicuruka coposa ca alembi ndi Afarisi, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:20)**

Alembi ndi Afarisi anali atsogoleri achipembedzo mu nthawi ya Yesu Khristu. Maziko awo auzimu amakhazikika mukuyesa kwao pofuna kukhala olungama. Iwo anali ndi malamulo ndi zikhalidwe zimene amatsata pamoyo wao wa tsiku ndi tsiku.

Kulungama kumene Ufumu wa Mulungu wakhazikika ndi kulungama kwa Mulungu. Baibulo limafotokoza kuti:

---

\* Chili chonse chimene Yesu Khristu anaphunzitsa chimakhudza Uthenga wa Ufumu wa Mulungu. Muphunziro lina la Harvestime International Institute, lotchedwa "*Ukadaulo wa kuphunzitsa*" limagwirizana ndi phunziro ili chifukwa limaphunzitsa zinthu zonse zimene Yesu Khristu anaphunzitsa. Komanso Mukhoza kuphunzira zambiri zimene yesu anaphunzitsa pogwiritsa ntchito Baibulo limene limaonetsa zonse zimene Yesu anaphunzitsa pozilemba ndi Utoto ofira.

**Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)**

Maziko a Ufumu wa Mulungu akhazikika pa anthu olungama amene amakhala moyo olungama.

**Koma ndithu maziko a Mulungu aimika pokhazikika, ndi cukhala naco cizindikilo ici, Ambuye azindikira iwo amene ali ace; ndipo, Adzipatule kwa cosalungama yense wakutchula dzina la Ambuye. (2 Timoteo 2:19)**

Maziko a Ufumu wa Mulungu akuonekera mu chithunzi chili munsimuchi:

Maziko a Ufumu wa Mulungu	
Anthu olungama ----->	Mulungu amadziwa anthu ake
Kukhala moyo olungama --->	Onse otchedwa mudzina la Ambuye Asiye mphulupuru zao ndi Ndikudzipatura

Pali magawo awiri akudzipereka pa nkhani ya kulungama. Ma gawo awiri amenewa akuonekera mu ndime imeneyi;

**Ndipo onani, munthu anadza kwa Iye, nati, Mphunzitsi, cabwino nciti ndicicite, kuti ndikhale nao mayo wosatha? Ndipo Iye anati kwa iye, Undifunsiranji za cinthu cabwino? alipo Mmodzi ndiye wabwino: koma ngati ufuna kulowa m'moyo, sunga malamulo.**

**Mnyamatayo ananena kwa Iye, Zonsezi ndinazisunga, ndisowanso ciani? Yesu ananena naye, Ngati ufuna kukhala wangwiro, pita, kagulitse zomwe uli nazo, nupatse aumphawi, ndipo udzakhaia ndi cuma Kumwamba; ndipo ukadze kuno, unditsate. Koma mnyamatayo m'mene anamva conenaco, anamuka wacisoni; pakuti anali naco cuma cambiri. (Mateyu 19:16-17; 20-22)**

Gawo loyamba la kulungama ndi “kulowa moyo wina.” Uku ndi kulungama kumene kumabwera pamene munthu wabadwanso mwatsopano pakutsukidwa kuchimo ndikuyamba kukhala molingana ndi mau a Mulungu. Mlingo wachiwiri ndi pamene munthu wakhwima mu uzimu. Kuti munthu akhwime muzimu zimalira kudzipatura ku zinthu za dziko lapansi zimene zimaoneka zosililika.

Izi sizikutanthauza kuti tigulitse zinthu zonse zimene tili nazo ndikuzipereka kwa anthu osowa. Yesu anauza munthu uja kuti akaguritse zinthu zake zonse chifukwa chuma chake chinali chofunika kuposa Mulungu. Palibe chinthu chimene chiyenera kukhala chofunikwa kwambiri padziko lapansi kuposa Mfumu Yesu. Kuti tikakule moyo wathu wauzimu, tiyenera kutaya mfundo za dziko lapansi ndi kuyamba kukhala molingana ndi mfundo za Ufumu wa Mulungu.

## **MFUNDO ZIWIRI ZOFUNIKA ZA UFUMU WA MULUNGU:**

Pali mfundo ziwiri za Ufumu wa Mulungu zimene mfundo zonse zakhazikika. Yesu atafunsidwa kuti kodi lamulo lalikulu ndi liti, Iye anayankhat nati:

**... Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba. Ndipo laciwiri lolingana nalo ndili, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini. Pa malamulo awa awiri mpokolowekapo cilamulo conse ndi aneneri. (Mateyu 22:37-40,)**

Maliko anafotokozera za mfundo yomweyi motere:

**Yesu anayankha, kuti, La m'tsogolo ndili, Mvera, Israyeli; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi; ndipo uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse. Laciwiri ndi ili, Uzikonda mnzako monga udzikonda mwini. Palibe lamulo lina lakuposa awa. (Marko 12:29-31)**

Yesu Khristu anafotokozera lamulo lachiwiri motere:

**Ndipo monga mufuna inu kuti anthu adzakucitirani inu, muwacitire iwo motero inu momwe. (Luka 6:31)**

Kungofotokozera mwachidule, mfundo zachiwiri zazikulu za Ufumu wa Mulungu ndi izi:

1. Kukonda Mulungu ndi mtima wako onse, mphamvu zako zonse ndi mzeru zako zonse.
2. Kukonda ndi kuchitira ena zimene ife tikhoza kukonda iwo atatichitira.

Mfundo zonse za Ufumu wa Mulungu zakhazikika pa mfundo zimenezi

## **CHIYAMBI CHA UFUMU WA MULUNGU**

Kuchokera pachiyambi cha Ufumu wa Mulungu, ndi zachidziwikire kuti Ufumu umenewu ndi Osiyana kwambiri ndi Ufumu wa dziko lapansi. Angelo atamuonekera Mariya ndikumuzu iye kuti adzakhala mayi wa Mfumu ikudzayo, iye analemekeza Mulungu. Mau amene iye anagwiritsa ntchito polemekeza Mulungu anali a uneneri chifukwa anaonetsera dongosolo latsopano la Ufumu wa Mulungu.

**Cifukwa iye Wamphamvuyo anandicitira ine zazikuru; Ndipo dzina lace liri loyera. Ndipo cifundo cace cifikira anthu a mibadwo mibadwo Pa iwo amene amuopa iye.**

**Iye anacita zamphamvu ndi mkono wace; Iye anabalalitsa odzitama ndi mlingaliro wa mtima wao, iye anatsitsa mafumu pa mipando yao yacifumu, Ndipo anakweza aumphawi, Anawakhutitsa anjala ndi zinthu zabwino, Ndipo eni cuma anawacotsa opanda kanthu. (Luka 1:49-53)**

Anthu onse amphamvu zao komanso odzikuza anatsitsidwa ndipo onse onyozeka anakwezedwa. Anjala anadyetsedwa ndipo anthu achuma chao anabwezedwa chimanjamanja.

Pamene Yohane M'batizi anavumbulutsa za Ufumu wa Mulungu, dongosolo lomweli linaonetseredwanso:

**Cigwa ciri conse cidzadzazidwa, Ndipo phiri liri lonse ndi mtunda uli wonse zidzacepsedwa; Ndipo zokhota zidzakhala zolungama, Ndipo njira za zigoloondo zidzakhala zosalala; Ndipo anthu onse adzaona cipulumutso ca Mulungu. (Luka 3:5-6)**

Chozizwitsa choyamba chimene Yesu Khristu anachita chinali kusandutsa madzi kukhala vinyo. Izi zinaonetsera kuti mfundo zoyendetsera Ufumu wa Mulungu zidzakhala zosiyana ndi mfundo za maufumu a dziko lapansi.

## **MFUNDO ZIKULUZIKULU: CHIKHALIDWE CHA UFUMU WA MULUNGU.**

Yesu Khristu anakhazikitsa mfundo zikuluzikulu za Ufumu wa Mulungu ndipo imodzi mwa mfundo zimenezi ndi: “koma sizikuyenera kukhala chocho pakati panu”

**Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akulu awo amacita ufumu pa iwo. Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala wankulu mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri. (Mateyu 20:25-28)**

**Koma sipadzatero ndi inu; komatu iye ali wamkuru mwa inu, akhale ngati wamng'ono; ndi iye ali woyamba, akhale ngati wotumikira. (Luka 22:26)**

**Koma mwa inu sikutero ai; kama amene ali yense afuna kukhala wamkuru mwa inu adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. (Maliko10:43-44)**

Ngakhale kuti Yesu Khristu amakamba nkhani yokhudza utsogoleri komanso iye amakhazikitsa mfundo yaikukulu yokhudza Ufumu wa Mulungu. “sizikuyenera kukhala choncho pakati panu.” Imene inaonetsera kuti Mfundo za Ufumu wa Mulungu ndi zosiyana ndi zadziko lapansi.

### **MFUNDO YA UMODZI:**

Pali ma ufumu adziko lapansi ambiri amene ndi ogawanika. Izi zimaonekera mu zinthu ngati kuukira boma. Koma Ufumu wa Mulungu ndi umodzi siogawanika. Ndi thupi limodzi lauzimu lokhala ndi ziwalo zambiri:

**Pakuti monga thupi liri limodzi, nilikhala nazo ziwalo zambiri; koma ziwalo zonse za thupilo, pokhala zambiri, ziri thupi limodzi; momwemonso Kristu. Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse tinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Ahelene, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu mmodzi. Pakutinso thupi silikhala ciwalo cimodzi, koma zambiri. (1 Akorinto 12:12-14)**

Mzika za Ufumu wa Mulungu ndizoyanjanitsidwa kudzera mwa Yesu Khristu ndi Mulungu:

**kuti onse akakhale amodzi, monga Inu Atate mwa Ine, ndi Ine mwa Inu, kuti iwonso akakhale mwa Ife: kuti dziko lapansi likakhulupire kuti Inu munandituma Ine. Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa Iwo; kuti akhale amodzi, monga Ife tiri mmodzi; Ine mwa iwo, ndi Inu mwa Ine, kuti akhale angwirowa mwa mmodzi; kuti dziko lapansi lizindikire kuti Inu munandituma Ine, nimunawakonda iwo, monga momwe munakonda Ine, (Yohane 17:21-23)**

Palibe ubale wina ulionse pakati pa Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa Satana:

**...Ufumu uli wonse wogawanika pa wokha sukhalira kupasuka, ndi mudzi uli wonse kapena banja logawanika pa lokha silidzakhala; ndipo ngati Satana amatulutsa Satana, iye agawanika pa yekha; ndipo udzakhala bwanji ufumu wace? Ndipo ngati Ine ndimaturutsa ziwanda ndi mphamvu yace ya Beelzebule, ana anu amazitulutsa ndi mphamvu ya yani? cifukwa cace iwo adzakhala oweruza anu. Koma ngati Ine ndimatulutsa ziwanda ndi mphamvu yace ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu. (Mateyu 12:25-28 werenganinso Maliko 3:23-26 ndi Luka 11:17-20)**

Chimodzi mwazifukwa za kufunika kwa umodzi mu Ufumu wa Mulungu ndi mphamvu yopanda malire imene imapezeka mu umodzi. Yesu Khristu analonjeza:

**Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati awiri ainu abvomerezana pansu pano cinthu ciri conse akacipempha, Atate wanga wa Kumwamba adzawacitira. Pakuti kumene**

**kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao  
(Mateyu 18:19-20)**

Chifukwa chakuti mzika za Ufumu wa Mulungu zikukhalabe moyo wakuthupi, mikangano imachitika nthawi ndi nthawi. Koma Yesu Khristu wapereka njira zothana ndi kusagwirizana kapena kugawikana kumeneku (Mateyu 18:15-35)

### **MFUNDO YAKUFALIKIRA:**

Ufumu wa Mulungu uyenera kufalikira kudzera njira ziwiri: Ngati mchere ndi Kuunika:

**Inu ndinu mcere wa dziko lapansi; koma mcerewo ngati ukasukuluka, adzaukoleretsa ndi ciani? Pamenepo sungakwanirensa kanthu konse, koma kuti ukaponyedwe kunjira, nuponedwe ndi anthu. Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi. Mudzi wokhazikika pamwamba pa phiri sungathe kubisika. Kapena sayatsa nyali, ndi kuibvundikira m'mbiya, koma aiika iyo pa coikapo cace; ndipo iunikira onse: ali m'nyumbamo. Comweco muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona nchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa Kumwamba (Mateyu 5:13-16)**

**Palibe munthu, atayatsa nyali, aiika m'cipinda capansi, kapena pansa pa muyeso, koma pa coikapo cace, kuti iwo akulowamo aone kuunika. Nyali ya thupi ndiyo diso lako; pamene paliponse diso lako liri langwiro thupi lako lonse liunikidwanso monsemo; koma likakhala loipa, thupi lako lomwe liri la mdima wokha wokha. Potero yang'anira kuunika kuli mwa iwe kungakhale mdima. Pamenepo, ngati thupi lako lonse liunikidwa losakhala nalo dera lace lamdima, lidzakhala lounikidwa monsemo, ngati pamene nyali ndi kuwala kwace ikuunikira iwe. (Luka 11:33-36)**

**Kotero mcere uli wokoma; koma ngati mcere utasukuluka adzaukoleretsa ndi ciani? Suyenera kuuthira pamunda kapena padzala, autaya kunjira. Amene ali nao makutu akumva amve. (Luka 14:34-35)**

**Ndipo ananena ndi iwo, Kodi atenga nyali kuti akaibvundikire mbiya, kapena akaiike pansa pa kama, osati kuti akaiike pa coikapo cace? (Marko 4:21)**

**Mcere uli wabwino; koma ngati mcere unasukuluka, mudzaukoleretsa ndi ciani? Khalani nao mcere mwa inu nokha, ndipo khalani ndi mtendere wina ndi mnzace. (Marko 9:50)**

Ku dziko lakuthupi, mchere umagwira ntchito mosaonekera. Umathandiza kuti chakudya chisaonogeke, kuchiza mabala komanso kukometsa chakudya.



**Masophenya a Ufumu wa Mulungu ndiko kufunafuna Ufumu wa Mulungu. Werengani Mateyu 6:19-34 ndipo mufananize ndimeyi ndi Luka 12: 22-34:**

- Yesu analankhula za mtima umodzi Mateyu 6:19-21.
- Masophenya amodzi Mateyu 6:22-23.
- Kudzipereka kwa thunthu Luka 16:13.
- Kudzipereka potumikira Mateyu 6:24 Luka 9:60 ndi 62.
- Kukhala ndi maganizo amodzi Mateyu 6: 25-32 ndi 34

Vesi ili munsiyi ikufotokozera mfundo yakukhala ndi masomphenya amodzi kapena osachulukidwa pakuchita zinthu.

Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)



## MAYESO ODZIYESA NOKHA:

1. Lembani vesi yotsogolera

---

---

2. Kodi ndi maziko ati amene mfundo zonse za Ufumu wa Mulungu zimakhazikikapo?

---

3. Kodi ndi malamulo ati awiri amene mfundo zonse za Ufumu wa Mulungu zimakhazikika?

Mfundo yoyamba \_\_\_\_\_

Mfundo yachiwiri \_\_\_\_\_

4. Perekani zifukwa zinayi zakufunika kodziwa mfundo za Ufumu wa Mulungu.

---

---

5. Mukhoza kugwiritsa ntchito Babulo lanu pofuna kulondoleza mfundo imene vesi ili yonse ikuphunzitsa. Yang'anani vesi mu gawo loyamba ndipo sankhani mfundo yopezeka gawo lachiwiri imene ikugwirizana ndi vezi imene mwasankhayo. Lembani nambala kutsogoo kwa vesi mu gawo loyamba ndipo funso loyamba layankhidwa ngati chitsanzo.

### Gawo loyamba

### Gawo lachiwiri

a. 2 Mateyu 5:13-16 1.

Mfundo ya umodzi

b. \_\_\_\_\_ I Akorinto 12:12-14 2.

Mfundo yakufalikira

c. \_\_\_\_\_ Mateyu 20:26 3

Mfundo yapephero

d. \_\_\_\_\_ Mateyu 7:7-12 4.

Mfundo za Ufumu wa Mulungu zimasiyana ndi zadziko lapansi

Mfundo yaikulu ya Ufumu wa Mulungu:

e. \_\_\_\_\_ Mateyu 6:1-18 5.

mfundo yakhala ndi masomphenya amodzi

f. \_\_\_\_\_ Mateyu 6:19-34 6.

mfundo yakupembedza

**(Mayankho amafunso ali kumapeto kwa bukuli)**

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

**Fotokozerani mwachidule mfundo zimene zikuphunzitsidwa mu buku la Luka:**

Luka 1:33

---

4:43

---

6:20

---

7:28

---

8:1,10

---

9:2,11,27,60

---

10:9-11

---

11:2, 17-20

---

12:31-32

---

13:18-29

---

14:15

---

16:16

---

17:20-21

---

18:16-29

---

19:11-15

---

21:10,31

---

22:16-30

---

23:42, 50-51

## CHAPUTALA 8

### CHIKHALIDWE CHA UFUMU WA MULUNGU:

#### MFUNDO ZA UFUMU WA MULUNGU- GAWO LACHIWIRI

##### ZOLINGA:

Pamapeto pamaphunziro awa muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsolera osaonera.
- Kupeza kusiyana pakati pa ufumu wa Mulungu ndi maufumu a dziko lapansi.

##### VESI YOTSOGOLERA:

**Mverani, abale anga okonedwa; kodi Mulungu sanasankha osauka a dziko lapansi akhale olemera ndi cikhulupiriro, ndi olova nyumba a ufumu umene adaulonieza kwa iwo akumkonda iye? (Yakobo 2:5)**

### MAU OYAMBA

Mu chaputala ichi muphunzira zachikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu pamene mukupitiriza kuphunzira mfundo za Ufumu wa Mulungu. Muphunziranso mfundo za Ufumu wauzimu zimene zimakhazikika pa mfundo zazikulu zimene zakambidwa mu chaputala 7.

#### ZOTSUTSANA MU CHIKHALIDWE CHA UFUMU WA MULUNGU.

Pakadali pano tiona mfundo zenizeni zokhudza Ufumu wa Mulungu zimene zakhazikika pa mfundo zikuluzikulu zimene zakambidwa kale. Zambiri mwa mfundo zotsutsanazi zikupezeka pa Mateyu 5-7 ndi Luka 6. Werengani ndime zimenezi musanalipitirize ndi phunziroli.

Ndime zimenezi ndi mbali imodzi yachiphunzitso cha Yesu chimene chimatchedwa chiphunzitso chapaphiri. Izi zili choncho chifukwa anaphunzitsa zinthu zimenezi paphiri. Ndipo chiphunzitso chimenechi chili ndi mfundo zenizeni za Ufumu wa Mulungu. Sikuti chiphunzitso chapaphiri chimakamba chirichonse chokhudza moyo wa munthu, koma mfundo zake ndizothandiza m'magawo ambiri amoyo wa munthu. Chiphunzitso ichi chimakhazikitsa ndondomeko za m'mene munthu angakhali komanso m'mene munthu angachitire munyengo ina ili yonse.

Gawo loyamba lachiphunzitso chapaphiri chimatchedwa, Mateyu 5:1-12 Madalitso. Gawo limeneli limakamba khalidwe limene ndi lodalitsidwa mu Ufumu wa Mulungu. Iwo amene ali odala Machitidwe awo ndi osiyana ndi m'mene anthu ambiri amachitira. Mau oti odala mundime imeyi akutanthauza kuti kuvomelezedwa pamaso pa Mulungu. Pali kusiyana pakati pakukhala

odala ndi okodwa. Kukhala odala zimatengera Mulungu ndipo izi sizimayang'anira zimene mukudutsamo ayi. Pamene kukhala okondwa zimatengera nyengo zimene munthu akudutsamo.

Zinthu zina zimene ndizotsutsana ndi makhalidwe adziko lapansi ndi izi:

#### **UFUMU WA MULUNGU NDI WA IWO AMENE NDI OSAUKA MUUZIMU:**

**Odala ali osauka mumzimu; cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:3)**

Dziko limalemekeza iwo amene ali ndi chuma koma Mulungu amasankha anthu osauka a dziko lapansi ndikupanga olemera mu chikhulupiriro:

**Ndipo anamuza iye, M'Betelehemu wa Yudeya; cifukwa kunalembedwa kotere ndi mneneri, kuti, Mateyu 2:5**

**Ndipo pamene anaunguza-unguza pa iwo onse, anati kwa iye, Tansa dzanja lako, Ndipo iye anatero, ndi dzanja lace linabwerera momwe. Luka 6:10**

#### **OSAUKA NDIYE OLEMERA PAMENE OLEMERA NDIYE ALI OSAUKA:**

Dziko lapansi limalimbikitsa mzimu odzidalira pawekha, komanso kudzipititsa patsogolo wekha. Koma Mulungu amavomereza anthu amene ndi osauka muuzimu amene amazindikira kuperewera kwao kuti sangathe kudzipulumutsa okha, kukonza mavuto awo paokha komanso kukhala anthu auzimu pa iwo okha.

**Koma tsoka inu eni cuma! cifukwa mwalandira cisangalatso canu. (Luka 6:24)**

#### **CHISONI CHDZETSA CHIMWEMWE:**

Pali mitundu iwiri ya chisoni. Chisoni chapadziko lapansi chimadza chifukwa cha tchimo kapena kuti chimadza ngati zotsatira zatchimo. Chisoni chimenechi sichimabweretsa kusinthika kulikonse kwamakhalidwe a munthu. Chisoni cha umulungu ndi chisoni chimene chimadza polingalira machimo athu. Ndipo zotsatira za chisoni chimenechi ndi zakuti munthu amalapa machimo ake.

**Pakuti cisoni ca kwa Mulungu citembenezira mtima kuchipulumutso, cosamvetsanso cisoni; koma chisoni chadziko lapansi cicita imfa. (2 Akorinto 7:10)**

Mulungu afuna chisoni chotere ndipo onse amene akhala ndi chisoni choterechi adzatonthozedwa.

**Odala ali acisoni; cifukwa adzasangalatsidwa... (Mateyu 5:4)**

**Odala inu akumva njala tsopano; cifukwa mudzakhuta. Odala inu akulira tsopano; cifukwa mudzaseka. (Luka 6:21)**

**Indetu, indetu, ndinena ndi inu, kuti mudzalira ndi kubuma maliro inu, koma dziko lapansi lidzakondwera; mudzacita cisoni inu, koma cisoni canu cidzasandulika cimwemwe. (Yohane 16:20)**

Mu Ufumu wa Mulungu, iwo ali kulira adzatonthozedwa ndipo chisoni chimabweretsa chimwemwe. Kwa iwo amene ali kunja kwa Ufumu wa Mulungu, chimwemwe chidzasandulika chisoni.

Kufatsa sichikhalidwe chimene chimaonekera pachokha kwa munthu pachilengedwe chatu. Kukhala ofatsa kumatanthauza kukhala oleza mtima kapena kukhala munthu osapsya mtima nsanga. Izi zimasiyana ndi mfundo zadziko lapansi zimene zimafotokoza kuti munthu ayenera kukakamila zinthu zimene ndi zake komanso ufulu wake kapena kuti kulimbana ndi iwo akulimbana ndi ufulu wathu.

**Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)**

Makhalidwe onsewa ayenera kuoneka pakati pa mzika za Ufumu wa Mulungu. Izi ndi zipatso za Mzimu Woyera zimene zimabwera ngati zotsatira zodzadzidwa nd Mzimu Woyera. Izi zakambidwa mwadongosolo mu phunziro lina lotchedwa “Utumuiki wa Mzimu Woyera”

Dziko lapansi silimawerengera anthu ofatsa ngati ogonjetsa, koma Mulungu analonjeza kuti iwo akufatsa adzalandira dziko lapansi.

**Odala ali akufatsa; cifukwa adzalandira dziko lapansi. (Mateyu 5:5)**

### **ANJALA ADZAKHUTITSIDWA:**

Munthu amakhala ndi njala ya zinthu zambiri mu Ufumu wa dziko lapansi. Anthu amakhala ndi njala yakufuna ulamuliro, kuchita bwino kapenanso chisangalalo. Koma mzika za Ufumu wa Mulungu sizikuyenera kukhala ndi njala ya zinthu zakuthupi ngati zimenezi. Ife tiyenera kufunafuna kukhala olungama pamaso pa Mulungu chifukwa iyi ndiye mfundo yaikulu ya ufumu wa Mulungu.

**Odala ali akumva njala ndi ludzu la cilungamo; cifukwa adzakhuta. (Mateyu 5:6)**

**Odala inu akumva njala tsopano; cifukwa mudzakhuta. Odala inu akulira tsopano; cifukwa mudzaseka. (Luka 6:21)**

Pali anthu ena okhulupirira amene amapita kumikumano yachipembedzo ndi cholinga choti apeze m'dalitso wa Mulungu. Iwo samakhutitsidwa pamoyo wao wauzimu. Koma Yesu Khristu anapereka mfundo ya Ufumu wa Mulungu yoti iwo akumva njala ya chilungamo chake adzakhutitsidwa.

Kudziko la kuthupi, munthu sumangokhala pamene wamva njala ndikuyembekezera kuti chakudyacho chikupeza. Umayenera kuchitapo kanthu posakasaka chakudya komanso kuphika chakudyacho. Chimodzimodzinso, kudziko lauzimu, sumangokhala kudikira kuti Mulungu akhutitsa njala yako yauzimu. Muyenera kutengapo gawo pakufunafuna chakudya chazimu kudzera mu Pemphero komanso kuwerenga mau a Mulungu.

Amene amva njala amakhutitsidwa mu Ufumu wa Mulungu pamene iwo amene ali mu maufumu adziko lapansi amakhala ndi njala.

**Tsoka inu okhuta tsopano! cifukwa mudzamva njala, (Luka 6:25)**

**ZOCHOKERA MKATI OSATI ZOONEKERA PANJA:**

Atsogoleri anthawi ya Yesu Khristu amasamala kusunga malamulo mwachikhalidwe chabe ndipo iwo samasamala moyo wao wauzimu mkati mwao. Iwo amusunga sabata osaphonyetsa, kusala chakudya pafupipafupi ndipo iwo amapemphera ndikuchita ntchito zachifundo kuti anthu awaone.

Koma Yesu anatsindika zakufunika kokonza mkati mwathu osati kungosamala moanekedwe athu achipembedzo pamaso pa anthu.

**Odala ali oyera mtima; cifukwa adzaona Mulungu. (Mateyu 5:8)**

Si anthu amene ali nao maonekedwe achipembedzo amene adzaone Mulungu, koma ndi iwo amane ali oyera mtima adzaone Mulungu.

**MTENDERE OSATI KUGALIKURA:**

Kugalukira kapena kuukira ndi njira imene dziko lapansi imagwiritsa ntchito pofuna kusintha Ufumu kapena ulamuliro padziko lapansi. Anthu obweretsa mtendere ndi iwo amene amabweretsa kusintha mu Ufumu wa Mulungu. Yesu Khristu anati:

**Odala ali akucita mtendere; cifukwa adzachedwa ana a Mulungu. (Mateyu 5:9)**



Mtendere sikuthawa mavuto ayi kapena nkhondo ndi kulimbana. Mtendere umene Yesu Khristu anayankhula si mtendere wa dziko lapansi ayi:

**Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa. Mtima wanu usabvutike, kapena usacite mantha. (Yohane 14:27)**

Mtendere wapadziko lapansi umabweretsa mantha chifukwa nthawi zina anthu amakhala akukayika ngati mbali imodzi ingalemekeze pangano lamtendere kapena malonjezano. Pamene pali mtendere wa Mulungu sipamakhala mantha. Okhulupirira akhoza kukhala ndi mtendere ngakhale pamalo pamene pali chisokonekero pano padziko lapansi.

### **ODALA IWO AKUZUNZIDWA CHIFUKWA ADZALANDIRA MPHOTO:**

Mfundo imeneyi ikulengeza madalitso kwa iwo amene akumana ndi mazuzo chifukwa cha chilungamo chao:

**Odala ali akuzunzidwa chifukwa ca cilungamo: chifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:10)**

**Odala inu, pamene anthu adzada inu, nadzapatula inu, nadzatonza inu, nadzalitaya dzina lanu monga loipa, chifukwa ca Mwana wa munthu. Kondwerani tsiku lomweli, tumphani ndi cimwemwe; pakuti onani, mphotho zanu nzazikuru Kumwamba; pakuti makolo ao anawacitira aneneri zonga zomwezo. (Luka 6:22-23)**

**Tsoka inu, pamene anthu onse adzanenera inu zabwino! pakuti makolo ao anawatero momwemo ananeri onama. (Luka 6:26)**

Izi sizikutanthuaza kuti onse amene akumana ndi mazuzo ndi odala. Ena amazunzika chifukwa cha zolakwika zao zomwe:

**Pakuti mbiri yokoma yanji, mukapirira pocimwa ndi kubwanyulidwapo? Komatu, ngati pocita zabwino, ndi kumvako zowawa mumapirira, kumeneko ndiko cisomo pa Mulungu. (1 Petulo 2:20)**

Nthawi zina chizuzo chimabwera chifuka cha tchimo:

**Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akuru a Mpingo, ndipo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m'dzina la Ambuye: ndipo pemphero la cikhulupiriro lidzapolumutsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa; ndipo ngati adacita macimo adzakhululukidwa kwa iye. Chifukwa cace mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzace kuti muciritsidwe.**

**Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidwe ace.  
(Yakobo 5:14-16)**

#### **WANG'ONO ADZATCHEDWA WAMKULU:**

Pa dziko lapansi, anthu opambana amalemekezedwa ndipo anthu amayesedwa opambana ngati ali ndi chuma kapena ndi otchuka. Pamene muufumu wa Mulungu, munthu amene amaphunzitsa mfundo zaufumu ndi amene ali wamkulu. Anthu oterewa okhoza kuyesedwa opanda pake pa dziko lapansi koma iwo ndi akulu mu Ufumu wa Mulungu.

**Cifukwa cace yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu comweco, adzachulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakucita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzachulidwa wamkulu mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 5:19)**

#### **ODZICHEPETSА ADZAKWEZEDWA:**

**Ndipo amene ali yense akadzikuza yekha adzacepetsedwa; koma amene adzicepetsa mwini yekha adzakulitsidwa. (Mateyu 23:12)**

#### **ATSOGOLERI NDIWO OTUMIKIRA:**

Dziko lapansi limapereka ulemu wambiri kwa atsogoleri. Iwo amalemekezedwa ndi kukwezedwa. Ndipo nthawi zambiri atsogoleri amatengedwa ngati anthu apamwamba osiyana ndi anthu onse:

Mu Ufumu wa Mulungu, iye ofuna kutsogolera ayenera kukhala otumikira:

**Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo. Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri. (Mateyu 20:25-28)**

**Koma sipadzatero ndi inu; komatu iye ali wamkuru mwa inu, akhale ngati wamng'ono; ndi iye ali woyamba, akhale ngati wotumikira. Luka 22:26**

**Koma mwa inu sikutero ai; kama amene ali yense afuna kukhala wamkuru mwa inu adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. (Marko 10:43-44)**

**Koma wamkuru wopambana wa inu adzakhala mtumiki wanu (Mateyu 23:11)**

**OMALIZA NDIWO OYAMBA:**

Iwo amene ndi oyamba mu Ufumu wa dziko lapansi ndi omaliza mu Ufumu wa Mulungu.

**Koma ambiri oyamba adzakhala akuthungo, ndi akuthungo adzakhala oyamba. (Mateyu 19:30)**

**Comweco omarizira adzakhala oyamba, ndipo oyamba adzakhala omarizira. (Mateyu 20:16)**

**Ndipo onani, alipo akuthungo amene adzakhala oyamba, ndipo alipo oyamba adzakhala akuthungo. (Luka 13:30)**

**OCHEPA ADZAKHALA AKULU:**

Yesu anaonetsera mfundo imeyi pogwiritsa ntchito zitsanzo za mbeu yampiru, chotupitsa, zopereka za mkazi wamasiye:

**Ufumu wa Kumwamba uli wofanafana ndi kambeu kampiru, kamene anakatenga munthu, nakafesa pamunda pace; kamene kakhaladi kakang'ono koposa mbeu zonse, koma katakula, kali kakakuru kuposa zitsamba zonse, nukhala mtengo, kotero kuti mbalame za mlengalenga zimadza, nizibindikira mu nthambi zace. Fanizo lina ananena kwa iwo; Ufumu wa Kumwamba uli wofanafana ndi cotupitsa mikate, cimene mkazi anacitenga, nacibisa m'miyeso itatu ya ufa, kufikira wonse unatupa. (Mateyu 13:31-33. Werenganso also (Marko 4:30-32)**

**Ndipo Yesu anakweza maso, naona anthu eni cuma alikuika zopereka zao mosungiramo ndalama. Ndipo anaona mkazi wina wamasiye waumphawi alikuika momwemo timakobiri tiwiri. Ndipo iye anati, Zoonadi ndinena kwa inu, wamasiye uyu waumphawi anaikamo koposa onse; pakuti onse amenewa anaika mwa unyinji wao pa zoperekazo; koma iye mwa kusowa kwace anaikamo za moyo wace, zonse anali nazo. (Luka 21:1-4)**

**CHOKUZIKA PAMASO PA ANTHU CHINYOZEKA PAMASO PA MULUNGU.**

**Ndipo anati kwa iwo, Inu ndinu odziyesera nokha olungama pamaso pa anthu; koma Mulungu azindikira mitima yanu; cifukwa ici cimene cikuzika mwa anthu ciri conyansa pamaso pa Mulungu. (Luka 16:15)**

## **AKULU AMAKHALA ANA:**

Mu Ufumu wa Mulungu, akulu ayenera kukhala ngati ana. Izi zikutanthauza kuti iwo amayenera kuvomereza Uthenga Wabwino ndi chikhulupiriro changati chamwana:

**Nthawi yomweyo ophunzira anadza kwa Yesu, nanena, Ndani kodi ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba? Ndipo pamene Yesu anaitana kamwana, anakaimitsa pakati pao, nati, Indetu ndinena kwa inu, Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. Cifukwa cace yense amene adzicepetsa yekha monga kamwana aka, yemweyo ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 18:1-4)**

**Koma Yesu anawaitana, nanena, Lolani ana adze kwa Ine, ndipo musawaletse; pakuti Ufumu wa Mulungu uti wa otere. Indetu ndinena kwa inu, Ali yense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati mwana, sadzalowamo ndithu (Luka 18:16-17.)**

## **OTAYA MOYO WAKE AUPEZA:**

**Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ngati mbeu ya tirigu siigwa m'nthaka, nifa, ikhala pa yokha iyo; koma ngati ifa, ibala cipatso cambiri. (Yohane 12:24)**

**Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; ndipo yense wakutaya moyo wace cifukwa ca Ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwino, adzaupulumutsa. (Marko 8:35)**

**Iye amene apeza moyo wace, adzautaya; ndi iye amene ataya moyo wace, cifukwa ca Ine, adzaupeza. (Mateyu 10:39)**

Munthu amataya moyo wake pokana zilakolako za thupi za dziko lapansi ndi cholinga chofuna kutsata Mulungu:

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. Pakuti iye amene afuna kupulumutsa moyo wace adzautaya: koma iye amene ataya moyo wace cifukwa ca Ine, adzaupeza. (Mateyu 16:24-25)**

## **KUDANA NDI MOYO OSATI KUUKONDA:**

**Iye wokonda moyo wace adzautaya; ndipo wodana ndi moyo wace m'dziko lino lapansi adzausungira ku moyo wosatha. (Yohane 12:25)**

## **PEREKANI KUTI MULANDIRE:**

**Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu; muyeso wabwino, wotsendereka, wokhutchumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani m'manja mwanu. Pakuti 7 kudzayesedwa kwa inu ndi muyeso womwewo muyesa nao inu. (Luka 6:38)**

## **ZOSATHEKA ZIMATHEKA:**

**Koma iye anati, Zinthu zosatheka ndi anthu zitheka ndi Mulungu. (Luka 18:27)**

**Ndipo Yesu anawayang'ana, nati kwa iwo, ici sicitheka ndi anthu, koma zinthu zonse zitheka ndi Mulungu. (Mateyu 19:26)**

**Yesu anawayang'ana iwo nati, Sikutheka ndi anthu, koma kutheka ndi Mulungu; pakuti zinthu zonse zitheka ndi Mulungu. (Marko 10:27)**

## **ALI NDI MASO NDI AKHUNGU NDIPO AKHUNGU AMAPENYA:**

**Ndipo Yesu anati, Kudzaweruza ndadza Ine ku dziko lino lapansi, kuti iwo osapenya apenye; ndi kuti iwo akupenya akhale osaona (Yohane 9:39)**

Yesu anabwera kudzapereka maso auzimu kwa iwo otayika mu mdima wauzimu. Atsogoleri achipembedzo amene amaona ngati amapenya, sapenya.

## **KUSENZA GORI NDI ZOWAWA NDI ZOLEMETSА KUTI UPEZE MPUMURO:**

Goli ndi chida chimene chimagwira ntchito yomangilira nyama kungolo ndipo mau oti goli amaonetsera kuti pali ntchito imene ikugwirika. Cholemetsa ndi chinthu chimene chimanyamulidwa. Yesu anafotokoza kuti:

**Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti 1 gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-30)**

Timapeza mpumulo weniweni pamene tamangidwa limodzi ndi Yesu Khristu ponyamula goli lake. Goli la Yesu Khristu ndi chikhumbokhumbo choti Uthenga ulalikidwe dziko lonse lapansi.

## **KUTSINDIKIZIDWA CHUMA CHAKUMWAMBA OSATI CHA DZIKO LAPANSI:**

**Musadzikundikire nokha cuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: koma mudzikundikire nokha cuma m'Mwamba, pamene njenjete kapena dzimbiri siziononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba; pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso. (Mateyu 6:19-21)**

Yesu Khristu anafananiza iwo akutsindika chuma chapadziko lapansi ndi munthu opusa:

**Atero iye wakudziunjikira cuma mwini yekha wosakhala naco cuma ca kwa Mulungu, (Luka 12:21)**

### **ULEMELERO WA KUMWAMBA OSATI WA DZIKO LAPANSI:**

**Iye wolankhula zocokera kwa iye yekha afuna ulemu wa mwini yekha, iye wakufuna ulemu wa iye amene anamtuma, yemweyu ali wona, ndipo mwa iye mulibecosalungama. (Yohane 7:18)**

**Mungathe inu bwanji kukhulupira, popeza mulandira ulemu wina kwa mnzace ndipo ulemu wakucokera kwa Mulungu yekha simuufuna? (Yohane 5:44)**

**Yesu anayankha, Ngati Ine ndidzilemekeza ndekha, ulemerero wanga uli cabe; Atate wanga ndiye wondilemekeza Ine; amene munena za iye, kuti ndiye Mulungu wanu; (Yohane 8:54)**

### **KUGAWIKANA OSATI MTENDERE:**

Yesu Khristu ndiye mtendere. Pamene anabwera kuthupi pa dziko lapansi, nthawi imeneyo kunali mtendere. Koma Iye anabweretsa kugawanikana osati mtendere ku maufumu a dziko lapansi. Mabanja, mizinda ndi maufumu anagawanikana chifukwa cha iye. Ena anamukhulupulira iye ndikumuvomeleza ngati mbuye ndi mphulumutsi. Ndipo anakhala mzika za Ufumu wa Mulungu kudzera mukubadwanso mwatsopano. Ena sanamulandire Iye ngati mfumu. Chifukwa cha ichi, sanali mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu. Izi zinabweretsa kugawanika.

**Kodi muyesa kuti ndinadzera kudzapatsa mtendere pa dziko lapansi? Ndinena kwa inu, Iaitu, komatu kutsutsana; pakuti kuyambira tsopano adzakhala m'nyumba imodzi anthu asanu, atatu adzatsutsana ndi awiri, ndi awiri adzatsutsana ndi atatu. Adzatsutsana atate ndi mwana wace, ndi mwana ndi atate wace; amace adzatsutsana ndi mwana wamkazi ndi mwana wamkazi ndi amace, mpongozi adzatsutsana ndi mkazi wa mwana wace, ndi mkaziyo ndi mpongozi wace. (Luka 12:51-53)**

**... ndipo apabanja ace a munthu adzakhala adani ace. Mateyu 10:36**

## **ZOBISIKA ZONSE ZIDZAULURIKA:**

**Pakuti palibe kanthu kanabvundikiridwa, kamene sikadzaululidwa; kapena kanthu kobisika, kamene sikadzadziwika. Cimene ndikuuzani inu mumdima, tacinenani poyera; ndi cimene mucimva m'khutu, mucilalikire pa macindwi nyumba. (Mateyu 10:26-27)**

## **UFUMU UNABWELERA ANTHU OCHIMWA OSATI OLUNGAMA:**

**Koma mukani muphunzire nciani ici: Ndifuna cifundo, si nsembe ai; pakuti sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa. (Mateyu 9:13)**

## **KUTSINDIKA ZAUZIMU OSATI KUTHUPI:**

**Pakuti ufumu wa Mulungu sukhalakakudya ndi cakumwa, koma cilungamo, ndi mtendere, ndi cimwemwe mwa Mzimu Woyera. Aroma 14:17**

**Pakuti ufumu wa Mulungu sulim'mau, koma mumphamvu, Mufuna ciani? Akorinto 4:20**

### **Zotsutsana zoonjezera**

Gwiritsani ntchito ma vesi ali munsimuwa kuti muonjezere zinthu zina zotsutsana pakati pa Ufumu wa dziko lapansi ndi wa kumwamba.

Njira ndi zipata ziwiri:	Mateyu 7:13-14
Aneneri awiri:	Mateyu 7:15
Mitengo iwiri:	Mateyu 7:17-20; Luka 6:43-44
Onse amati adzalowa kumwamba:	Mateyu 7:21-23
Nyumba ziwiri:	Mateyu 7:24-27; Luka 6:46-49



## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

---

---

2. Lembani mau oyenelera pa mpata umene ili munsimu kuti mumalize ziganizo zili munsimu.

### Mfundo za Ufumu wa Mulungu

- a. Osauka ndi \_\_\_\_\_.
- b. chisoni chimabweretsa \_\_\_\_\_.
- c. Akufatsa ndi \_\_\_\_\_.
- d. Anjala \_\_\_\_\_.
- e. Achifundo adzalandira \_\_\_\_\_.
- f. zamkati mwa munthu osati \_\_\_\_\_ zimatsindikizidwa
- g. Kugawiakana m'malo mwa \_\_\_\_\_.
- h. Ozunzidwa \_\_\_\_\_.
- i. Omaliza adzakhala \_\_\_\_\_.
- j. Odzichepetsa \_\_\_\_\_.
- k. Otutumukira ndi \_\_\_\_\_.
- l. omaliza adzakhala \_\_\_\_\_.
- m. wang'ono adzakhala \_\_\_\_\_.
- n. Zinthu zolandira ulemu \_\_\_\_\_.
- o. Akulu adzakhala \_\_\_\_\_.
- p. Umafa kuti \_\_\_\_\_.
- q. Umataya moyo wako kuti \_\_\_\_\_.
- r. Umadana ndi moyo kuti \_\_\_\_\_.
- s. Umapereka kuti \_\_\_\_\_.
- t. zosatheka zimakhala \_\_\_\_\_.
- u. Akhungu ndi \_\_\_\_\_.
- v. Umasenza goli ndi cholinga choti \_\_\_\_\_.
- w. Zakumwamba osati \_\_\_\_\_ chuma chimatsindikizidwa.
- x. chili chonse chobisika \_\_\_\_\_.

## CHAPUTALA 9

### CHIKHALIDWE CHA UFUMU:

#### MFUNDO ZA UFUMU: GAWO LACHITATU

#### ZOLINGA:

Pamapeto paphunziro ili, muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza ubale wa pakati pa Mfundo za chipangano Chakale ndi Chatsopano.
- Kupeza malamulo a Chipangano Chatsopano amene azamitsidwa mu chipangano Chatsopano.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Koma unyinji wa anthu, pamene anadziwa, anamtsata Iye; ndipo iye anawalandira, nayankhula nao za Ufumu wa Mulungu, naciritsa amene anasowa kuciritsidwa. (Luka 9:11)**

#### MAU OYAMBA

Chaputala ichi chikupitiliza kuona za Chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu pounikira ubale wapakati pa malamulo a Chipangano Chakale ndi Chatsopano.

#### CHUMA CHOBISIKA: CHAKALE NDI CHATSOPANO

Mu chitsanzo chimodzi chimene Yesu anapereka chokhudza Ufumu wa Mulungu, Iye anatsindika kubwera pamodzi kwa mfundo zakale ndi zatsopano:

**Ndipo Iye anati kwa iwo, Cifukwa cace, mlembi ali yense, wophunzitsidwa mu Ufumu wa Kumwamba, ali wofanana ndi munthu mwini banja, amene aturutsa m'cuma cace zinthu zakale ndi zatsopano (Mateyu 13:52)**

Mfundo zimene Yesu Khristu anaphunzitsa zinali zakale ndi zatsopano. Yesu anatcha zimenezi ngati chuma chakale ndi chatsopano. Chilamulo chopezeka m'mabuku a Ekisodo, Livitiko ndi Deteronome chinakhala maziko a mfundo za moyo mu Ufumu. Ndipo chilamulo cha Chipangano Chakale chimakhudza kwambiri m'mene munthu angachitire kapena machitidwe owoneka ndi maso. Pamene mfundo zimene Yesu Khristu anaphunzitsa zimakhudza kwambiri zamkati mwa mtima wa munthu osati zooneka ndi maso.

Chiphunzitso cha Yesu sikuti chinathetsa Chilamulo, koma kukwanilitsa:

**Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula cilamulo kapena aneneri, sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kace kamodzi sikadzaeokera kucilamulo, kufikira zitacidwa zonse. (Mateyu 5:17-18)**

**Ndipo anati kwa iwo, Awa ndi mauwo ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'cilamulo ca 6 Mose, ndi aneneri, ndi masalmo. (Luka 24:44)**

Yesu anapereka kamvetsetsedwe kena ka mfundo za Ufumu pogwiritsa ntchito maziko a Chipangano Chakale. Iye sanabwera kudzathetsa Chilamulo koma kuchikwanilitsa. Iye anatsindika zakufunikira kosamala zinthu za mkati mwathu osati maonekedwe chabe.

Chiphunzitso cha Yesu chinali chogwirizana ndi Chipangano Chakale, koma chinali chosemphana ndi atsogoleri achipembedzo anthwawi imeneyo. Alembi ndi Afarisi amaonjezera kamvetsetsedwe ndi zikhalidwe zao pofuna kumvetsetsa mau a Mulungu. Iwo amalimbana kwambiri ndi kungosunga chilamulo chonse kuonjezera zikhalidwe zao ndi kamvetsetsedwe kao ka chilamulo. Pamene Yesu amatsindika mfundo zazikulu zokhala kuseli kwa chilamulo.

### **MFUNDO ZAKALE ZILIBE ZATSOPANO**

Mfundo zimene Yesu anaphunzitsa sizimapezeka mu chipembedzo chakale. Yesu Khristu anaonetsera mfundo imeneyi pokamba nkhani ziwiri. Anakamba za nsalu yakale ndi yatsopano.

**Ndipo kulibe munthu aphathika cigamba ca nsaru yaiwisi pa copfunda cakale; pakuti cigamba cace cizomoka ku copfundaco, ndipo cicita ciboo cacikuru. (Mateyu 9:16)**

**Palibe munthu asokerera cigamba ca nsaru yaiwisi pa copfunda cakale; pena cimene coti cidzakonza cizomolapo, catsopanoco cizomoka pa cakaleco, ndipo ciboo cikulapo. (Marko 2:21)**

**Ndipo iye ananenanso fanizo kwa iwo, kuti, Palibe munthu ang'amba cigamba ca malaya atsopano, naciphatika pa malaya akale; cifukwa ngati atero, angong'ambitsa atsopano, ndi cigamba ca atsopano sicidzayenerana ndi akalewo. (Luka 5:36)**

Iye anakambaso za vinyo wakale ndi watsopano:

**Kapena samathira vinyo watsopano m'matumba akale; akatero, matumba aphulika, ndi vinyo atayika, ndi matumba aonongeka: koma athira vinyo watsopano m'matumba atsopano, ndi zonse ziwiri zisungika. (Mateyu 9:17)**

**Ndipo palibe munthu amatsanulira vinyo watsopano m'matumba akale: pena vinyo adzaphulitsa matumba, ndipo aonongeka vinyo, ndi matumba omwe: koma vinyo watsopano amatsanulira m'matumba atsopano. (Marko 2:22)**

**Ndipo palibe munthu atsanulira vinyo watsopano m'matumba akale; cifukwa ngati atero, vinyo watsopanoyo adzaphulitsa matumba, ndipo ameneyo adzatayika, ndi matumba adzaonongeka. Koma kuyenera kutsanulira vinyo watsopano m'matumba atsopano. Ndipo palibe munthu atamwa vinyo wakale afuna watsopano; pakuti anena, Wakale ali wokoma. (Luka 5:37-39)**

Mapembedzedwe akale sakanatha kupezeka ndi vinyo watsopano wa Mfundo za Ufumu wa Mulungu. Vinyo watsopano ayenera kuikidwa mu chotengera chatsopano. Ichi ndi chifukwa chake kuti munthu alowe mu Ufumu wa Mulungu, ayenera kubadwanso muuzimu.

Yesu Khristu sanaononge mapembedzedwe akale koma iye analora kuti mapembedzedwe akale asungike kwinku akuthira vinyo watsopano muzotengera zauzimu zatsopano za amayi ndi abambo obadwanso mwatsopano mwakhristu Yesu. Iye analola kuti nthawi idutse kuti anthu achoke mu Ufumu wakale ndi kulowa watsopano.

Imeneyi ndi mfuno yofunika kwambiri pamene titalitsa Uthenga Wabwino mumadera amene ali ndi zipembedzo zina kale. Cholinga chenicheni chikhale kuthira vinyo watsopano muzotengera zatsopano osati kulimbana ndi kuononga chipembedzo chakale cha anthu. Chipembedzo chakale cha anthu chimatha chokha pamene abambo ndi amayi azindikira kuti vinyo watsopanoyo ndi wabwino kusiyana ndi wakale.

#### **NDONDOMEKO ZA KAZINDIKIRIDWE KA MFUNDO ZAKALE NDI ZATSOPANO:**

Mukhoza kuzindikira mfuno zakale ndi zatsopano mu chipangano Chatsopano poona kagwiritsidwe ntchito ka mau awa:

1. Yesu amayamba kuphunzitsa ziphunzitso zimenezi ndi mau oti “kunalembedwa kapena munawerenga”
2. Chipangano chakale chimatchulidwa.
3. Yesu Khristu amati, “koma ndikuuzani inu”
4. Mfundo za Ufumu zochokera mu Chipangano Chakale zimatchulidwa

#### **MFUNDO ZA UFUMU**

M'ndandanda uli munsiu ukufotokoza mfundo za ufumu wa Mulungu zimene zopezeka mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano zimene Yesu Khristu anaphunzitsa. Onani ndime zalembedwazi kuti mukasanthule Mfundo za Ufumu wa Mulungu.

**Mfundo yakale**

**Mfundo yatsopano**

**“Kunalembedwa”**

**“koma ndikuuzani”**

Mateyu 5:21-26      Usaphe  
ndikupha

Mkwiyo popanda chifukwa

kupembedza kumatengera zochita zathu

kupembedza kumatengera mtima wathu.

Mateyu

6:1-8;

23:14,23-27

Marko

7:6-8;

11:25-26

Luka

18:10-14

Mateyu              Usachite chigololo.

Kuganizira ndikuchita kale.

5:27-32

Mateyu              Musalumbire kumwamba

musalumbire pa chilichonse

5:33-37

23:16-22

Mateyu              Diso kwa diso

mudzibweza choipa ndi chabwino

5:38-42

Mateyu              kondani nansi wanu

mudzikonda adani anu

5:43-47

Luka

6:27-35

Mateyu              Chiyero chimadza potsata mfundo za Ufumu

Chiyero ndi kusunga  
mfundo zopangidwa ndi anthu.

15:3-9

Maliko

7:7-13

Mateyu              Munthu analengedwa kuti  
Asunge sabata ndipo aligwiritsitse

Sabata linapangidwira munthu

12:3-14

Maliko

2:23-28;

3:1-6;

Luka

6:1-11;

Yohane

5:1-47		
Mateyu	Kutsindika chiyero chakunja.	Kutsindika chiyero cha mkati.
15:10-20;		
Maliko		
7:14-23		
Mateyu	chilekano pa chifukwa chili chonse.	Chilekano si dongosolo la Mulungu
5:31-3		koma pazifukwa zochepe anthu
19:1-9		akhoza kulekana
Maliko		
10:2-12		

M'ndandanda mwaonau sikuti uli ndi mfundo zonse za Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Wangotsindika zitsanzo zikuluzikulu zimene zingakuthandizileni kuti mupitilizebe kuphunzira panokha.

Werengani mabuku a Maliko, Luka, Mateyu ndi Yohane kuti mukaphunzire zambiri.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsolera osaonera

---

---

2. Lembani mau oti “Yakale” kapena “Yatsopano” ma mipata imene yaperekedwayo kuti muonetsera ngati mfundooyo ili yakale kapena yatsopano.

- a. \_\_\_\_\_ kutsindika za mkati mwa munthu.
- b. \_\_\_\_\_ kutsindika machitidwe ndi kaonekedwe ka zinthu
- c. \_\_\_\_\_ Ndiyolunjika.
- d. \_\_\_\_\_ Imapereka mwayi waukulu kapena ufulu
- e. \_\_\_\_\_ Chilamulo chitsatidwe m'mene chalembedwera.
- f. \_\_\_\_\_ Kutsata zimene lamulo limatanthauza
- g. \_\_\_\_\_ Usaphe.
- h. \_\_\_\_\_ Kukwiya opanda chifukwa ndi kupha kumene
- i. \_\_\_\_\_ Musalumbire pa china chilichonse.
- j. \_\_\_\_\_ Musalumbire Mwa inu nokha.
- k. \_\_\_\_\_ bwezani choipa ndi chabwino.
- l. \_\_\_\_\_ bwezani choipa kwa choipa.
- m. \_\_\_\_\_ Kondani anansi anu.
- n. \_\_\_\_\_ Kondani adani anu.
- o. \_\_\_\_\_ Kupembedza kumatengera zimene zili mkati mwanu.
- p. \_\_\_\_\_ kupembedza kumatengera zimene mumachita.
- q. \_\_\_\_\_ Sabata linapangidwa munthu.
- r. \_\_\_\_\_ Munthu anapangiridwa sabata.
- s. \_\_\_\_\_ Chiyero ndi kusunga malamulo a anthu.
- t. \_\_\_\_\_ Chiyero ndi kusunga Chilamulo cha Mulungu.
- u. \_\_\_\_\_ Kutsindika chiyero chakunja.
- v. \_\_\_\_\_ kutsindika chiyero chamkati.
- w. \_\_\_\_\_ Chilekano pazifukwa zochepa.
- x. \_\_\_\_\_ Chilekano pa chifukwa chilichonse.

3. Zungulizani yankho limene ndi lolondora kuti mumalizitse ziganizo zili munsimu.

Yesu anabwera kuti \_\_\_\_\_

- a. Kudzafafaniza Chipangano Chakale
  - b. Kudzakwanilitsa Chilamulo cha Chipangano Chakale.
4. Kodi pali ubale wanji pakati pa Chipangano Chakale ndi mfundo za Chipangano Chatsopano.
- 

**(Mamayanko mafunso ali kumapeto kwa buku ili)**



## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Buku la Yohane lilibe ma vesi ambiri okamba za ufumu wa Mulungu. koma mavesi ochepa omweo ndi ofunika kwambiri.

Yohane 1:45-49: Natanieli anamuzindikila Yesu ngati Mfumu komanso Iye ngati kukwanilitsidwa kwa ulosi wa Chipangano Chakale.

Yohane chaputala cha 3 ndi chaputala chimodzi chofunika kwambiri chimene chimafotokezera malowedwe a Ufumu wa Mulungu.

Yohane 8:36 ndi vesi yofunika ya Ufumu wa Mulungu, imafotokozera kuti Ufumu wa Mulungu siwapadziko pano.

2. Pitirizananibe kuphunzira panokha zokhudza mfundo zakale ndi zatsopano za ufumu wa Mulungu mu ma Buku a Uthenga Wabwino ndi Yohane. Ndipo lembani zimene mupeze pa mpati uli pansipa.

### **Mfundo yakale**

“kunalembedwa”

### **mfundo yatsopano**

“koma ndikuuzani ine”

---

---

---

---

---

---

---

---

## CHAPUTALA 10

### MAFANIZO A UFUMU

#### ZOLINGA:

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanits zinthu izi;

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la “fanizo”
- Kufotokoza chifukwa chimene Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo pophunzitsa mfundo za Ufumu wa Mulungu.
- Kuphunzira mafanizo a Yesu ndi cholinga choti muzindikire mfundo za Ufumu.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Ndipo Iye anayankha nati, Cifukwa kwapatsidwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa Kumwamba, koma sikunapatsidwe kwa iwo. (Mateyu 13:11)**

Mu chaputala chapitachi, taphunzira mfundo zoyendetsera moyo mu Ufumu wa Mulungu. Munthawi ya Utumiki wake pa dziko lapansi, Yesu anali kugwiritsa ntchito njira yapaderadera pofuna kuphunzitsa. Ndipo njira imeneyi ndi “mafanizo.” Amachita izi pofuna kuulula choonadi chazimu cha Ufumu wa Mulungu.

Mu chaputala chimenechi, muphunzira tanthauzo la fanizo komanso chifukwa chimene Yesu Khristu amagwiritsa ntchito mafanizo. Ndipo tionanso mafanizo owerengeka okhudza Ufumu wa Mulungu.

#### KODI FANIZO NDI CHIANI?

Fanizo ndi nkhani imene imagwiritsa ntchito chitsanzo chakuthupi pofuna kuonetsera choonadi chazimu. Koma tanthauzo lenileni la mau oti “fanizo” ndi kufananiza zinthu. Mu mafanizo, Yesu amagwiritsa ntchito chitsanzo chakuthupi kenako ndikuchifananitsa ndi choonadi chazimu. Tikhoza kunena kuti fanizo ndi nkhani yapadziko lapansi koma yokhala ndi tanthauzo lakumwamba. Chinthu chakuthupi ndi chimene tikhoza kuona ndi maso athu, kuchigwira kapena kuchimva kumene. Pamene chinthu chazimu ndi chimene chikhoza kuzindikiridwa ndi makutu auzimu.

## MUTU WAUKULU WA MAFANIZO

Mutu waukulu wa mafanizo a Yesu unali Ufumu wa Mulungu ndipo nthawi zina asanalakhule ena mwa mafanizo amenewa, Iye amafotokoza mutu wake.

**Ndipo ananena, Tidzafaniziranji Ufumu wa Mulungu? kapena tidzaulinganiza ndi fanizo lotani? (Maliko 4:30)**

**Ndipo pempherani kuti kusakhale m'nyengo yacisanu. (Maliko 13:18)**

**Ndipo Ambuye akadapanda kufupikitsa masikuwo, sakadapulumuka munthu mmodzi yense; koma cifukwa ca osankhidwa amene anawasankha, anafupikitsa masikuwo. (Maliko 13:20)**

Ngakhale mutu wa fanizo usatchulidwe mwachindunji, komabe mutu wake umakhalabe Ufumu wa Mulungu. Mafanizo onse a Yesu amakhala okhudzana ndi Ufumu wa Mulungu kapena munjira ina yake, amakhala ogwirizana ndi Ufumu wa Mulungu.

### **NDI CHIFUKWA CHIANI YESU AMAGWIRITSA NCHITO MAFANIZO?**

Kodi ndi chifukwa chiani Yesu Khristu anasankha kugwiritsa ntchito njira imeneyi pofuna kuvumbulutsa choonadi chazimu cha ufumu wa Mulungu? Ophunzira ake anafunsaso funso lomweri:

**Ndipo ophunzirawo anadza, nati kwa Iye, Cifukwa canji muphiphiritira iwo m'mafanizo? (Mateyu 13:10)**

Ndipo Yesu anawayankha iwo nati:

**... Mateyu 13:11 Cifukwa kwapatsidwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa Kumwamba, koma sikunapatsidwa kwa iwo. Werenganinso (Luka 8:10)**

Chidziwitso cha choonadi cha Ufumu wa Mulungu chinaperekedwa kwa ophunzira a Yesu Khristu chifukwa iwo anali ndi kaonedwe kuzimu. Koma anthu opanda maonedwe auzimu kunali kovuta kuti amvetsetse mafanizo chifukwa choonadi chake ndi cha anthu okhao amene ali ndi maonedwe auzimu a zinthu.

**Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu. (1 Akorinto 2:14)**

Iwo amene ali ndi maonedwe auzimu amatha kumvetsa mfundo za Ufumu wa Mulungu zopezeka mu mafanizo. Koma iwo amene ali ndi maganizo kuthupi kapena akukhala mu uchimo, sangamvetse zinthu izi. Yesu khristu amagwiritsa ntchito mafanizo ndi cholinga choti akabise choonadi cha Ufumu wa Mulungu kwa anthu osakhulupirira.

## **MAFANIZO MU UFUMU.**

Mafanizo onse amane Yesu Khristu anaphunzitsa amaonetsera mfundo kapena choonadi chosiyanasiyana. Mitu ya mfundo zopezeka mu fanizo lililonse zatchulidwa pansipa. Werengani ma vesi amafanizo atchulidwa.

### **MAFANIZO OKHUDZA KUPEREKEDWA KWA UFUMU:**

**Fanizo lachigamba chophatikidwa:** Mateyu 9:16; Marko 2:21; Luka 5:36

**Matumba akale a vinyo:** Mateyu 9:17; Marko 2:22; Luka 5:37

Mafanizo awiri amenewa akuonetsera kuti Yesu anapereka Ufumu umene unali watsopano komanso osiyana kwambiri. Ufumu umenewu unali osiyana kwambiri ndi ndondomeko za chipembedzo chakale. Chifukwa chaichi, ndizosatheka kumvetsa ufumu umeneu ndi ndondomeko zachipembedzo chakale komanso makhalidwe ndi kaganizidwe ka chipembedzo chakale.

**M’busa wabwino: Yohane 10:1-16**

Mfumu Yesu imafananizidwa ndi m’busa. Iye amatsogolera nkhoa zake kuchoka mu ukapolo wachipembedzo ndikuwapatsa Ufulu wa Ufumu wake. Nkhosa zake zimamva mau ake ndikuchitapo kanthu pakuitanira kwake mu Ufumu wa Mulungu.

**Nkhosa yotaika:** Mateyu 18:12-14; Luka 15:4-7

**Ndalama yotaika:** Luka 15:8-10

**Mwana olowelera:** Luka 15:11-32

Mafanizo awa akuonetsera mmene Atate amafunira nkhoa zotaika kuti zikalowe mu Ufumu wa Mulungu, komanso mmene otsatira ake ayenera kufunira anthu otaika ndi kufunika kwa kulapa kuti munthu alowe Ufumu wa Mulungu.

**Fanizo laukwati:** Mateyu 22:1-14

**Fanizo la phwando lalikuru:** Luka 14:16-24

Mu mafanizo onsewa, Yesu akuitana m’bado walero kuti ukalowe mu Ufumu wa Mulungu. Uthenga oyamba unatumizidwa kwa Israeli ngati gulu la anthu osankhika a Mulungu. koma sionse osankidwao amene anavomera kuitana kumeneku. Chifukwa chaichi, anthu amitundu nao anapatsidwa mwayi oti alowe mu Ufumu wa Mulungu.

**Anthu awiri Omanga nyumba:** Mateyu 7:24-27

Mu fanizo limeneli, Yesu anaphunzitsa kuti maziko a Ufumu wa Mulungu ndi Iye mwini ndipo anadziyerekeza ndi thanthwe limene Munthu akhoza kumangapo moyo wake. Nyumba yomangidwa pa thanthwe lolimba imaimabe ngakhale mphepo yamphamvu imenye. Chimodzimidzi Yesu anapereka mwayi kwa anthu onse kuti amange moyo wao pamaziko amuyaya a Ufumu wa Mulungu.

**Zipata ziwiri:** Mateyu 7:13-14; Luka 13:24-28

Ndi chipata chimodzi chokha chomutengera munthu ku Ufumu wa Mulungu ndipo chipata chimenechi ndiye Yesu Khristu.

**MAFANIZO OKHUDZA KUKANIDWA KWA MFUMU:**

**Osungira munda akupha:** Mateyu 21:33-44; Marko 12:1-11; Luka 20:9-18

Yesu anagwiritsa ntchito mafanizo pofuna kuonetsa kuti iye adzakanidwa ndi Israeli ngati Mesiya komanso Mfumu. Ndipo izi zinaonetsedwa mu fanizo la osungira munda akupha. Mulungu anatumiza aneneri ku dziko lapansi ndi cholinga chofuna kupereka Ufumu wa Mulungu kwa Israeli, koma Israeli anapha aneneri amenewa. Komabe Mulungu anatumizanso mwana wake amene anaphedwanso ndikukanidwa.

**Mtengo wamkuyu osabara:** Luka 13:6-9

Mtengo wamkuyu umayimira mtundu wa ana Asraeli. Mulungu anadzutsa Israeli ndi cholinga choti akakuze Ufumu wake pa dziko lonse lapansi. Nthawi ndi nthawi Mulungu amayembekezera kuti Israeli abala zipatso pakati pa anthu amitundu pogawana nao chidziwitso cha Mulungu wao. Koma Israeli anakhala osabara zipatso.

**Ukwati:** Mateyu 22:2-14

Yesu Khristu anagwiritsanso ntchito fanizo la ukwati. Akapolo anatumidwa kuti ayitanire anthu ku ukwati umeneu. Koma anthu anapha akapolowa nakana kuitanidwako. Izi zinaonetsera mmene kuperekedwa kwa Ufumu wa Mulungu kunakanidwira.

**MAFANIZO OKHUDZA KUIMITSIDWA KWA UFUMU WA MULUNGU**

**Matalenti:** Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27

**Munthu wa paulendo wautali:** Marko 13:34-37

**Akapolo:** Mateyu 24:43-51; Luka 12:39-46

**Kapolo wochezera** Luka 12:36-38

Yesu anakamba mafanizo amene amaonetsa kuti Ufumu udzakhazikitsidwa komaliza mtsogolo. Ndipo ufumu sunakabwera nthawi imeneyo chifukwa Israeli anakana Yesu ngati mfumu yao. Mafanizo amanewa amaonetsa kuti pakadali pano, Yesu sakutengapo gawo mdera limene Ufumu omaliza udzakhazikitsidwe. Ndipo mafananizowa akutsindika kuti okhulupirira akhulupiririke ku ntchito imene apatsatsidwa pogwiritsa ntchito maluso ndi kuthekera kwao pofalitsa ufumu wa Mulungu.

**Mtengo wamkuyu:** Mateyu 24:32-34; Marko 13:28-30; Luka 21:29-32

Fanizo limeneli linaotsera nthawi imene Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwe. Iye anafotokoza kuti munthu akhoza kuzindikira kuti chilimwe chayandikira chifukwa chakuti mtengo wa mkuyu umameranso masamba. Tinafotokoza kale kuti mtengo wa Mkuyu ndi chitsanzo chimene chimayimira Israeli. Yesu amaulula kuti pamene Israeli adzabwezeretsedwe mu dziko lake ndikuyambanso kuchita bwino, ndiye kuti kubweranso kwa Mfumu kwayandikira (izi zachitika kale chifukwa Israeli anabwenzeretsedwa mu dziko lao.)

**MAFANIZO OKHUDZA KUKULA KWA UFUMU WA MULUNGU.**

Yesu anafotokoza mafanizo angapo amene anaonetsa kuti Ufumu wa Mulungu udzafalikira dziko lonse lapansi.

**Matalenti:** Mateyu 25:14-30; Luka 19:11-27

Fanizo limeneli limaonetsera kuti Ufumu wa Mulungu udzafalikira kudzera mukugwiritsa ntchito mphatso zauzimu ndi kuthekera kumene Mulungu wapereka kwa okhulurira.

**Ofesa:** Mateyu 13:3-8; Maliko 4:3-8; Luka 8:5-8

Uthenga wa ufumu wa Mulungu udzafalikira kudzera kufesa mbeu ya mau a Mulungu. Ndipo anthu osiyanasiyana adzachitsanso mosiyana pamene adzamva mau a Mulungu. Chipatsocho sichimatengera ofesayo, koma zimatengera moyo umene uli mu mbeuyo komanso chonde cha nthaka.

**Tirigu ndi nansongore:** Mateyu 13:24-30

Satana adzayesa kugonjetsa kufalikira kwa Ufumu wa Mulungu pofesa tchire pakati pa mbeu za Ufumu wa Mulungu. Ndipo nansongore amene Satana adzafese amafanana ndi tiligu. Koma nthawi yokolora tiligu ndi nansongole zidzalekanitsidwa.

**Ukonde:** Mateyu 13:47-50

Ufumu wa Mulungu umafanizidwa ndi ukonde waukulu oponyedwa mu nyanja. Nsomba zamitundu yosiyanasiyana zimakodwa koma pamapeto pake somba zabwino ndi zoipa zimalekanitsidwa. Chimodzimodzi, ufumu wa Mulungu ukuitanira anthu onse a dziko lapansi, koma pachimaliziro cha nthawi, padzakhala chiweruzo pofuna kuona iwo amene sayenera kulowa Ufumu wa Mulungu.

**Mbeu ya mpiru:** Mateyu 13:31-32; Maliko 4:31-32; Luka 13:19

Ufumu wa Mulungu udzakula ngati mbeu ya mpiru. Kambewuka ndi kakang'ono kwambiri, koma kamakula modabwitsa.

**Chotupitsa:** Mateyu 13:33; Luka 13:21

Ngati mmene chotupitsa chifalikira mu mkate, chimodzimodzinso ufumu wa Mulungu udzafalikira pa dziko lapansi. Mphamvu ya Ufumu umeneu ndi yoonekera mkati osati kunjira.

### **MAFANIZO ACHIWERUZO MU UFUMU:**

**Anamwari khumi:** Mateyu 25:1-12

**Nkhosa ndi mbuzi:** Mateyu 25:31-46

Yesu anafotokoza mafanizo angapo okhudza chiweruzo chamtsogolo mu Ufumu wa Mulungu. pa nthawi yachiweruzo, onse amene ndi nkhosa za m'busa weniweni amene ali Yesu adzaloledwa. Ndipo ena onse adzathamangitsidwa mu Ufumu wa Mulungu.

### **MAFANIZO OWONETSERA MTENGO WAKE WA UFUMU WA MULUNGU.**

Yesu khristu anagwiritsa ntchito mafanizo angapo pofuna kuonetsera kuti Ufumu wa Mulungu ndi wapamwamba kapena kuti uli ndi mtengo wake wapamwamba. Ena mwa mafanizo amenewa ndi awa.

**Ngale zabwino:** Mateyu 13:45-46

**Chuma chobisika:** Mateyu 13:44

Mafanizo amenewa amaonetsera kuti Ufumu wa Mulungu ndi wapamwamba kotere kuti palibe chithu chimene tingafananize. Ndi wapamwamba kuposa chili chonse chimene munthu akhoza kukhala nacho. Ichi ndi chifukwa chake munthu akhoza kutaya zinthu zonse zimene ali nazo ndi cholinga choti apeze Ufumu wa Mulungu poti ndi wantengo wapamwamba.



**Mwina banja:** Mateyu 13:52

Mu fanizio limeli, yesu anadzifananiza ndi mwini nyumba amene amakhala akubweretsa katundu ofunika m'nyumbamo. Iye amatha kubweretsa vinyo wakale kapena watsopano. Mwini ndi amene amakahala ndi ulamuliro pa zinthu. Malingana ndi zinthu zimene amakhala akubweretsa, zosowa za panyumbapo zimapezeka. Mumadera ena, ufumu wa Mulungu umene Yesu Khristu anabweretsan unali ofanana ndi wakale uja. Komanso mu magawo ena, Ufumu uemeneu unali watsopano. Chifukwa cha izi, zinthu zina zakale ndi zatsopano zinali zofunikira kwa mzika za Ufumu wa Mulungu.

### **MAFANIZO OKHUDZA MOYO MU UFUMU WA MULUNGU:**

Mafanizo ambiri a Yesu Khristu amaonetsera mfundo za Ufumu wa Mulungu.

**Ana amuna awiri:** Mateyu 21:28-32

Yesu khristu anaphunzitsa kuti kumvera ndiye chizindikiro chokhala mwana mu Ufumu wa Mulungu.

**Msamariya wachifundo:** Luka 10:30-37

Mfundo ya chikondi ikuphunzitsidwa kwa anthu onse mu fanizo limeneli. M'nansi ndi wina aliyenense amene ali ndi chosowa. Chosowa chimene tikuchidziwa ndipo tikhoza kukwanitsa kuthandiza.

**Angongore awiri:** Luka 7:41-43

Fanizo ili limaonetsa kuti chikondi chimaonetsedwa ndi amene wakumana ndi chikondi cha Ufumu wa Mulungu.

**Wamisonkho ndi mfarisi** Luka 18:10-14

Mfarisi anafika pamaso pa Mulungu ndi chiyero chake chomwe kapena kuti anadzilungamitsa yekha. Pamene wamisonkho anazindikira kuti panalibe chabwino mwa iye yekha chimene anakatha kuima nacho pamaso pa Mulungu. Mu fanizo limeneli, Yesu akuphunzitsa mmene tiyenera kufikira pamaso pa Mulungu; tiyenera kukhala odzichepetsa pa maso ma Mulungu pamene tipemphera ndipo fanizo ili limachenjezi kuti sitiyenera kudzilungamitsa tokha.

**Mzimayi wamasiye okakamira:** Luka 18:1-8

**Bwenzi lokakamira:** Luka 11:5-10

Mafanizo awiri amenewa akuphunzitsa kufunika kokakamira mupemphero.

**Kapitao okhulupirika: Mateyu 25:14-30**

Fanizo ili limatsindika kufunika kokhaa ndi umwini pa chuma cha Ufumu chimene Mulungu watidalira nacho ife okhulupirira.

**Fanizo la mipando ya ulemu: Luka 14:7-11**

Fanizo limeli limatsindika kufunika kodzichepetsa ndipo limawonetsera kuti kukwezedwa mu Ufumu wa Mulungu kumachokera kwa Mulungu.

**Mphesa ndi thambi zake Yohane 15:1-6**

Fanizo limeli limafotokoza ubwenzi wa Yesu ndi mpingo.

**Antchito m'munda: Mateyu 20:1-16**

Fanizo il limaonetsa kuti mphoto zakumwamba sizimaperekedwa malinga ndi mfundo za dziko lapansi.

**Kutumikira: Luka 17:7-10**

Fanizo ili limaphunzitsa kuti ndi Udindo wathu kuti titumikire ndikuchita zinthu zimene Yesu khristu walamulira.

**Kupita kunkhondo: Luka 14:31-33**

**Womanga nsanja: Luka 14:28-30**

Mafanizo awiriwa amatsindika kufunika kokhala ndi kumvetsetsa ndi kudzipereka mu Ufumu wa Mulungu.

**Chovala chaukwati: Mateyu 22:10-14**

Fanizo limeneli limatsindika kufunika kovala chiyero kapena chilungamo kuti tikhalebe mu Ufumu. Ndipo tikhoza kukwanitsa izi mwa Yesu yekha osati kudziletsa tokha.

**Zoganiza za munthu wachuma: Luka 12:16-21**

Fanizo limeneli limatsindika kupusa kodalira chuma chapadziko. Chinthu chofunika kwambiri ndiye ufumu wa Mulungu.

**Chitsotso ndi mtanda:** Mateyu7:1-5; Luka 6:41-42

Fanizo limeneli limaphunzitsa kuti tiyenera kudziweruza tokha osati anthu ena.

**Kholora Mateyu** 9:37-38; Luka 10:2

Iyi ndi nkhani ya kholora, imene ikuonetsa kuti kholora lacha ndipo liyenera kututidwa. Yesu anagwiritsa ntchito nkhani imeneyi pofuna kutsindika kwa ophunzira ake kufunika kokuza Ufumu wa Mulungu. Ndipo awa anali masomphenya opezeka mu nkhani imeneyi amene anasintha “asodzi asomba ndi kukhala asodzi a anthu”

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yoloweza osaonera

---

---

---

2. Kodi fanizo ndi chiani?

---

---

---

3. Ndi chifukwa chiani Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo pofuna kuphunzitsa choonadi cha Ufumu wa Mulungu?

---

---

---

4. Kodi mutu waukulu mu mafanizo unali chiani?

---

---

**(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)**

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Buku lachibvumbulutso monga mwa dzina lake limavumbulutsa zinthu zimene sizimadziwika ndi kale lomwe. Mulungu anaululira Yohane za zinthu zimene zidzachitike mtsogolo ndipo izi ndi zinthu zimene Yohane sakanizidziwa ndi nzeru zakuthupi. Pamene Mulungu amabvumbulutsa zinthu zimenezi, Iye anazilemba mu buku la Chibvumbulutso.

Mavumbulutso amenewa ndi okhudza zinthu zimene ziyenera kuchitika chimaliziro cha dziko lapansi chisanachitike. Ngati mafanizo, buku la Chibvumbulutso ndi lovuta kulimvetsa ndi maganizo a umunthu. Bukuli liyenera kuwerengedwa ndi maganizo auzimu.

Buku la Chibvumbulutso limaonetsera zambiri zokhudza Ufumu wa Mulungu wa mtsogolo:

1. Werengani ndime izi zokhudza Ufumu wa Mulungu mu buku la Chibvumbulutso: 1:9; 11:15; 12:10
2. Ndime izi zimafotokoza za maufumu a dziko lapansi a Satana: 16:10; 17:17
3. Pa Chibvumbulutso 20:10-15 amaonetsera mathero a Satana ndi mzika zonse za ufumu wake.
4. Fotokozerani mwachidule zimene mwawerengazi zokhudza chiphunzitsa cha Ufumu wa Mulungu.

---

---

---

---

---

---

---

---

## CHAPUTALA 11

### AKAZEMBE A UFUMU WA MULUNGU.

#### ZOLINGA

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la Kazembe.
- Kufotokoza tanthauzo la “mboni”
- Kufotokoza kufunika kofalitsa Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)**

#### MAU OYAMBA

Muphunziro ili, mwaphunzira zokhudza Ufumu wa Mulungu. Taona zokhudza maufumu auzimu wa Satana komanso wa Mulungu. Kale la Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa Mulungu mtsogolo zakambidwanso. Pamene tafikapa, mwapatsidwa zifungulo za Ufumu wa Mulungu ndi kuchenjezedwa pa zinthu zolepheretsa kulowa ufumu wa Mulungu.

Mu chaputala ichi, mupatsidwa ntchito yapadera yoti muchite ndipo ntchitoyi imatenge moyo wanu onse kuti muyimalize. Mutumizidwa ngati akazembe a ufumu wa Mulungu.

#### CHOLINGA CHA YESU

Yesu anabwera pa dziko lapansi ndi cholinga chofuna kukhazikitsa Ufumu wa Mulungu:

**Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino. (Marko 1:14-15)**

**Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 4:17)**

kudzipereka kwa Yesu khristu ku Ufumu wa Mulungu kunali koonekeratu mu Utumiki wake:

**Koma anati kwa iwo, Kundiyenera Ine ndilalikire Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ku midzi yinanso: cifukwa ndinatmidwa kudzatero. (Luka 4:43)**

Atafa ndi kuukitsidwa, Iye anakahalabe pa dziko lapansi mwakanthawi kochepe ndipo anaonekera kwa anthu ambiri. Uthenga wake sunasithe chifukwa iye anatsindikabe kwambiri za Ufumu wa Mulungu.

**kwa iwonso anadzionetsera yekha wamoyo ndi zitsimikizo zambiri, zitatha zowawa zace, naonekera kwa iwo masiku makumi anai, ndi kunena zinthu za Ufumuwa Mulungu; (Macitidwe 1:3)**

Yesu anayamba utumiki wake ndi kulalika uthenga wa Ufumu wa Mulungu (Mateyu 4:17) ndipo anamalizanso utumiki wake polakhula zokhudzana Ufumu wa Mulungu (Machitidwe 1:3). chapakatikati pa utumiki wake, Iye anakamba kwambiri za kukuza Ufumu wa Mulungu.

### **KUTUMIDWA KWAKUKULU**

Angakhale Yesu Khristu asanafe, anawakonzekeretsa ophunzira ake kuti apitirizebe kukuza ufumu wa Mulungu. Pachiyambi, iwo anakonzekeretsedwa kafalitsidwe ka uthenga wa Ufumu wa Mulungu:

**Ndipo kunali, katapita kamphindi anayendayenda kumizinda ndi kumidzi, kulalikira ndi kuwauza Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu, ndi pamodzi naye khumi ndi awiriwo, (Luka 8:1)**

Yesu anawakonzekeretsa ophunzira ake powapatsa mwayi oti etengepo gawo. Iye anali kuwatumiza madera osiyanasiyana ndi cholinga choti:

**Ndipo anawatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuciritsa anthu odwala. (Luka 9:2)**

Pamapeto pake, Iye anawatuma ndikuwapatsa udindo oti akuze Ufumu wa Mulungu ku maiko onse a dziko lapansi:

**Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano. (Mateyu 28:18-20)**

**Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)**

## AKAZEMBE A UFUMU

Yesu asanabwelere kumwamba, Iye anauza otsatira ake kuti:

**Ndipo Ine ndikuikirani ufumu, monganso Atate wanga anandiikira Ine, kuti mukadye ndi kumwa kugome kwanga mu Ufumu wanga; (Luka 22:29)**

Ufumu unaperekedwa ndi Yesu kwa ophunzira ake. Ife tili ndi mwai wa ukulu lero lino kukhala mbali imodzi ya Ufumu umeneu. Koma Mulungu anatisankha ife ndi cholinga. Yesu anatisiyira udindo oti tikuze Ufumu wa Mulungu pa dziko lapansi. Tikuyenera kukhala akazembe a Ufumu pa dziko lapansi.

Kazembe ndi nthumwi yotumizidwa ndi mfumu kuti ikayimire Ufumu ku dziko lina. Iye amakhala wanthenga wa ufumu umene akuyimira. Paulo analakhula:

**Cifukwa cace tiri atumiki m'malo mwa Kristu, (2 Akorinto 5:20)**

Ndife akazembe otumizidwa ndi Mfumu ku maufumu a dziko lapansi. Ndipo ntchito imene tapatsidwa ngati akezembe ndi ya moyo wathu onse kotere kuti pamene tavomera kutumidwa kumeneku, sitingayang' anenso mbuyo.

**Koma Yesu anati kwa iye, Palibe munthu wakugwira cikhasu, nayang'ana za kumbuyo, ayenera Ufumu wa Mulungu. (Luka 9:62)**

## NDIFE MBONI

Ngati akazembe, ndife mboni zaufumu wa Mulungu. Mbomi ndi munthu amane amatha kuchitira umboni pazimene iye anazona ndi maso. Kapena kuti ndi munthu amene anaona kapena kukumana nazo zinthu. Yesu ananena kwa ophunzira ake nati:

**Ndipo inunso mucita umboni, pakuti muli ndi Ine kuyambira ciyambi. (Yohane 15:27)**

Umboni wa akazembe a Ufumu wa Mulungu cholinga chake ndi kukuza Ufumu wa Mulungu pa dziko lonse lapansi.

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)**

Uthenga wa mboni umayenera kukhala:



**Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacidatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. Inu ndinu mboni za izi. (Luka 24:46-48)**

Pamene ophunzira anatuluka kukachitira umboni, Mulungu naye amawachitira umboni.

**pocita umboni pamodzi nao Mulungunso ndi zizindikilo, ndi zozizwitsa ndi mphamvu za mitundu mitundu ndi zogawira za Mzimu Woyera, monga mwa cifuniro cace. (Aheberi 2:4)**

Ndife akazembe a Ufumu wa Mulungu, ochitira Umboni uthenga wa Ufumu wa Mulungu. Ndipo Mulungu amachitira umboni kutumikira kwathu kudzera mukuonetsera kwa mphamvu yake.

### **UDINDO OFUNIKIRA**

Ndi chifukwa chiani uli udindo wathu kukuza Ufumu wa Mulungu?

Chifukwa chake ndi chakuti Yesu anati:

**Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)**

kukhazikitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu komaliza sikudzachitika pokhapokha uthenga utalalikiidwa dziko lonse lapansi. Ndipo muyenera kuzindikira kuti uthenga umeneu si uthenga wamba koma ndi uthenga wa Ufumu wa Mulungu. Paulo akufotokozerza za Ufumu wa Mulungu:

**Ndipo ndikudziwitsani, abale, Uthenga Wabwino umene ndinakulalikirani inu, umenenso munalandira, umenenso muimamo, umenenso mupulumutsidwa nao ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikirira kwa inu; ngati simunakhulupira cabe. Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa pa tsiku lacidatu, monga mwa malembo; (1 Akorinto 15:1-4)**

Uthenga Wabwino ndi wakuti Yesu anafera machimo athu, anaikidwa mmanda, nauka kwakufa. Izi ndi malinga ndi mau a Mulungu.

### **KUFALITSA UFUMU**

Ndondomeko za kufalitsa Uthenga Wabwino zinaperekedwa ndi Yesu. Uthenga wa Ufumu wa Mulungu uyenera kuitanira anthu kuti alape machimo ao:

**Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino. (Maliko 1:14-15)**

**Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 4:17)**

Uthenga wa Ufumu uyenera kufalitsidwa polalika ndi kuphunzitsa komwe:

**Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)**

Yesu anauza ophunzira ake:

**Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 10:7)**

Uthenga wa Ufumu wa Mulungu sikungolalika mau okha ayi. Koma pamakhalanso kuonetsera mphamvu ya Mulungu. Izi zinaonekera mu chitsanzo chimene Yesu Khristu anakhazikitsa:

**Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:35)**

**Koma unyinji wa anthu, pamene anadziwa, anamtsata Iye; ndipo iye anawalandira, nalankhula nao za Ufumu wa Mulungu, naciritsa amene anasowa kuciritsidwa. (Luka 9:11)**

**Ndipo ciritsani odwala ali momwemo nimunene nao, Ufumu wa Mulungu wayandikira kwa inu. Koma ku mudzi uli wonse mukalowako, (Luka 10:9)**

**Ndipo anawatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuciritsa anthu odwala (Luka 9:2.)**

Kuonetsera kwa mphamvu, zozizwa ndi machilitso zimaonetsera Ufumu wa Mulungu. Paulo anati:

**Pakuti ufumu wa Mulungu suli m'mau, koma mumphamvu, Mufuna ciani? (1 Akorinto 4:20)**

## **KUKWANILITSA KUTUMIDA KWAKUKULU**

Mtumwi Paulo, Kazembe wamkulu wa Ufumu wa Mulungu anayakhula izi:

**Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)**

Mpingo oyamba unakwanilita kutumidwa kokuza Ufumu wa Mulungu osati pakungolalakira kokha kapena kuphunzitsa. Koma anali kuonetsera mphamvu ya Ufumu. Ufumu sunafalikire ndi anthu ophunzira bwino mu maphunziro a zauzimu kapena kudzera mukumanga nyumba zikuluzikulu.

Kukuza Ufumu wa Mulungu linali gawo lofunika mu utumiki wa Mpingo oyamba. Posatengera mazuzo amene anakumana nawo, iwo anapitilizabe udindo wao ngati akazembe otumidwa a Ufumu wa Mulungu.

**Ndipo tsikulo kunayamba kuzunza kwakukuru pa Mpingo unali m'Yerusalemu; ndipo anabalalitsidwa onse m'maiko a Yudeya ndi samariya, koma osati atumwi ai. (Macitidwe 8:1)**

Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapita nalalikira mauwo.

Gawo limodzi la ndondomeko zokhazikitsa mipingo linali logwirizana ndi Ufumu wa Mulungu:

**Pamene analalikira Uthenga Wabwino pamudzipo, nayesa ambiri akuphunzira, anabwera ku Lustra ndi Ikoniyo ndi Antiokeya, nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandaulira iwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri. (Macitidwe 14:21-22)**

Angakhale anthu wamba nao a mumpingo anakangalika ndi kulalika uthenga Wabwino.

**Koma pamene anakhulupirira Filipo wakulalikira Uthenga Wabwinowa Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Kristu, anabatizidwa, amuna ndi akazi. (Macitidwe 8:12)**

Naonso atsogoleri chidwi chao chachikulu chinali pa Ufumu wa Mulungu:

**Ndipo iye analowa m'sunagoge, nanena molimba mtima, miyezi itatu, natsutsana ndi kukopa kunena za Ufumu wa Mulungu. (Macitidwe 19:8)**

Utumiki wa Paulo nao unakhazikika pa Kulalika za ufumu wa Mulungu. Chakumapeto a utumiki wake Paulo anauza okhulupirira kuti:

**Ndipo tsopano, taonani, ndidziwa ine kuti inu nonse amene ndinapitapita mwa inu kulalikira ufumuwo, simudzaonanso nkhope yanga (Macitidwe 20:25).**

Ngakhale kuti Paulo anali wandende ku Roma, komabe iye anapitirizabe kufalitsa wa Ufumu wa Mulungu.

**Ndi kulalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Kristu ndi kulimbika konse, wosamletsa munthu. (Macitidwe 28:31)**

## KUMANGA UFUMU WA MULUNGU

Mpingo wa makono wayiwala zakumanga Ufumu wa Mulungu. Nthawi zambiri chidwi chathu chili pakumanga makachisi okongora komanso mpingo okhala ndi anthu ambiri. Pali kutsindikwa kwakulu utumiki wakumanga zipatala, masukulu komanso nyumba za ana amasiye.

Ngakhale kuti zinthu izi ndi gawo limodzi la utumiki wampingo, koma sizikuyenera kukhala patsogolo. Kupeza ndalama kapena kumanga simayitanidwe athu. Zotsatira za zinthu izi zikhoza kukhala kumanga ma ufumu athu osati kukuza Ufumu wa Mulungu pa dziko lonse lapansi.

Paulo anachenjeza za izi:

### **Pakuti onsewa atsata za iwo okha, si za Yesu Kristu. (Afilipi 2:21)**

Madongosolo onse a zomangamanga a utumiki pa mpingo ayenera kuunguzidwa bwino pogwiritsa ntchio funso ili: *kodi izi zithandiza bwanji kukwanilitsa kutumidwa koti tifaritse Ufumu wa Mulungu?* Nthawi zambiri timalalika ndi kuphunzitsa zinthu monga ngati: ukwati ndi banja komanso uneneli. Mitu yonse ndi yabwino imene ikufunika mu nthawi yathu lero lino. Koma uthenga uli onse olalikidwa uyenera kuunikidwanso ndi funso ili: kodi uthenga umeneu ukufotokozera bwanji za mfundo za Ufumu wa Mulungu?

Muyenera kudzifunsa mafunso awa...

- Kodi padutsa nthawi yaitali bwanji musanamve uthenga wa Ufumu wa Mulungu?
- Kodi mpingo ukukwanilitsa bwanji kukuza Ufumu wa Mulungu?
- Kodi mukutengapo gawo lanji pokwanilitsa gawo lanu ngati Kazembe wa Ufumu wa Mulungu.

Yesu khristu anaphunzitsa kuti mapemphero athu ayenera kulunjika pa Ufumu wa Mulungu. Tiyenera kupemphera kuti:

### **Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco panso pano. (Mateyu 6:10)**

Chinthu choyambilira kufunafuna m'moyo wathu chiyenera kukhala Ufumu wa Mulungu.

### **Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)**

### **Komatu tafuna-funani Ufumu wace, ndipo izi adzakuonjezerani. (Luka 12:31)**

mpingo unakhazikitsidwa ndi Mulungu ndi cholinga choti ukakhale chida chofalitsira kapena kukuza Ufumu wake ku maiko onse a dziko lapansi. Koma mipingo yambiri yataya maso mphenya akuitanidwa kumeneku. Iwo chidwi chao chili pakukuza nambala ya anthu ao malo moti amange Ufumu wa Mulungu.

komanso mpikisano pakati pa mipingo, azibusa waononga umodzi mumpingo wa Khristu Yesu. Tataya masomphenya a Ufumu umodzi wa Mulungu umene mpingo uli onse ndi mbali imodzi ya Ufumu umeneu. Mmallo mothandizana wina ndi mzake pa utumiki ofalitsa Ufumu wa Mulungu, tili pa mpikisano omanga nyumba zikuluzikulu, kukhala ndi anthu ambiri mumpingo wathu, komanso kutolera ndalama zambiri ndi cholinga choti timange maufumu athu.

Dongosolo la Mulungu ndi lakuti mpingo usangolalika za Ufumu wa Mulungu, koma tiyenera kukhala chitsanzo cha Ufumu wa Mulungu. Kodi ife tikukwaniritsa zimenezi?

Mpingo uyenera kuzindikira udindo wake weniweni osati kungokuza nambala ya athu ake. Mpingo uyenera kudzipereka kwanthunthu osati pongomanga nyumba zopemphelelamo zokha. Chinthu choyamba ndi chakuti mpingo uyenera kufunafuna kaye Ufumu wa Mulungu ndipo zinthu zina zonse zidzatitsata ngati mpingo.

### **CHITSANZO CHA CHIPANGANO CHAKALE**

Kutumidwa koyamba kwa munthu kunali kuti abalane ndikulidzadza dziko lapansi (Genesis 1:28) Kutsindika kwenikweni kunali pa anthu ndipo cholinga chenicheni chinali chakuti dziko lapansi lidzale ndi amayi ndi abambo olengengedwa muchifanizo cha Mulungu komanso okhala ndi ubale ndi Mulungu. koma tikuona kuti cholinga chimenechi chinasinthidwa ndi munthu. Werengani ndime ya Genesis 11:1-9.

Cholinga cha anthu amenewa chinali kumanga mzinda ndi nsanja yaikulu osati kubalana. Ntchito za zomangamanga ndi zimene zinatenga gawo lalikulu. Zokhumba zao zinali za iwo okha; kuti akatchukitse dzina lao ndikubweretsa anthu ambiri pamodzi.

Mulungu anabwera kudzaona ntchito imene imachitika pa nsanja ya Babulo ndipo iye sanauze anthu kuti angwire ntchito imeneyi. Izi ndi zimene zikuchitika ndi mipingo yathu yambiri lero lino. Tayiwala kutumidwa kwakulu ndipo tatanganidwa ndi kumanga nsanja zikulu zikulu za mipingo yathu. Koma kodi ndi chiani chimene Mulungu angalakhule atoana zimene tikumanga?

Anthu aku Sinara anati tiyeni “timange mzinda.” Pali kusiyana pakati pa mzinda omangidwa ndi Mulungu ndi omangidwa ndi anthu. Anthu amenewa amamanga kuti akwaniritse zofuna zao osati za Mulungu.

Mulungu anachitapo kanthu nasokoneza chilankhulo chao:

**Tiyeni, titsike, pomwepo tisokoneze cinenedwe cao, kuti wina asamvere cinenedwe ca mnzace. Ndipo Yehova anabalalitsa iwo pa dziko lonse lapansi, ndipo analeka kumanga mudzi. Cifukwa cace anacha dzina lace Babele; pakuti kumeneko Yehova anasokoneza cinenedwe ca dziko lonse lapansi; kuyambira pamenepo Yehova anabalalitsa iwo pa dziko lonse lapansi. (Genesis 11:7-9)**

Chifukwa chakuti wina aliyense amayankhula chinenero chake, kumanga kwao kunathera panjira.

## **CHITSANZO CHA CHIPANGANO CHATSOPANO**

Yesu anatuma mpingo oyambirira kuti ukapange ophunzira ake pa dziko lapansi, osati kuti akamange kachisi wamkulu wa ku Yerusalemu. Koma tikupeza kuti mpingo unakula kwambiri kotere kuti panali zinthu zina zovuta mukayendetsedwe ka zinthu. (Machitidwe 6). Iwo anali kupanga ophunzira ambiri mu Yerusalemu osati kupita kudziko lapansi ngati mmene Yesu anawalamulira. Chifukwa cha ichi, Mulungu analora chizuzo pakati pao ndipo iwo anamwazikana.

**... Ndipo tsikulo kunayamba kuzunza kwakukuru pa Mpingo unali m'Yerusalemu; ndipo anabalalitsidwa onse m'maiko a Yudeya ndi samariya, koma osati atumwi ai (Macitidwe 8:1)**

Chifukwa cha mazuzo, iwo anabwela ku dongosolo lapoyamba loti akhale akazembe a Ufumu wa Mulungu.

Pamene mipingo yaikulu yatha, anthu ake a Mulungu amapitilirabe. Ufumu wa Mulungu sungafalikire pa dziko lapansi kudzera mukumanga makachisi akuluakulu. Ufumu umafalikira kapena udzafalikira ndi akazembe ochitira umboni za uthenga wa Ufumu ndi kupanga ophunzira.

Mu chaputala changopitachi, “Mfundo za Ufumu,” tinafotokoza mmene Ufumu udzafalikire pa dziko lonse lapansi. Mafanizo a Matalenti Luka 19 ndi Mateyu 25 aonetsera kuti Ufumu wa Mulungu udzafalikira pogwiritsa ntchito mwanzeru mphatso zauzimu komanso kuthekera kumene tili nako.

Fanizo la chotupitsa (Mateyu 13:33) limaonetsera kuti ufumu wa Mulungu chiyambi chake chidzakhala chaching’ono, koma ngati chotupitsa mu mkate udzakhala ukufalikirabe mosalekeza. Fanizo la ukonde oponyedwa munyanja limaonetsera kuti Ufumu wa Mulungu udzabweretsa anthu amitundu yonse pamodzi.

Ufumu umafalikiranso pamene anthu afesa mbeu mumitima ya amayi ndi abambo. Ngati mbeu yakuthupi, chimodzimodzinso Ufumu wa Mulungu umakula, ngakhale kuti kukula kwake sikungamvetsetseke ndi iwo amene akufesa mbeuyo (Marko 4: 26-27).





## UFUMU WANU UDZE

Idzafika nthawi imene Ufumu wa Mulungu udzakhazikitsidwa komaliza ndipo ufumu wa Satana udzagonjetsedwa:

**Ndipo ndinamva mau akulu m'Mwamba, nanena, Tsopano zafika cipulumutso, ndi mphamvu, ndi ufumu wa Mulungu wathu, ndi ulamuliro wa Kristu wace; pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku. (Cibvumbulutso 12:10)**

**Pomwepo pali cimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera ciweruzo conse, ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe. (1 Akorinto 15:24)**

**Ndipo mngelo wacisanu ndi ciwiri anaomba, ndipo panakhala mau akulu m'Mwamba, ndi kunena, Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Kristu wace: ndipo adzacita ufumu kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 11:15)**

**Ndipo iye adzacita ufumu pa banja la Yakobo ku nthawi zonse; ndipo ufumu wace sudzatha. (Luka 1:33)**

Kufikira nthawi imeneyi, tikhoza kulandira lonjezano limeneli.

**Ambuye adzandilanditsa ku nchito yonse yoipa, nadzandipulumutsa ine kulowa Ufumu wace wa Kumwamba; kwa iye ukhale ulemerero ku nthawi za nthawi. Amen. (2 Timoteyo 4:18)**

Pemphero lathu ndi lakuti...

**kuti muyende koyenera Mulungu, amene akuitanani inu mulowe ufumu wace wa iye yekha, ndi ulemerero. (1 Atesalonika 2:12)**

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

---

2. Kodi mau oti Kazembe amanthauza chiani?

---

---

3. Kodi tanthauzo la mau oti mboni ndi chiani?

---

---

4. Paulo anati kulalika kwake si kwa mau okha kodi china chimene chimayendera limodzi ndi mau ndi chiani?

---

---

5. Ndi chifukwa chiani kufalitsa Ufumu wa Mulungu kuli udindo ofunika kwambiri?

---

---

6. Kodi mutu waukulu wa utumiki wa Yesu unali chiani?

---

---

**(mayankho amafunso amenewa ali kumapeto kwa buku limeneli)**

## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

Kuchokera makuku a Machitidwe mpaka buku la Yuda mu Chipangano chatsopano amaonetsera zimene okhulupirira oyamba anachita pamene anazindikira kuitanidwa kwao ngati akazembe. Werengani ndime zili munsimu kuti muone mmene izi zinakwanilitsidwira:

Machitidwe 1:3,6,9-11; 8:12; 14:22; 19:8 20:25; 28:23,31

Aroma 14:17

I Akorinto 4:20; 6:9-10; 15:24,50

Agalatiya 5:19-21

Aefeso 5:5

Akolose 1:13; 4:11

I Atesalasonika 2:12

II Atesalonika 1:5

I Timoteyo 6:15; 17:14; 19:16

II Timoteyo 4:1,18

Aheberi 1:8; 11:33; 12:28

Yakobo 2:5

II Petulo 1:11

## MAYANKHO AMAYESO ODZOFUSA NOKHA

### CHAPUTALA 1

1. Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni.
2. Kwa anthu mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. Mateyu 24:14
3. Kuti muone magawo azinthu zakuthupi kapena zauzimu werengani I Akorinto 24: 14)
4. Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa Satana.
5. Satana amalamulira Ufumu wa Satana ndipo Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera amalamulira Ufumu wa Mulungu.
6. Mzika za Ufumu wa Satana ndi Satana, ziwanda ndi anthu onse amane samvera Mulungu.
7. Mzika za Ufumu wa Mulungu ndi Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera ndi anthu onse amene okhala moyo wangwiro ndi kumvera Mulungu.
8. Ufumu ndi malo ndi anthu olamulidwa ndi mfumu.

### CHAPUTALA 2

1. Ndipo iye adzacita ufumu pa banja la Yakobo ku nthawi zonse; ndipo ufumu wace sudzatha. Luka 1:33
2. Mfumu ndi olamula wa mphamvu wa fuko, dziko kapena mtundu wa anthu. Mau oti “wamphamvu” kuti iye ali ndi mphamvu zonse, ulamuliro onse komanso sangalamulidwe ndi wina aliyense.
3. Yesu.
4. Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane.

### CHAPUTALA 3

1. Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi: Mateyu 25:34
2. Mufananitse kufotokera kwanu mwachidule ndi kufotokozedwa kwa Ufumu wa Mulungu mu mbiri yakale.
3. Mufananitse kufotokoza kwanu mwachidule ndikufotokozeledwa kwa Ufumu wa Mulungu lero lino mu chaputala 3.
4. Mufananitse kufotokoza kwanu machidule ndi kufotokozeredwa kwa Ufumu wa Mulungu mtsogolo mu chaputala 3.
5. Onani mfundo zazikulu za Ufumu wa Mulungu mu chaputala 3.

### CHAPUTAL 4.

1. Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. Mateyu 16:19
2. Mpingo
3. Izi ndi mphamvu zauzumu zakumanga mphamvu zoipa, komanso kumasula mphamvu ya umulungu, ndikutsegula makomo okuza Ufumu wa Mulungu.
4. Kulapa machimon ndikubadwanso mwatsopano.
5. Kubadwanso mwauzimu ndi mwatsopano.
6. Pamene tabwadwanso mwatsopano kudzera muchikhulupiriro, tiyenera kukulabe muuzimu kuti tikalowe Ufumu wa Mulungu.
7. Kumanga chinthu kumatanthauza kuli ngati kutseka chipinda ndi zifunguro.
8. Kumasula chinthu kuli ngati kupereka Ufulu kapena kutsekula chitseko cha muchipinda.

## CHAPUTAAL 5

1. Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. Mateyu 7:21
2. I Akorinto 6:9-10 ndi Agalatiya 5:19-21.
3. a. Zabodza b. zolondora. c Zolondora. d. Zolondora e. Zolondora. f. Zabodza. g. Zolondora.
4. I Yohane 1:8-9.

a.	2	m.	23
b.	5	n.	18
c.	9	o.	19
d.	11	p.	20
e.	6	q.	16
f.	10	r.	21
g.	12	s.	22
h.	7	t.	17
i.	3	u.	3
j.	14	v.	4

## CHAPUTALA 6

1. Mbiri 28:19 Conseci, anati Davide, anandidziwitsa ndi kucilemba kucokera kwa dzanja la Yehova; ndizo nchito zonse za cifaniziro ici.
2. Ndongomeko ndi chinthu choyamba chimene chimagwiritsidwa ntchito ngati chitsanzo chopangira zinthu zina. Kapena kuti ndi chinthu chimene chimapangidwa ndi cholinga choti achitengere.
3. Mfundo ndi ndongomeko kapena lamulo la kachitidwe ka zinthu. Ndi choonadi chachikulu chimene chimakhala ndi mfundo zina zing'onozing'ono.
4. Ndongomeko za Baibulo ndi chitsanzo chimene chimaperekedwa mu Baibulo kuti ena achitsate
5. Mfundo ya Baibulo ndi choonadi chauzimu mu Baibulo chimene chimakhala ndi mfundo zina zothandizira.

## CHAPUTALA 7

1. Ndipo Ine ndikuikirani ufumu, monganso Atate wanga anandiikira Ine, kuti mukadye ndi kumwa kugome kwanga mu Ufumu wanga; (Luka 22:29)
2. Chilungamo.
3. Choyamba ndiye kukonda Mulungu, chachiwiri kukondananso ndi wina ngati mmene mudzikondera inu mwini.
4. - muyenera kugwiritsa ntchito mfundo zimenezi kuti mupitilire kukhala mzika zaufumu.

-Yesu anati ndi zofunika.

-Zipatso za Ufumu wa Mulungu zimaonetsera umboni wa Umzika.

-Kuti mulamulire mu Ufumu muyenera kudziwa mfundo za Ufumu.

5. a. 2 d. 3

b. 1 e. 5

c. 4 f. 6

## CHAPUTALA 8

1. Mverani, abale anga okonedwa; kodi Mulungu sanasankha osauka a dziko lapansi akhale olemera ndi cikhulupiriro, ndi olowa nyumba a ufumu umene adaulonieza kwa iwo akumkonda iye? (Yakobo 2:5)
2. Onani mfundo zopezeka mu chaputala ichi:

- |                |                |                    |
|----------------|----------------|--------------------|
| a. Chuma       | j. Kukwezedwa  | s.                 |
| b. Chimwemwe   | k. Wamkulu     | t. Kulandira       |
| c. Kugonjetsa  | l. Oyamba      | u. Zotheka         |
| d. Kukhutsidwa | m. Wamkulu     | v. Kuona           |
| e. Chifundo    | n. Zonyozeka   | w. Kupuma          |
| f. Zakunja     | o. Ana         | x. Zadziko lapansi |
| g. Mtendere    | p. Wamoyo      | y. Kuvumbulutsidwa |
| h. Mphoto      | q. Kupulumutsa |                    |
| i. Atsogoleri  | r. Kukonda     |                    |

## CHAPUTALA 9

1. Ndipo Herode anati, Yohane ndinamdula mutu ine; koma uyu ndani ndikumva zotere za iye? Ndipo anafunafuna kumuona iye. Luka 9:9
2.
  - a. yatsopano
  - b. yakale
  - c. yakale
  - d. yatsopano
  - e. yakale
  - f. yatsopano
  - g. yakale
  - h. yatsopano
  - i. yatsopano
  - j. yakale
  - k. yatsopano
  - l. yakale
  - m. yakale
  - n. yatsopano
  - o. yatsopano
  - p. yakale
  - q. yatsopano
  - r. yakale
  - s. yakale

- t. yatsopano
- u. yakale
- v. yatsopano
- w. yatsopano
- x. yakale

3. Yankho ndi B.
4. Mfundo za Chipangano chatsopano ndizokhazikika pa maziko Chilamulo cha Chipangano chakale.

## **CHAPUTALA 10**

1. Ndipo Iye anayankha nati, Cifukwa kwapatsidwa kwa inu kudziwa zinsinsi za Ufumu wa Kumwamba, koma sikunapatsidwa kwa iwo. Mateyu 13:11
2. Fanizo ndi nkhani imene imagwiritsa chitsanzo chakuthupi pofuna kuonetsera choonadi chazimu. Tanthauzo lenileni la mau oti fanizo ndi “kufananiza.” Mu mafanizo a Yesu Khristu, amagwiritsa nchito chitsanzo chakuthupi ndikufananitsa ndi choonadi chazimu. Kapena kuti ndi nkhani yakudziko yokhala ndi tanthauzo lakumwamba.
3. Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo ndi cholinga choti okhao ali ndi maganizo auzimu kapena kaonedwe kuzimu kuti azindikire mfundo zofunika. Ndipo onse okhala ndi maganizo akuthupi kapena osakhulupirira samamvetsa mafanizo amenewa. Iyi inali njira imodzi yobisa choonadi kwa iwo.
4. Ufumu wa Mulungu.

## **CHAPUTALA 11**

1. Ndipo pamene mulikupita lalikani kuti, Ufumu wa Kumwamba wayandikira. Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. Mateyu 10:7-8.
2. Kazembe ndi nthumwi yotumidwa imene imaimilira ufumu mu dziko lina. Iye amakhala m'thenga wa Ufumu umene akuimilira.
3. Mboni ndi munthu amene amaperekeram umboni wa zinthu zimene anazona ndi maso ake zikuchitika.
4. Kuonetsera m'phamvu.
5. Chimaliziro sichingafike komanso Ufumu sungakhazikitsidwe pokhapokha uthenga utalalikidwa dziko lonse lapansi.
6. Kufalitsa uthenga wa Ufumu wa Mulungu.